# ***MKAZI MOLINGANA NDI BAIBULO***

**HARVESTIME INTERNATIONAL INSTITUTE**

Phunziro limeneri ndi gawo limodzi la maphunziro a **Harvest International Institute** ndipo cholinga chake ndi kukonzekeretsa okhulupilira kuti akatute zokolora zambiri zauzimu.

Mutu waukulu mumaphunzirowa ndikuphunzitsa zimene Yesu anaphunzitsa, zimene zinasandulitsa anthu wamba monga asodzi, otolera misonkho ndi ena kulalikira Uthenga Wabwino ndi kuwonetsera mphamvu ya uthengawo mu nthawi yawo.

Bukuli ndi phunziro limodzi mwa maphunziro ambiri amene cholinga chake ndikuwakopa okhulupilira kuti akakonze dongosolo, kuyendetsa, ndi kubweretsa pamodzi anthu kuti Uthenga Wabwino ukalalikidwe.

**ZAMKATI MWA BUKULI**

KAGWIRITSIDWE NTCHITO KA BUKHULI……………………………………………..…3

NDONDOMEKO ZA KUPHUNZIRA PAGULU…………………………………..……….4

MAU OYAMBA………………………………………………………………………….5

ZOLINGA ZA MAPHUNZIRO………………………………………… ………........6

1. PACHIYAMBI……………………………………………………………………7
2. KUGWA KWA MKAZI….…………………………………………….………15
3. MKAZI WA CHILENDO NDI MKAZI WANGWIRO……………….……..………27
4. BUKHU LA RUTE……………….……………………………………………...39
5. BUKHU LA ESTERE……………………………………………….…………...52
6. UBALE WA YESU NDI AZIMAYI……………………………………………….60
7. UTUMIKI WA YESU KWA AZIMAYI……………………...…………………....69
8. AZIMAYI M'BUKHU LA MACHITIDWE…………………….……………….....79
9. AZIMAYI M'MAKALATA: MAUTUMIKI A PADERADERA…..………………...88
10. AZIMAYI M'MAKALATA: MAUDINDO MU MPINGO……...………………...95
11. AZIMAYI M'MAKALATA: MALANGIZO A PADERA…………………………110
12. MALO ANU MU UTUMIKI……………………………………….………......123
13. ZOTCHINGA NDI ZOSIYANITSA……………………………..……………141
14. UTUMIKI WA KWA AZIMAYI……………………………………………...151
15. AZIMAYI ONSE M'BAIBULO………………………………...……….......166
16. MAYANKHO A MAFUNSO….…………………………………...……...…..179

## KAGWIRITSIDWE NTHCITO KA BUKULI

## KAKONZEDWE KA BUKULI

Phunziro liri lonse limakhala ndi zinthu izi:

**Zolinga**: Izi ndi zimene mukuyenera kukwaniritsa kapena kudziwa pa mapeto pa phunziro. Welengani zimenezi musanayambe phunziro lanu.

**Vesi Yotsogololera:** Ndimeyi imatsindika mfundo yayikulu mu phunziro lathu.

**Zopezeka mu Magawo**: Gwiritsani ntchito Baibulo lanu kuti mufufuze mavesi amene sanalembedwe mu bukuli koma angotchulidwa.

**Mayeso Odziyesa Nokha:** Osathamangira kulememba mayeso musanamalize kuwerenga chaputala, komanso polemba musagwiritse ntchito Baibulo kapena bukuli polemba mayesowa. Mayankho amayesowa muwapeza kumapeto a bukuli.

**Zophunzira Zowonjezera:** Ndime imeneyi ikuthandizani kuti muwerenge mau Mulungu ndi kuzamitsa ukadaulo wanu pophunziro komanso kugwiritsa ntchito mu utumiki zimene mwa.

**Mayeso Omaliza:** Ngati mwayamba kuphunzira phunziroli mukuyenera kulemba mayeso pamapeto a phunziroli ndipo mayesowo aperekedwa kwa aphunzitsi anu kuti mupatsidwe malikisi.

## ZOWELENGA ZINA ZOFUNIKA POHUNZIRA PHUNZIROLI

Mudzafunikira Buku Lopatulika

## NDONDOMEKO ZOTHANDIZIRA KUPHUNZIRA LIMODZI PAGULU

## MKUMANO WOYAMBA

**Kutsekulira:** Yambani ndi pemphero ndi kudziwana wina ndi mnzake ndipo ophunzira alembetse mayina.

**Khazikitsani Ndondomeko Zapagulu:** Musankhe amene atsogolere mkumano wanu, sankhaninso malo ndi masiku amene muzikumana.

**Mayamiko ndi Matamando:** Yitanirani kupezeka kwa Mzimu Woyera pamene muchita mkumano wanu.

**Gawani Mabuku Kwa Ophunzira:** Awuzeni ophunzira dzina laphunziro, zolinga zake ndi dongosolo.

**Perekani Ntchito Yoyamba**. Ophunzira ayenera kuwerenga ma chaputala amene apatsidwa ndikulemba mayeso odziyesa okha isanafike nthawi ya mkumano wina. Ndipo kuchuluka kwa machaputala amene aziphunzitsidwa pa mkumano uli wonse kuzitengera kutalika kwa chaputala komanso kumvetsetsa kwa ophunzira.

## MKUMANO WACHIWIRI NDI KUKUMANA KWINA PATSOGOLO

**Kutsekulira:** Tsekulirani ndi pemphero kenako lembani mayina a ophunzira atsopano ndikuwapatsa buku lawo. Muyitane mayina a ophunzira amene abwera. Komanso osayiwala mayamiko ndi matamando kwa Mulungu.

**Kukumbutsira**: Yambani ndi kubwereza mwachidule zimene munaphunzitsa mu mkumano wanu womaliza.

**Phunziro:** Afunseni ophunzira ndemanga zawo kapena mafunso okhudza phunziro limene aphunzira komanso m'mene angagwiritsire ntchito zimene aphunzira pamoyo wawo ndi utumiki.

**Mayeso Odziyesa Nokha**: Konzetsani mayeso amene ophunzira amaliza ndipo mukhonza kusankha kupereka mayankho kapena kuwachotsa mubukuli kuti ophunzira adzipezere okha mayankho.

**Mayeso omaliza:** Pamapeto pa maphunziro amenewa, gulu la ophunzira onse lidzapemphedwa kulemba mayeso omaliza ndipo aphunzitsi awonetsetse kuti ophunzira wina aliyense ali ndi buku laphunziroli.

## MAU OYAMBA

Pali magulu ambiri lero omwe akulankhula m'malo mwa azimayi.

- Tamva za anthu akumenyera ufulu wa azimayi kuti akhale ndi mwayi wofanana ndi azibambo.
- Maiko ena akuti azimayi akhale pansi pa ulamuliro wa azibambo.
- Anthu ochita maphunziro a Baibulo akulimbanabe pa nkhazi yokhuza udindo wa amayi mu mpingo.
- Akadaulo pa maphunziro osiyanasiyana nawonso ali ndi maganizo osiyanasiyana pa munthu wamayi.

Kwakuru, nkhaniyi ikukhuzana ndi cholinga ndi udindo wa mzimayi pakati pa anthu. Magulu omenyera ufulu wa azimayi akhala akuonesera poyera kusakondwa kwao ndi mavuto omwe azimayi akukumana nawo.

Nkhani yomenyera ufulu azimayi siyachilendo. Titha kuona kuchokera pachiyambi kwa mzimayi woyamba, Hava, yemwe anakana kukhala pansi pa ulamuliro wa Mulungu. Komano ufulu weni weni wa mzimayi umapezeka mwa Khristu Yesu komanso kuzindikira mfundo zomwe Baibulo likupereka zotithandizira kumvetsa bwino nkhani ya mzimayi.

Phunziro ili likukamba mwachidule zonse zomwe Baibulo likufotokozera pa nkhani ya azimayi. Likuthandaninso kupeza mosavuta ndime zonse zomwe zikukamba za azimayi m'Baibulo.

## ZOLINGA ZA PHUNZIRO

Pomaliza phunziro lino mukhala mukukwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kufotokozera mwachidule mbiri ya azimayi molingana ndi Baibulo.
- Kulemba mndandanda wa zolinga zomwe azimayi adalengedwera.
- Kuyerekezetsa magulu awiri a azimayi opezeka m'Bukhu la Miyambo.
- Kufotokozera udindo wa azimayi mu utumiki wa Yesu wa pansi pano.
- Kufotokozera malo a azimayi mu utumiki molingana ndi Bukhu la Machitidwe komanso Makalata.
- Kugwiritsa ntchito malemba pofotokozera mwayi wa utumiki womwe azimayi ali nawo.
- Kulemba mwachidule Bukhu la Rute.
- Kulemba mwachidule Bukhu la Estere.
- Kupitiriza panokha kusanthula nkhani ya azimayi molingana ndi Baibulo.
- Kuphunzitsa azimayi zomwe mwaphunzira.
- Kuyamba utumiki wofikira azimayi.

# CHAPUTALA 1

# PACHIYAMBI

**Zolinga:**

Pomaliza pa phunziro lino muzikwanitsa kuchita izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera.
- Kulemba mavesi olankhula za chiyambi cha mkazi.
- Kulemba mwachidule za chilengedwe chauzimu cha mkazi.
- Kufotokozera ubale wake ndi Mulungu komanso mwamuna molingana ndi Mau a Mulungu.
- Kuzindikira cholinga cha Mulungu polenga mwamuna ndi mkazi.

VESI LOTSOGOLERA

> **Mulungu ndipo adalenga munthu m'chifanizo chache, m'chifanizo ch Mulungu adamlenga iye; adalenga iwo mwamuna ndi mkazi.Genesisi 1:27**

## MAU OYAMBA

Bukhu la Genesis limadziwika kuti ndi Bukhu la Ziyambi. Limafotokozera chiyambi cha dziko, mwamuna ndi mkazi, tchimo ndi dongosolo la Mulungu pofuna kupulumutsa munthu, komanso momwe maiko anapangidwira.

Chaputala choyamba cha Genesis za kulengedwa kwa dziko. Chaputala chachiwiri za kulengedwa kwa mwamuna ndi kutchulidwanso kwa mkazi pa Genesis 1:27. Mavesi eni eni okamba za chiyambi cha mkazi ali mu Genesis 2:

> **Yehova Mulungu ndipo anati, Si kwabwino kuti munthu akhale yekha; ndidzampangira womthangatira iye,**
>
> **Koma Yehova Mulungu anamgonetsa Adamu tulo tatikuru ndipo anagona ndipo anatengakoko nthiti yache imodzi, natsekapo ndi mnofu pamalo pache:**
>
> **Chifukwa chotero mwamuna adzasiya atate wache ndi amache nadzadziphatika kwa mkazi wache: ndipo adazakala thupi limodzi. Genesis 2:18, 21-24**

Baibulo limafotokoza kuti mkazi:

## ANALENGEDWA NDI MULUNGU

Genesis 2:7 imanena kuti mwamuna analengedwa kuchokera ku dothi. Kenako Mulungu anauzira mwa munthu mpweya wa moyo, ndipo munthu anakhala wamoyo. Mulungu anaona

kuti sikwabwino kuti Adam akhale yekha (Genesis 2:22). Mulungu anamgonetsa Adam tulo tatikulu, ndipo anatenga nthiti yake imodzi napanga mkazi woyamba yemwe anatchulidwa kuti Hava.

Adam anatchula bwezi lakeli mkazi, ndipo tanthauzo lake ndi lakuti "wolumikizidwa kwa mwamuna," popeza anapangidwa kuchokera kwa mwamuna. Apa ndi pamene mau oti, "mkazi" anachokera.

## ANALENGEDWA M'CHIFANIZO CHA MULUNGU

Genesis 2:26-27 imatsindika kuti mwamuna ndi mkazi onse analengedwa m'chifanizo cha Mulungu:

> **Ndipo anati Mulungu, tipange munthu m'chifanizo chathu, monga mwa chikhalidwe chathu; alamulire pa nsomba za m'nyanja, ndi pa mbalame za m'mlengalenga, ndi pa ng'ombe ndi pa dziko lonnse lapansi, ndi pa zokwawa zonse zakukwawa pa dziko lapansi.**
>
> **Mulungu ndipo adalenga munthu m'chifanizo chache, m'chifanizo cha Mlungu adalemlenga iye adalenga iwo mwamuna ndi mkazi. Genesis 1:26-27**

## UDINDO WOYAMBA WA MUNTHU

Mulungu anauza Adam ndi Hava kuti:

- Abalane
- Achurukane
- Adzadze dziko lapansi
- Agonjetse dziko lapansi
- Akhale nawo ulamuliro pa cholengedwa chiri chonse (Genesis 1:28)

Ndi zochititsa chidwi kuona kuti lamulo loyamba lomwe Mulungu anapereka kwa Adam ndi Hava ndi lakuti "abalone. Dongosolo la maphunziro a Harvestime International Institute linakonzedwa potsatira mutu wa "khsolola la uzimu, kapena kukhala wobereka. Kukhala wobala muuzimu ndi mfundo ya Baibulo yomwe imaoneka kuchokera mu lamulo ili la Adam mpaka kholola lomaliza la maiko m'bukhu la Chibvumbulutso.

Adam ndi Hava amayenera kukhala obereka m'magawo onse atatu a moyo wao – kuthupi, kuuzimu komanso moyo pamene akudzadza dziko lapansi, kuligonjetsa ndi kukhala nawo ulamuliro pa ilo.

## UBALE WA MKAZI NDI MULUNGU

Mkazi analengedwa ndi Mulungu, mu chifanizo cha Mulungu, ndi moyo wosatha (Genesis 2:7) wokhala pa ubale ndi Mulungu mwa padera. Ubale uwu ndi wauzimu popeza Mulungu ndi mzimu (Yohane 4:24). Mulungu anali wokondwa ndi ubale wake ndi Adam ndi Hava (Genesis 3:8). Ubale wao unasokonekera pamene munthu anagwa mu uchimo, komabe Mulungu anakonza dongosolo lobwezeretserea ubale wauzimu wa munthu ndi Mlengi wake. Muphunzira zambiri pa nkhani iyi mu chaputala chikubwerachi.

## UBALE WA MKAZI NDI MWAMUNA

Ubale wa mkazi kwa mwamuna ndi wa:

**CHIKONDI:**

Ngakhale phunziro lino si likukhuzana ndi zifanifani za Baibulo, komabe pakuyenera kufotokozeredwa mau ena ofunika kuti tikathe kumvetsa bwino ubale wa pakati mkazi ndi mwamuna monga m'mene Mulungu anakonzera pachiyambi. Tikakamba za zifanifani za Baibulo, timatanthauza kuti nkhani zina zomwe zalembedwa m'Baibulo ndi zongofunika pazokha, koma ndi zitsanzo za zoonadi zauzimu zazikuru.

Anthu komanso nkhani zambiri zomwe ziri m'Chipangano Chakale ndi zifanifani za zoonadi zauzimu zobvumbulutsidwa m'Chipangano Chatsopano. Kasanthulidwe ka zifanifani kali m'phunziro la Harvestime International Institute lotchedwa "Njira za Kasanthulidwe Baibulo Kaluso."

Kulengedwa kwa mwamuna ndi mkazi ndi chitsanzo cha chifanifani cha ubale womwe unadzakhalapo wa pakati pa Khristu ndi Mpingo. Pamene Hava anapangidwa Adam atang'ambidwa m'nthiti ali mtulo, Mpingo unapangidwa Yesu atapachikidwa pa mtanda chifukwa cha machimo athu. Yesu anabaidwa m'nthiti momwe munaturuka mwanzi woombola ndi kuyeretsa Mpingo.

> **Amuna inu, kondani akazi anu, monganso Khristu anakonda Eklesia, nadziperekea yekha m'malo mwache. Aefeso 5:25-26**

Kulengedwa kwa mkazi kumalankhula za ubale wa chikondi, wofanana ndi womwe ulipo pakati pa Khristu ndi Mpingo. Chikondi ichi ndi chozama, chokhalitsa komanso chauzimu, osati chogonera pa zilakolako zathupi ndi maonekedwe ayi.

**UBWENZI**

Mulungu anati sikwabwino kuti munthu akhale yekha. Anali ndi cholinga chakuti mwamuna ndi mkazi akhale abwenzi.

**WOTHANGATIRA**

Mulungu anati ampangira munthu womthangatira (Genesis 2:18). Mau oti “wothangatira” amapezeka malo okwana 40 mu Chipangano Chakale, ndipo amagwiritsidwa ntchito pofotokozera za Mulungu monga wothandizira anthu ake. Mauwa satanthauza kugonjera, popeza Mulungu sagonjera kwa munthu. Koma amapereka chithunzithunzi cha ubale wopereka, wokonda, ndi wosamalira monga womwe ulipo pakati pa Mulungu ndi munthu.

**WODZIPEREKA**

Genesis 2:24 amalankhula za ubale wodzipereka wa pakati pa mwamuna ndi mkazi. Mwamuna akuyenera:

Kusiya mai ake ndi bamboo ake: Kudzipereka m’maganizo

Nadziphatika yekha ndi kwa mkazi wake: Kudzipereka mu mtima.

Nakhala thupi limodzi: Kudzipereka ku thupi.

Chikondi, ubwenzi, kudzipereka ndi kuthandizana mofanafa ndi zomwe Mulungu amafuna kuti zikhalepo pa ubale wa pakati pa mwamuna ndi mkazi.

**MAYESO ODZIYESA NOKHA**

1. Lembani mavesi enieni ofotokozera za kulengedwa kwa mkazi.
______________________________________________________________________
______________________________________________________________________
2. Pa ntchito zomwe ziri m'musizi, ndi ntchito iti yomwe Mulungu sanapereke kwa mwamuna ndi mkazi.
   a. Kubalana
   b. Kuchurukana
   c. Kugonjetsa dziko lapansi
   d. Kumanga mizinda ndi midzi
   e. Kukhala nawo ulamuliro pa zolingedwa zonse.
   f. Kudzadza dziko lapansi.
3. Chongani yankho limodzi lolondola. Ubale wa pakati pa mkazi ndi Mulungu ndi:
   a. Wa kuthupi chabe, popeza tinalengedwa m'chifanizo chake.
   b. Si kuthupi kokha komanso ndi ubale wauzimu.
   c. Palibe ubale popeza munthu anagwa mu uchimo.
4. Lembani maubale akuluakulu omwe akuyenera kukhalapo pakati pa mwamuna ndi mkazi. Perekani ndime zoyenera za m'Baibulo zofotokozera ubale umenewu.
   Ubale Ndime
   1. ____________________________________________________________
   2. ____________________________________________________________
   3. ____________________________________________________________
   4. ____________________________________________________________
   5. Pezani ndime yomwe ikufotokozera bwino tanthauzo la mau oti, "womthangatira."
      ____ Mkazi ndi kapolo wa mwamuna
      ____ Monga momwe Mulungu amathandizira anthu ake.
      ____ Ndi mau omwe ofotokozera ubale wa mwamuna ndi mkazi koma sali m'Malemba.
   6. Lembani Vesi Lotsogolera osaonera.
   7. ____________________________________________________________
      ____________________________________________________________

(Mayankho a mafunso onsewa ali ku mapeto a bukhu lino).

## KUPITIRIZA KUPHUNZIRA

Onjezerani chidziwitso chanu pa nkhani ya chiyambi. Santhulani ndime iriyonse yomwe yaperekedwa ndipo mulembe mwachidule zomwe mungapeze zokhuzana ndi chilengedwe molingana ndi chitsanzo chimene chaperekedwachi.

| NDIME | NDEMANGA |
|---|---|
| Eksodo 20:11 | Mulungu analenga dziko lapansi m'masiku asanu ndi limodzi, ndipo tsiku la chisanu ndi chiwiri anapuma nalitchula Sabata. |
| Nehemiya 9:6 | |
| Yobu 12:9 | |
| Yobu 26:7 | |
| Yobu 38:4-7 | |
| Masalimo 24:2 | |
| Masalimo 33:6 | |

| | |
|---|---|
| Masalimo 95:5 | |
| Masalimo 102:25` | |
| Yesaya 40:28 | |
| Yesaya 45:12 | |
| Yesaya 48:13 | |
| Machitidwe 4:24 | |
| Machitidwe 7:50 | |
| Machitidwe 14:15 | |

| | |
|---|---|
| Ahebri 11:3 | |

## CHAPUTATALA 2

## KUGWA KWA MKAZI

### ZOLINGA

Mukamaliza phunziro lino mukhala mukukwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera.
- Kufotokozera kugwa koyambilira kwa mkazi.
- Kulemba tsatanetsane wa zotsatira za tchimo.
- Kupereka ndime ya m'Baibulo ya lonjezo loyambirira la Mpulumutsi.
- Kudziwa msampha wa mayesero

### VESI LOTSOGOLERA

> **Ndipo ndidzaika udani pakati pa iwe ndi mkaziyo ndi pakati pa mbeu yako ndi mbeu yache ndipo idzalalira mutu wako, ndipo iwe udzalalira chitende chache. Genesis 3:15**

### MAU OYAMBA

Genesis 3 ndi chaputala chomvetsa chisoni mwa machaputala onse m'Baibulo, koma mbali inanso ndi chodabwitsa. Munapitirire ndi phunziro lino werengani Genesis 3 m'Baibulo lanu.

### YESERO

Satana akupezeka pa Genesis 3 ngati njoka, ndipo ndi dzina lake lina molingana ndi Chibvumbulutso 12:9. Anaonekera mwa maonekedwe a njoka. Kuti timvetse bwino yesero la Hava, tiyeni tione kaye malamulo oyambilira omwe Mulungu anampatsa munthu:

> **Ndipo Yehova Mulungu anamuuza munthuyo, nati mitengo yonse ya m'munda udyeko.**
>
> **koma mtengo wakudziwitsa zabeino ndi zoipa usadye umewo chifukwa tsiku lombwe udzaya umenewo udzafa. Genesis 2:16-17**

Stepe yoyamba ya kugwa kwa Hava ndi kukhala malo olakwika. Mu Genesis 3 tikumpeza ali pafupi ndi mtengo woletsedwa. Miyambo amakamba za njira ya oipa:

> **Pewapo osapitamo patukapo nupitirire Miyambo 4:15**

Kachiwiri, Hava samayenera kuyamba kulankhula ndi Satana yemwe amalankhula mau otsutsa malamulo a Mulungu kwa munthu:

> **Ndipo zinatha kupangidwa zakumwamba ndi dziko lapansi, ndi khamu lao lonse. Genesis 3:1**

Nthawi zonse Satana amabweretsa mayesero mu njira yotipanga ife kuyamba kukaikira Mau a Mulungu. Hava poyankha Satana, analankhula Mau a Mulungu koma molakwika. Anaonjezerapo pa Mau a Mulungu komanso kuchepsa chilango chobwera chifukwa cha uchimo:

> **Mulungu ndipo anadalita tsiku la chisanu ndi chiwiri, naliyeretsa limenelo chifukwa limennero ada puma ku nthcito yache yonse imene Muulungu anailenga ndi kupanga. Genesis 3:3**

Yerekezani mau awa ndi Genesis 2:16-17. Mulungu sananene kuti, "ndipo musaukhudze." Zinazi anaonjezerapo ndi Hava. Kuyambira pachiyambi munthu anayamba kuonjezera maganizo ndi malamulo ake ku Mau a Mulungu. Chinanso nchakuti Mulungu anati, "mudzafa ndithu." Ichi chinali chilango chimene Mulungu ananena kuti chidzawagwera akadzadya zipatso za mtengo uja. Koma Hava anasintha mau a chilango ndipo anati, "kuti mungafe" kutanthauza kuti "mukhoza kufa."

Lero tili ndi bvuto lakuti anthu amachepsa chilango cha uchimo. Amati, "Mulungu ndi wachifundo, sangaponye anthu ku Gahena. Zoona, Mulungu sadzaponya aliyense ku Gahena. Munthu amasankha kupita yekha ku Gahena chifukwa cha ntchito zake zauchimo. Chilango cha uchimo sichinasinthe – kusiyana ndi Mulungu kwa muyaya uli ku Gahena. Nthawi zambiri anthu amapeputsa uchimo. Kuchotsa pakati amati "kulera" osati "kupha." Chiwerewere nthawi zina chimatchedwa "ubwenzi."

Poyankha Hava, Satana anatsutsa Mau a Mulungu:

> **Njokayo ndipo inati kwa mkaziyo, kufa simudzafai;**
>
> **Chifukwa adziwa Mulungu kuti tsiku limene mukadya umenewo dzatseguka maso anu ndipo mudzakhala ngati Mulungu, wakudziwa zabwino ndi zoipa.**
>
> **Ndipo pamene anaona mkaziyo kuti mtengo unli wabwino kudya, ndi kuti unali wokoma m'maso mtengo wolakalakika wakupatsa nzeru, anatenga zipatso zache,nadya, napatsanso mwamuna wache amene ali naye, nadya iyenso,**
>
> **Ndipo anatseguka maso awo onse awiriri, nadziwa kuti anali amariseche; ndipo adasoka masamba amkuyu, nadzipangira matewera.**
>
> **Ndipo anamva mau a Yehova Mulungu alinkuyendayenda m'munda nthawi yamadzulo; ndipo anabisala Adamu ndi nkazi wake pamaso pa Yehova Mulungu pakati pa mitengo ya m'munda.**
>
> **Ndipo Yehova Mulungu anaitana mwamunayo nati kwa iye Uli kuti? Genesis 3:4-9**

Onani momwe Mau a Mulungu anagwiritsidwira ntchito molakwika mu yesero loyamba:

**Poyamba**: Mau a Mulungu anakaikiridwa – "Kodi Mulungu anati?"

**Kachiwiri**: Mau a Mulungu anaonjezeredwa – "ndipo musaukhudze"

**Kachitatu**: Chilango chinachepsedwa – "kuti mungafe" m'malo mwa "mudzafa ndithu"

**Kachinayi**: Mau a Mulungu anatsutsidwa – "kufa simudzafa ayi"

Kuzindikira ndondomeko iyi nkofunika, popeza Satana amagwiritsa ntchito ndondomeko yomweyi mpaka lero pofuna kulowetsa anthu mu uchimo. Amatsutsa Mau a Mulungu napangitsa anthu kuti adzimva kusakhutitsidwa. Hava anali woyera pamaso pa Mulungu ali m'munda wokongola wa Eden, koma Satana anampa kuyamba kumva kusakhutitsidwa. Anampanga iye kukhulupirira kuti atha kufanana ndi Mulungu ndi kudziwa chirichonse. Kusakhutitsidwa kumatilowetsa mu uchimo. Mwa chitsanzo, kusakhutitsidwa ndi ndalama zomwe mumapeza kutha kukulowetsani moyo wakuba ndi bodza. Kusakhutitsidwa ndi ukwati wanu kutha kukutsogolerani ku chigololo.

Satana anafunisitsa kusiyanitsa Hava ndi Mulungu. Iye anaonetsa kuti akudziwa kuti Mulungu sakufuna kuti Hava apindule pakudya chipatsocho kuti akhale wodziwa zonse ndi kufanana ndi Mulungu. Mu njira ina amanena kuti, "Hava, Mulungu sakukuganizirani, nanga bwanji sakufuna kuti mufanane naye." Hava amayenera kuyankha kuti, "ndine wofanana kale ndi Mulungu" popeza kuti analengedwa nchifanizo cha Mulungu.

Nthawi zonse kumbukirani kuti: Uchimo ukamabwera umakhala ndi maonekedwe a mwayi.

**KUGWA**

Genesis 3:6 amafotokozera ngozi yaikuru imene inachitikako mu mbiri ya anthu:

> **Ndipo pamene anaona mkaziyo kuti mtengo unali wabwino kudya, ndi kuti unali wokoma m'maso mtengo wolakalakika wakuptatsa nzeru, anatenga zipatso zache nadya, napatsanzo mwamuna wake amene ali naye nadya iyenso, Genesis 3:6**

Onani momwe tchimo linayendera:

**Anamva**: Mau a Satana.

**Anaona**: Ndipo chinaoneka chokoma m'maso.

**Anatenga**: Kuchibweretsa kwa iye.

**Anadya**: Kutafuna chipatso cha mtengo.

**Anapatsa**: Kupangitsa Adam kuti achimwe.

**Adam anadya**: Ndipo naye anachimwanso.

Ndi chinthu chofunikira kudziwa ndi kumvetsa momwe zinthu zinayendera pamene munthu anachimwa. Popeza kuti njira yake imakhala yomwe imene lero anthu amagwera mu uchimo. Poyamba Hava anali malo olakwika. Anakapezeka pa malo pamene kunali kosavuta kulowa m'mayesero. Kenako, anapereka mpata kwa mdani pomumvetsera zomwe amalankhula.

Kuchoka apo, anayang'ana mwa chikoka chinthu chomwe Mulungu anawaletsa. Apapa yesero linali likhadali padali, koma tsopano Hava anapita nakathyola chipatsocho ndikudya. Anadya chipatso chomwe Mulungu anachitchula kuti TCHIMO.

Chotsatira chake chinali chakuti tchimo lija linakhuzanzo Adam pamene Hava anampatsa chipatsocho kuti adye ndipo anadya. Munthu akachimwa, tchimo lija limakhuzanso iwo amene amuzungulira munthuyo, nawonso amalowa m'chiononongeko chomwecho.

Paulo akuchenjeza pa nkhani yomweyi:

> **Wodala munthuyo wosayenda mu umphungu wa oipa, kapena wosaimirira m'njira ya ochimwa, kapena wosakhala pansi pa bwalo la onyoza.**
>
> **Komatu m'chiilamulo cha Yehova muli chikondwerero chake; ndipo m'chilamulo chache amalingingalila usana ndi usimu. Masalimo 1:1-2**

Poyamba umayenda mu yesero la tchimo. Ngati suthawa, ukhala ukuima kuti ulingalire za tchimolo. Kenako ukhazikika nawo pa malo a anthu ochimwa kukhazikika mu uchimo.

Onani chojambula chiri m'musichi. Posatengera kuti muli chapati mkati mwa ulendo wa mayesero ndi tchimo, mphamvu ya mayesero ndi uchimo itha kuphwanyidwa ndi mphamvu ya Yesu Khristu amene analipira dipo la uchimo wa anthu onse.

**Momwe Uchimo Umayendera**

-kuyenda m'malo a mayesero

-kuona tchimo lokanizidwa nd ikusilira

-Kumva mau a Satana

-Kuvomereza kugwa mu uchimo

-Kulowa mu uchimo

-Kukopa ena kuti nawo achimwe

Ulendo wa mayesero uwu utha kuphwanyidwa pena paliponse pamene munthu angakhale ali kudzera mu mphamvu ya mtanda wa Yesu. Pa mtanda Yesu analipira dipo la uchimo. Anaphwanya mutu ndi mphamvu ya Satana kuti inu mukamasulidwe ku mphamvu ya uchimo ndi imfa.

Ngati ulendo wa mayesero ukhala wosaphwanyika pa moyo wanu, mukhala mukupangitsa ena omwe ali pafupi nanu kulowa mu uchimo. Muwakopa kuti nawo achimwe ndikuyambitsanso ulendo wina wa mayesero m'moyo, kufikira nawonso atakopa ena kuti alowe mu uchimo. Chimakhala tcheni chosaduka kufikira chitafalikira pa dziko lonse. Ndipo mphamvu itha kuphwanyika ndi mphamvu ya Uthenga Wabwino wa imfa ya Yesu yofera machimo ndi kuukitsidwa kwake kugonjetsa imfa, Gahena ndi Satana.

Pali maulendo awiri omwe anthu lero akuyenda. Ulendo wa uchimo ndi ulendo wa chipulumutso. Ulendo wa chipulumutso ndiwo kumva Uthenga Wabwino, kuukhulupirira, kubvomereza choonadi, ndi kulowa m'dongosolo la chipulumutso, ndi kutsogolera ena kwa Khristu.

Kodi ndi ulendo uti umene moyo wanu ukuyendamo?

## ZOTSATIRA ZA UCHIMO ZA NTHAWI YOMWEYO

Panali zotsatira zingapo za uchimo zimene zinabwera nthawi yomwe munthu anachimwa:

### KUDZIWA CHABWINO NDI CHOIPA

Atangochimwa Adam ndi Hava sanakhalenso opanda banga. Anazindikira kusiyana kwa pakati pa chabwino ndi choipa ndi kuzindikira kuti ali a maliseche. (Genesis 3:7).

### KUDZILUNGAMITSA

Adam ndi Hava anayesera kuphimba umaliseche wao ndi masamba a mkuyu (chitsanzo cha kuthupi) cha zomwe munthu amayesera kuchita payekha pofuna kudzilungamitsa muuzimu. Podziwa kuti ndife ochimwa, timayesera kudzikonza tokha. Timaganiza kuti kuyesayesa kwathu

kutha kuchotsa tchimo lathu (Genesis 3:7), koma kuyesayesa kwathu nkosakwanira monga m'mene masamba a mkuyu anakanika kuphimba umaliseche wa Adam ndi Hava.

> **Pakuti ife sonse takhala ngati wina amene ali wosakonzeka; ndi zolungama zathu zonse ziri ngati chovala chodetsedwa; ndipo tonse tifota monga tsamba, ndi zoipa zathu zitiuluza monga m'phepo. Yesaya 64:6**

## MANTHA NDI MANYAZI

Mulungu atabwera kudzayenda ndi kucheza ndi Adamu ndi Hava, iwo anabisala chifukwa cha mantha komanso manyazi (Genesis 3:10). Manyazi chifukwa cha zomwe zachitika ndi mantha pa zomwe zichitike mtsogolo ndiye maziko a kusowa mtendere konse komwe munthu amakhala nako.

## KUSIYANITSIDWA NDI MULUNGU

Mulungu sanadzichotse yekha pamaso pa munthu koma anali munthu yemwe anachoka pamaso pa Mulungu. Pali ndondomeko ina yofunikanso. Onani zomwe ziri m'musimu:

**Anakaikira Mulungu**

"Eya, kodi Mulungu anati"

> **Ndipo njoka inali yakuchenjeara yoposa zamoyo za m'thengo zimene anazipanga Yehova Mulungu, ndipo inati kwa mkaziyo, eya kodi anatitu Mulungu usadye mitengo yonse ya m'mundamu? Genesis 3:1**

**Sanamvera Mulungu**

"Anatenga ndipo anadya.."

> **Ndipo pamene anona mkaziyo kuti mtengo unali wawino kudya ndi kuti unali wokoma m'maso mtengo wolakalalkika wakupatsa nzeru natenga zipatso zache nadya napantsanzo mwmuna wache amene alinaye nadya iyenso, Genesis 3:6**

**Anakana Mulungu**

"Adam ndi mkazi wake anabisala kuopa Mulungu"

> **Ndipo anamva mau a Yehova Mulungu alinkuyendayenda m'munda nthawi yamadzulo: ndipo anabisala Adamu ndi mkazi wache pamaso pa Yehova Mulungu pakati pa mitengo ya m'munda Genesis 3:8**

Kudziwa zabwino ndi zoipa, kudzilungamitsa, mantha, manyazi, ndi kusiyanitsidwa ndi Mulungu zinali zotsatira za tchimo za nthawi yomweyo.

**KUKUMANA NDI MULUNGU**

Kukumana ndi Mulungu kunachitika munthu atangochimwa. Mulungu, Adam, ndi Hava onse analipo pa zokambiranazo:

**Mulungu**: "Uli kuti?" Funso la Mulungu silinali lofuna kudziwa komwe Adam ndi Hava anabisala. Mulungu amadziwa chirichonse, ndipo amadziwa komwe anali. Mulungu amafuna kuti Adam ndi Hava alingalire za malo auzimu omwe anali. "Adam, uli kuti? Uli kuti muuzimu? Chinachitika ndi chiyani?"

Mulungu amafunsa funso lomwelo mtundu wa anthu ochimwa lero lino. Tikuyenera kudziwa pomwe moyo wathu wauzimu uli chifukwa chakuti popanda Khristu, chilango cha Mulungu chiri pa ife.

**Adam**: Adam anayankha kuti anamva liu la Mulungu koma anaopa popeza anali maliseche ndipo anabisala pamaso pa Mulungu.

**Mulungu**: Mulungu anamuyankha Adam ndi funso:

> **Ndipo anati, ndani anakuuza iwe kuti uli wamariseche? Kodi wadya za mtengo uja, umene ndinakuuza iwe kuti usadye? Genesis 3**:11

Mulungu anali atadziwa kale Adam wadya za mu mtengo muja. Cholinga chake chinali chakuti Adam abvomereze za tchimo lake:

> **Ngati tivomereza machimo athu, ali wokhulupirirka ndi wolungama iye, kuti atikhuluplukire machimo athu, ndi kutisambitsa kutichotsera chosalungama chirichonse. 1 Yohane 1:9**

Adam: Yankho lake linaonetsera kuti sanali wokonzeka kubvomereza kulakwa. Pamene amaloza chala mkazi wake Hava, anali kuti akulozanso chala Mulungu:

> **Nkaziyo ndipo anati kwa njoka, Zipatso za mitengo ya m'mundamu tidye. Koma zipatso za mtengo umene uli mkati mwa munda, Mulungu nati, musadye umenewo, musakhudze umenewo, mungadzafe. Genesis 3:12**

Mulungu: Kenako Mulungu anafunsa mkazi. "Kodi wachitachi nchiyani?"

Hava: Potsatira zomwe mwamuna wake anachita, Hava anakananso kuvomereza kulakwa. Analoza chala njoka.

Mulungu: Kwina konseko amalankhula ndi Mulungu pamene amalengeza za matembelero ngati zotsatira za tchimo.

## ZILANGO ZA TCHIMO

Taona kale zotsatira za tchimo za nthawi yomweyo pamene Adam ndi Hava anachimwa. Palinso zotsatira zina pamene Mulungu akulengeza zilango kwa njoka, mwamuna, ndi mkazi.

**KWA NJOKA:**

1. Kusintha maonekedwe: Maonekedwe omwe Satana anagwiritsa ntchito kuyesa mkazi anatembeleredwa. Njoka poyamba imayenda tsonga koma kuyambira nthawi imene inatembeleredwa inayamba kukwawa ndi mimba.
2. Udani pakati pa Satan ndi munthu: Ichi chinali chiyambi cha "nkhondo yauzimu," ndi Satana kulimbirana moyo wa munthu. Nkhondoyi ikupitilirabe mpaka pano. Harvestime International Institute imapereka maphunziro otchedwa "Nkhondo Yauzimu" omwe akutsindika za nkhondo ndi kupereka njira za chipambano pa mdani.
3. Mutu wophwanyika: Chilango chachitatu pa njoka ndi lonjezanonso kwa munthu wochimwa. Ngakhale Satana adzalalira chitendene cha munthu muuzimu, mbeu (mwana) yemwe adzachokere kwa mkazi adzaphwanya wa Satana (Genesis 3:15). Ili linali lonjezano loyamba la mpulumutsi ku tchimo la munthu. Ngakhale Satana adzazunza munthu kudzera mu tchimo, Mpulumutsi adzatumizidwa ndi Mulungu kudzera mwa mkazi ndipo mphamvu ya tchimo idzaonongedwa. Bvuto la tchimo linadzera m'kugwa kwa mkazi m'modzi, koma chiombolo chidzabweranso kudzera mwa mkazi yemwe adzabale Ambuye Yesu Khristu.

**KWA ADAM:**

1. Kukhetsa thukuta pogwira ntchito: Asanachimwe Adam amagwira ntchito yosamalira munda wa Eden ndipo inali yosakhetsa thukuta. Koma tsopano akuyenera kugwira nthito kwambiri. Nyengo ya pa dziko lapansi inasintha. Nthaka yomwe inali ya chonde ndi yopanda tizirombo, tsopano inadzala ndi minga.
2. Imfa: Chilango cha imfa ya kuthupi chinaikidwa pa Adam. Mulungu anati thupi lake lidzabwelera ku nthaka, pakuti "ndiwe nthaka ndipo ku nthaka udzabwelera." Chilango china chinali imfa ya kuuzimu. Mulungu anati "moyo wochimwawo, udzafa" (Ezekiel 18:20). Popanda kukhululukidwa kwa, munthu amafa imfa yauzimu ndiyo kulekanitsidwa ndi Mulungu kwa muyaya.

**KWA HAVA:**

Mkazi naye analandira zilango zake chifukwa cha tchimo:

1. Chisoni pobereka: Thembelero la ululu ndi chisoni pobereka linaikidwa pa mkazi.
2. Kugonjera: Hava adzagonjera pa mwamuna wake. (Tikambirana zambiri za kugonjera patsogolopa pamene tikhale tikusanthula makalata).

**ZILANGO ZA PA ONSE – ADAM NDI HAVA**

Mulungu anatchotsa Adam ndi Hava m'munda wa Eden malo okongola kwambiri kuwapititsa ku dziko lodzala ndi chisoni, ululu, minga ndi imfa.

**LONJEZO LA KHRISTU**

Malo okhawo opereka chiyembekezo mu Genesis 3 ndi pamene pali lonjezo la Momboli ali nkuza yemwe adzaphwanya mphamvu ya Satana (Genesis 3:15).

Onani momwe izi zinakwaniritsidwira mwa Khristu:

| **Tchimo Linabweretsa** | **Khristu anakwaniritsa** |
|---|---|
| Chizunzo | Yesu anazunzika m'malo mwathu (Yesaya 53:11). |
| Kugonja: | Anagonjera chilamulo (Agalatiya 4:4) |
| Minga | Anavekedwa minga m'malo mwathu (Mateyu 27:29). |
| Thukuta | Yesu anakhetsa thukuta longa magazi (Luka 22:44) |
| Chisoni | Indedi anasenza zisoni zathu (Yesaya 53:4-5) |

Yesu anasenza chilango chiri chonse cha tchimo m'malo mwathu. Kudzera m'moyo imfa ndi chiukitso chake, mutu wa Satana unaphwanyidwa.

CHIYAMBI NDI CHIMALIZIRO

M'machaputala awiri oyambilirawa taphunzira zimene zinachitika pamene mkazi woyamba analengedwa. Bukhu la Chibvumbulutso likusiyanitsa chiyambi ndi chimaliziro. Werengani Chibvumbulutso 21 ndi 22 omwe akufotokozera masiku omalizira a nthawi ino ndi kumwamba kwatsopano komanso dziko latsopano lomwe Mulungu wakonzera anthu ake. Onani pa tchati ili m'musiyi momwe chilango chiri chonse cha tchimo chidachotsedwera:

| **GENESIS** | **CHIBVUMBULUTSO** |
|---|---|
| Paradizo watsekedwa 3:23 | Paradizo watsegulidwa 21:25 |
| Kulandidwa mdalitso ndi tchimo 3:24 | Kubwezeretsedwa mwa chisomo 21:24 |
| Tembelero laikidwa 3:17 | Tembelero 22:3 |
| Kukanizidwa mtengo 3:24 | Kulelodwa ku mtengo 22:14 |

| | |
|---|---|
| Chiyambi cha chisoni 3:16-19 | Kutha kwa chisoni, imfa 21:4 |
| Munda wadetsedwa 3:5-7 | Kulibe kudetsedwa 21:27 |
| Ulamuliro wa munthu waduka 3:19 | Ulamuliro wabwezeretsedwa 22:5 |
| Uchimo wapambana 3:13 | Chiyero chapambana 20:10 |
| Ubale wa munthu ndi Mulungu waonongeka 3:8-10 | Ubale wayambikanso 21:3 |

Ngakhale nthawi ya kugwa mu uchimo kwa munthu inali nthawi yowawitsa kwambiri mu mbiri, pali chiyembekezo cha tsogolo lopambana kwa munthu kudzera mwa Khristu Yesu.

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Kondi ndi vesi lanji lomwe ndi lonjezo loyamba la Mpulumutsi m'Baibulo?
   ______________________________________________________________
2. Lembani Vesi Lotsogolera osaonera.
   ________________________________________________________________
   ___________________________________________________________
3. Lembani "I" (inde) kumayambiliro kwa ndime iriyonse yomwe mukugwirizana nayo. Ndipo mulembe "A" (ayi) kumayambiliro a ndime yomwe simukugwirizana nayo.
   a. _____ Hava analankhula Mau a Mulungu molakwitsa pamene amalankhula ndi satana.
   b. _____ Adamu analoza chala satana pa uchimo wake.
   c. _____ Hava analoza chala Adamu pa uchimo wake.
   d. _____ Hava anachepsa chilango cha uchimo monga momwe Mulungu anachenjezera.
   e. _____ Munthu atha kuturuka mu tcheni cha yesero pena pali ponse kudzera mu mphamvu ya Khristu.
4. Werengani zilango zonse zomwe zalembedwa m'musizi. Ndipo mulembe:
   S (serpent) ngati chilango chimapita kwa njoka.
   W (woman) ngati chilango chimapita kwa mkazi
   M (man) ngati chilango chimapita kwa mwamuna
   MW (man, woman) ngati chilango chimapita kwa mwamuna ndi mkazi wonse pamodzi.

   a. ______ Imfa yauzimu
   b. ______ Kudziwa chabwino ndi choipa
   c. ______ Idzaphwanya mutu wako
   d. ______ mantha ndi manyazi
   e. ______ Kukhetsa thukuta
   f. ______ Ululu pobereka

(Mayankho a mafunso awa ali ku mapeto a bukhuli)

## KUPITIRIZA KUPHUNZIRA

Pitirizani kuphunzira kusiyana kwa chiyambi ndi mapeto a dziko lapansi pogwiritsa ntchito ndime ziri m'musizi:

| **CHIYAMBI – GENESIS 1-3** | **MAPETO – CHIBVU. 20-22** |
|---|---|
| Mulunga alenga kumwamba ndi dziko lapansi 1:1 | Kumwamba kwatsopano ndi dziko latsopano: 21:1 |
| Kuwale: 1:3-5 | Sikufunika kuunika 21:23; 22:5 |
| Madzi otchedwa Nyanja 1:10 | Kulibe njanja 21:1 |
| Kukanizidwa ku mtengo wamoyo: 2:8-9 | Kuloledwa ku mtengo wamoyo 22:2 |
| Mtsinje woturuka m'Eden 2:10 | Mtsinje wamoyo 22:1 |
| Imfa kuchokera mu mtengo 2:17 | Moyo kuchokera mu imfa 22:2 |
| Tembelero kukhazikitsidwa 3:17 | Kulibe thembelero 22:3 |
| Kumva ululu 3:17 | Kulibe kupweteka 21:4 |
| Khomo la m'munda litsekeredwa 3:24 | Chipata chotsegula 21:5 |
| Kusiyanitsidwa ndi Mulungu 3:8 | Kukhala pamaso pa Mulungu kwamuyaya 20:12 |
| Imfa inakhazikitsidwa 2:17 | Imfa ichotsedwa 20:14 |
| Satana ananamiza anthu 3:4-6 | Satana sanganimenso munthu 20:3 |
| Satana wamasulidwa kukachita zoipa 3:4-6 | Satana wamangidwa 20:3 |
| Chisoni 3:17 | Kulibenso chisoni 21:4 |
| Mphamvu yolenga ya Mulungu 1:1 | Mphamvu ya Mulungu yoononga |
| Zinayamba 1:1 | Zikumalizika 21:6 |

## CHAPUTALA 3

## MKAZI WANGWIRO NDI WACHILENDO

### ZOLINGA:

Pomaliza pa phunziro lino mukhala mukukwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kudziwa mitundu iwiri ya akazi yomwe iri mu m'bukhu la Miyambo
- Kufotokozera maonekedwe a mkazi wachilendo
- Kufotokozera maonekedwe a mkazi wangwiro

### VESI LOTSOGOLERA

> **Kukongola kungonyenga, maonekedwe okoma ndi chabe koma mkazi woopa Yehova adzatamandidwa. Miyambo 31:30**

### MAU OYAMBA

Pamene Mulungu amalenga mkazi, anamlenga wokongola ndi wopanda banga. Koma chifukwa cha kugwa kwake mu uchimo, akazi onse tsopano ali m'magulu awiri:

Mkazi wopanda Mulungu: Mkazi wochimwa yemwe sanalandire Yesu monga Mpulumutsi ndi kuti sanalandire chikhulululukiro cha machimo ake.

Mkazi wokhala ndi Mulungu: Mkazi uyu anali wochimwa koma analandira Yesu monga Mpulumutsi. Ndipo tsopano ali wangwiro pamaso pa Mulungu.

Bukhu la Miyambo, limatsindika kusiyana kwa akazi magulu awiri amenewa. Mkazi wopanda Mulungu akufotokozeredwa monga "mkazi wa chilendo" ndipo mkazi wokonda Mulungu akufotokozeredwa monga "mkazi wangwiro."

Nkhani ya mkazi wachilendo ikuyenda kuchokera ku mayambiliro a Bukhu la Miyambo mpakana chaputala chomaliza chomwe chikupereka makhalidwe a mkazi wangwiro mu njira ya ulemelero waukuru.

### BUKHU LA MIYAMBO

Bukhu la Miyambo limatchedwa bukhu la "nzeru za kumwamba zothandizira moyo watsikutsiku." Timapezamo nzeru za Mulungu zomwe tingagwiritse ntchito kuti tikakhale bwino ndi anthu ena pansi pano.

Mau oti "miyambo" amatanthauza "mau a chidule osati ambiri." Ndime iriyonse m'bukhuli ndi mau olunjika opatsa nzeru.

Solomo, mwana wa Davide, ndi yemwe analemba miyambo yambiri. Timamva kuchokera ku 1 Mafumu 4:32 kuti Solomoni ananena miyambo yokwana mazana atatu motsogozedwa ndi Mulungu. Miyambi ina ndi imene Mzimu Woyera anaisunga ndipo ikupezeka M'bukhu la Miyambo.

Solomoni anatsindika za akazi achilendo ndi owopa Mulungu molingana ndi zomwe anadutsamo ndi mabanja ake. Iye anachimwira Mulungu pokwatira akazi ambiri oposera m'modzi ndipo ena mwa akazi omwe anakwatira anali achilendo, otumikira milungu yonama.

**MKAZI WA CHILENDO**

Mau oti "chilendo" M'bukhu la Miyambo amatanthauza "wa dziko lina, mlendo, kapena wachigololo." Amafotokozera za mkazi amene wasiyanitsidwa ndi Mulungu, mlendo ku chilungamo chake. Popeza kuti Mulungu anakonza kuti mkazi akhale mbali imodzi ya Thupi lake, Mpingo, ngati satero amakhala wa chigololo posiyanitsidwa ndi Mulungu ndi kukhala m'moyo wa uchimo.

M'bukhu la Miyambo timapezamo makhalidwe angapo a mkazi "wachilendo." Ngakhale si makhalidwe onse mwa awa omwe angaoneke mwa mkazi wachilendo, komabe chikhalidwe chirichonse chitha kuonekera m'moyo wa mkazi wachilendo.

**WOSAONA MTIMA**

Mkazi wachilendo amagwiritsa ntchito malankhulidwe opsapsalika, kuyamikira osati kuchokera pansi komanso ndi zolinga zolakwika. Miyambo akutiphunzitsa kuti mkazi wotereyo akuyenera kupewedwa:

> **Nzeru idzakkupulumutsa kwa mkazi wachiwerwere, kwa mkazi wachilendo wosyasyalika ndi mau ache. Miyambo 2:16**
>
> **Ndipulumutse wekha ngati mphoyo kudzanja la msaki ndi mballame ku dzanja la msodzi. Miyambo 6:24**
>
> **Kuti zikuchinjirizire kwa mkazi wachiwerewere kwa mlendo wamkazi wosyasyalika ndi mau ache Miyambo 7:5**

**WOIPA**

Chimodzi cha zolinga za Bukhu la Miyambo ndicho kupereka mfundo.

> **Zikuchinjiriza kwa mkazi woipa ndi ku lilime losyasyalika la mkazi wachiwerewere. Miyambo 6:24**

**OWONONGA**

Mkazi wachilendo amafuna kuononga ena ndikuwatsogolera ku uchimo:

> **Pakuti ukayamba ndi ndi mkazi wadama udzamariza ndi nyenyeswa; ndipo mkazi wa mwini amasaka moyo wa mtengo wapatari. Miyambo 6:26**

**OPANDA ULEMU**

Mkazi wauchimo amavala mosadzilemekeza:

> **Ndipo taona mkaziyo anamchingamira, Atabvala zadama wochenjera mtima. Miyambo 7:10**

**WOCHENJERA PAKAMWA**

Mkazi wachilendo ndi wa pakamwa ponyenga komanso pochenjera:

> **Ndipo taona mkaziyo anamchingamira, Atabvala zadama wochenjera mtima Miyambo 7:10**

Amafotokozeredwa monga dzenje la msampha lopangitsa ena kugwamo:

> **Pakuti mkazi wadama ndiye dzenje lakuya; Ndipo mkazi wachiwerewere ndiye mbuna yopatiza. Miyambo 23:27**

Amalankhula mau onyenga okopa ena kuti agwe mu uchimo:

> **Pakuti milomo ya mkazi wachiwerewere ikukhala uchi; M'kamwa mwache muti see koposa mafuta Miyambo 5:3**

**WAMAKANI**

Amakhala akukangana ndi ena nthawi zambiri:

> **Mwana wopusa ndiye Tsoka la atate wache ndipo makangano a mkazi ndiwo kudothadothabe. Miyambo 19:13**
>
> **Kudothadotha tsiku lamvula ndi mkazi wolongolola ali amodzimodzi. Miyambo 27:15**
>
> **Kukhala m'chipululu kufunika kuposa kukhala mkazi wolongolola wong'ung'udza. Miyambo 21:19**

**WOLONGOLOLA**

Mavesi awiri amalankhula za kulongololа kwa mkazi wachilendo. Kutanthauza kuti amakhala akulankhula mokweza komanso mwa mapokoso. Miyambo akuchenjeza kuti:

> **Kukhala m'chipululu kufunika koposa kukhala mkazi wolongolola wong'ung'udza. Miyambo 21:9**

Ngakhale ngodya ya denga iri bwino poyerekeza ndi mkazi wolongolola:

> **Kukhala pa ngodya ya tsindwdi kufunika kuposa kukhala m'nyumba ndi mkazi wolongolola. Miyambo 25:24**

**WACHIGOLOLO**

Mkazi wachigolololoyu atha kukhala ndi zibwenzi za mtseri zomagonana nazo. Apotu wakhala wachigololo popeza kuti wanyozera ubale wake ndi Mulungu:

> **Chomwecho njira ya mkazi wachigololo adya, napukuta pakamwa, nati Sindinachita zoipa. Miyambo 30:20**

> **Pakuti ukondwerenji mwanawanga ndi mkazi wachiwerewere ndi kufungatira chifuwa cha mkazi achilendo? Miyambo 5:20**

**WODZILUNGAMITSA YEKHA**

Mkazi wachilendo satha kuzindikira za momwe moyo wake wauzimu uliri:

Miyambo 30:20

**WAMKWIYO**

Miyambo amanena kuti mkazi wachilendo amakhala wodzala ndi mkwiyo:

> **Chomwecho njira ya mkazi wachigololo adya napukuta pakamwa nati sindinachita zoipa. Miyambo 30:23**

**WAKWIYA**

> **Kukhala m'chipululu kufunika kkuposa kukhala ndi mkazi wolongolola ndi wong'ung'udza. Miyambo 21:19**

**WOPANDA PHINDU**

Mavesi awiri amafotokozera kuti mkazi wachilendo atha kubweretsa mabvuto akulu a zachuma:

**Tenga maraya a woperekera mlendo chikole, woperekera mkazi wachiwerewere chikole umgwire mwini.**

**Tenga maraya a woperekera mlendo chikole, woperekera mkazi wachilendo chikole umgwire mwini. Miyambo 27:13 ndi 20:16**

**WOPUSA NDI WOLONGOLOLA**

Kukhala wopusa ndiko kukhala wosowekera nzeru ndipo kukhala wolongololа ndiko kudandaula mokweza:

**Utsiru umalongolola nwa chibwana osadzidwa kanthu. Miyambo 9:13**

**WOSADZIWA KANTHU**

**Utsiru umalongolola nnnwa chibwana osadziwa kanthu. Miyambo 9:13**

**WOPANDA CHIDZIWITSO**

Kutanthauza kuti wopanda luso la kachitidwe ka zinthu. Miyambo akuyerekeza mkazi wokongola koma wopanda chidziwitso ndi chipini cha golide m'mphuno ya nkhumba.

Bukhu la Miyambo limafotokozere mkazi wachilendo ngati munthu wosowetsa mtendere. Ndi kwabwino kugona padenga (Miyambo 21:9) m'chipululu (Miyambo 21:19), kapena pangodya ya denga (Miyambo 25:24) kusiyana ndi kukhala pamodzi naye m'nyumba.

**KUSIYANITSA PAKATI PA MKAZI WACHILENDO NDI WANGWIRO**

Bukhu la Miyambo limasiyanitsa momveka bwino mkazi wachilendo kapena wopusa ndi mkazi wangwiro kapena wanzeru:

| **WACHILENDO** | **WANGWIRO** |
|---|---|
| Amaongonga nyumba yake (14:1) | Amamaga nyumba yake (14:1) |
| Wopanda chidziwitso, wosadziwa kanthu (9:13) | Wopatsidwa ulemu (11:16) |
| Chipini m'mphuno ya nkhumba (11:22) | Korona kwa mwamuna wake (12:4) |

**MZIMAYI MKAZI WA MUNTHU**

Bukhu la miyambo limafotokozera zinthu zingapo zokhuza udindo wa mzimayi ngati mkazi wa munthu. Ndipo izi zikupiriza kusiyanitsa mkazi wachilendo ndi mkazi wangwiro:

> **Nkazi wodekha ndiye korona wa mwamuna wache, koma wochititsa manyazi akunga chobuvndaitsa mafupa a mwamunayo. Miyambo 12:4**

Azibambo akuchenjezedwa za maubwenzi achigololo ndi akazi:

**Udzagona mpaka liti wolesi iwe? Udzauka ku tulo takko liti? Miyambo 6:29**

> **Wochita chigololo ndi mkazi alibe nzeru wofuna kuonga moyo wache wache ndiye amatero. Miyambo 6:32**

Mwamuna akuyenera kukhutitsidwa ndi mkazi wake osati akazi achilendo:

**Adalitsike kasupe wako, ukondwere ndi mkazi wokula naye. Miyambo 5:18**

Mkazi wangwiro ndi mphatso yochokera kwa Mulungu:

**Ula uletsa makangano nulekanitsa amphamvu. Miyambo 18:22**

Mkazi wanzeru amachokera kwa Ambuye

> **Nyumba ndi chuma ndizo cholowa cha atate koma mkazi wanzeru achokera kwa Yehova. Miyambo 19:14**

Mkazi wachilendo amakhala wa makangano ndi woyesa mopirira

> **Mwana wopusa ndiye Tsoka la atate wache ndipo makangano a mkazi ndiwo kudothadothabe. Miyambo 19:13**

**MKAZI WANGWIRO**

Atatha kufotokozera mkazi wopusa m'bukhu la Miyambo, wolemba akumaliza ndi kafotokozeredwe kabwino ka mkazi wangwiro:

> **Mkazi wangwiro ndani angampeze? Pakuti mtengo wache uposa ngale. Miyambo 31:10**

Werengani Miyambo 31:10-31 ndipo muona mwatsatane tsatane za makhalidwe a mkazi wangwiro. Pamene mukhale mukuona za makhalidwe a mkazi wangwiro Baibulo lanu likhale lotsegula.

Kumbukirani kuti monga momwe mkazi wochimwa sangaonetsere makhalidwe onse a mkazi wachilendo, chomwechonso kuti makhalidwe otsatirawa sikuti angaonekere onse mwa mkazi wangwiro. Amachita kubwera pamene munthu akukula muuzimu, komabe, akutipatsa chithunzithunzi cha mkazi wabwino.

Tsopano tisanthula vesi iliyonse mu ndime yofotokozera za makhalidwe a mkazi wangwiro:

**VESI 10**

Mkazi wangwiro ndi osowa monga wolemba afunsira, “Mkwazi wangwiro angampeze ndani?” Kukhala wangwiro ndiko kukhala ndi makhalidwe okoma. Mkazi wotere amatengedwa kukhala wamtengo wache wapatali monga miyala yapamwamba.

**VESI 11**

Ndi wodalirika ndipo mtima wa mwamuna wake ukhutitsidwa naye.

**VESI 12**

Maubale ake amakhala abwino. Amafunira mwamuna wake zabwino zokhazokha. Mau oti “zabwino” amaphatikizapo kutonthoza ndi kulimbikitsa.

**VESI 13**

Amachita malonda ndi kugwira ntchito molimbika

**VESI 14**

Amasalira nyumba yake  ndi zonse zofunikira kuuzimu ngakhalenso kuthupi.

**VESI 15**

Amakhala wachifundo ndi wokhuzika. Amadzuka m’mawa kufuna zinthu zoti asamalire banja lake. Izi zimatanthauzanso ngakhale kuuzimu. Kudzuka m’mawa kukakumana ndi Mulungu. Amayang’aniranso bwino antchito ake ndikuwapatsa zosowa zawo.

**VESI 16**

Amalingalira mozama kaye asanachite kanthu kalikonse. Ndi wamachawi komanso wopindulitsa pa ntchito iriyonse yomwe Mulungu wampatsa. Ndiko kukhala wosanyozera udindo wake ndi kukula mwanzeru.

**VESI 17**

Mkazi wangwiro amakhala wamphamvu kuuzimu, m’malingaliro komanso kuthupi kuti akathe kugwira ntchito yomwe Mulungu wampatsa.

**VESI 19**

Amakhala waluso wophunzitsika pa ntchito yake. Amadziwa kugwiritsa bwino ntchito zipangizo zake pa malonda ake.

**VESI 21**

Mkazi wangwiro amakhala wopanda mantha. Amaveka banja lake osati kuthupi kokha, ngakhalenso kuuzimu. Ahebri 9:19-21 amalankhula za kuvekedwa muuzimu ndi mwanzi wa Yesu Khristu.

**VESI 22**

Ndime iyi imafotokozera mkazi wangwiro monga wosamalira nyumba yake mwaluso komanso wovala bwino.

**VESI 23**

Amathandizira udindo wa mwamuna wake.

**VESI 24**

Wochita malonda bwino

**VESI 25**

Ndi wamphamvu, waulemu, ndi woyang'ana za mtsogolo mwamsangala.

**VESI 26**

Ndi wamzeru ndi kutumikira kudzera mkulankhula kwake. Amadziwa kumanga lilime lake ndipo ndiwachifundo.

**VESI 27**

Amakhala woyang'anira bwino nyumba yake. Si waulesi, koma wa machitachita ndi wachangu.

**VESI 28**

Mkazi wangwiro amakhala mkazi wabwino pakhomo komanso mai wabwino kwa ana ake.

**VESI 29**

Amachita bwino m'makhalidwe abwino. Mzimu wopambana umaonekera m'moyo ndi utumiki wake.

**VESI 30**

Amakhala wopambana mu zochita zake zonse ndipo anthu amaona. Amaopanso Mulungu.

**VESI 31**

Adzakhala wobalal zipatso ndipo anthu adzamtama chifukwa cha ntchito zake. Sachita kufuna anthu amkweze popeza ntchito za manja ake zimamchitira umboni.

## CHINSINSI CHA MKAZI WANGWIRO

Kodi chinsinsi cha mkazi wangwiro ndi chiyani? Kodi angakwanitse bwanji kukhala ndi makhalidwe okoma otere?

Amaopa Ambuye! Chilungamo chake chonse, makhalidwe odabwitsa ake onse amachokera mu ubale wake ndi Mulungu.

Kuopa Mulungu sikungomupatsa ulemu chabe. Zimaphatikizapo kumzindikira monga Mulungu, kuzindikira ndi kubvomereza chimo lako, komanso kumlandira Yesu monga Mpulumutsi. Pamene ukhala wolengedwa watsopano mwa Khristu, zinthu zonse zakale zimakhala kuti zatha.

> **Chifukwa chache ngati munthu ali yense ali mwa khristu ali wolengedwa watsopanao zinthu zakale zapita, taonani zakhala zatsopano. 2 Akorinto 5:17**

Mkazi wangwiro anakhuzidwa ndi tchimo lomwe linadza kwa anthu onse kudzera mwa tchimo la Adam ndi Hava. Kusiyana komwe kulipo pakati pa iye ndi mkazi wochimwa ndi kwakuti mkazi wangwiro si wochimwanso ayi. Wayeretsedwa ndi mphamvu yopulumutsa ya Khristu.

Moyo wanu utha kuonongeka ndi tchimo. Mutha kukhala ndi makhalidwe ambiri a mkazi wochimwa m'moyo wanu. Tsopano, kudzera mwa Khristu, mutha kusinthika kuchokera ku mkazi wochimwa kuti mukhale mkazi wangwiro. Mutha kubwezeretsa ubale wanu ndi Mulungu ndi kumlola Iye kuti abweretse makhalidwe okoma a mkazi wangwiro m'moyo wanu.

Chomwe mukuyenera kuchita ndi kubvomereza tchimo lanu ndi kulandira Yesu Khristu ngati Mpulumutsi wanu. Ngati simunapange chinganizo ichi, pempherani kwa Mulungu panokha ndipo muchite izi panopa.

## KUOMBA MKOTA

Vesi limodzi likuomba mkota wa zomwe Bukhu la Miyambo limaphunzitsa pa phunziro la akazi. Ndi kusiyanitsa komaliza kwa pakati pa mkazi wachilendo ndi mkazi wangwiro.

> **Kukongola kungonyenga maonekedwe okoma ndi chabe mkazi woopa Yehova adzatamandidwa. Miyambo 31:30**

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera osaonera.

   ______________________________________________________________________

   ______________________________________________________________________

2. Kodi mau oti “Miyambo” amatanthauza chiyani?

   ______________________________________________________________________

   ______________________________

3. Kodi mau oti “chilendo” amatanthauza chiyani molingana ndi momwe agwiritsidwira ntchito m’bukhu la Miyambo?

   ______________________________________________________________________

   ______________________________________________________________________

4. Kodi mau oti “wangwiro” amatanthauza chiyani molingana ndi agwiritsidwira ntchito m’bukhu la Miyambo?

   ______________________________________________________________________

   ______________________________________________________________________

5. Werengani makhalidwe omwe ali m’musimu. Ngati ndi khalidwe la mkazi wachilendo lembani “S” (strange) koma ngati ndi la mkazi wangwiro lembani “V” (virtuous)

   a. ____ Wachipha maso
   b. ____ Woipa
   c. ____ Wamtima wonyenga
   d. ____ Wamikangano
   e. ____ Korona kwa mwamuna
   f. ____ Chipini m’mphuno ya nkhumba
   g. ____ Wamadano
   h. ____ Wovuta kupeza
   i. ____ Wopanda chidziwitso
   j. ____ Wokwiya
   k. ____ Wopusa
   l. ____ Wamalonda
   m. ____ Waluso
   n. ____ Wodzilungamitsa
   o. ____ Waphokoso
   p. ____ Wokhulupirika
   q. ____ Woopa Mulungu
   r. ____ Woyera.

(Mayankho onse a mafunso awa ali kumapeto kwa bukhu lino)

**KUPITIRIZA KUPHUNZIRA**

1. Ngati munadzipereka mwapadera kwa Khristu Yesu, m'pempheni kuti akukhululukireni tchimo lanu, ndipo mumulandire monga Mpulumutsi wa moyo wanu. Tikufuna titadziwa. Tilembereni kalata ndipo mutidziwitse za chisankho chomwe munapanga.
2. Kuti mupitirize kuphunzira zomwe Miyambo amaphunzitsa za azimayi, vesi iliyonse yalembedwa m'musimu. Malo aperekedwa oti inu mulembepo ndemanga yanu pa vesilo momwe mukudziwira.

**Ndime** **Ndemanga**

2:16 ________________________________________

5:3 ________________________________________

5:18 ________________________________________

5:20 ________________________________________

6:24 ________________________________________

6:26 ______________________________________

6:29 ________________________________________

6:32 ________________________________________

7:5 ________________________________________

7:10 ________________________________________

9:13 ________________________________________

11:16 ________________________________________

11:22 ________________________________________

12:4 ________________________________________

14:1 ________________________________________

18:22 ________________________________________

________________________________________

19:13

19:14

20:16

21:9

21:19

23:27

25:24

27:13

27:15

30:20

30:23

31:10-31

## CHAPUTALA 4

## BUKHU LA RUTE

### ZOLINGA

Pomaliza pa phunziro lino muyenera kukwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kulemba mwachidule nkhani ya Rute
- Kupeza cholinga cha bukhuli
- Kufotokozera ubale wa Rute ndi Boaz ngati chithunzithunzi cha Khristu ndi Mpingo
- Kuzindikira kuti Mulungu amagwiritsa ntchito nyengo zosiyanasiyana kuti akwaniritse madongosolo ndi zolinga zake

### VESI LOTSOGOLERA

> **Nati Rute musandiumirize kuti ndikusiyeni, ndi kubwerera osakutsatani pakuti kumene mumukako ndi muka inenso ndi kumene mugonako ndigona inenso anthu a kwanu ndiwo anthu a kwa inenso, ndi Mulungu wanu ndiye Mulunguwanga**
>
> **Kumene mudzafera inu ine ndidzafera komweko ndi kuikidwa komweko andilange Yehova naonjezeko chiri chonse chikasiyanitsa inu ndi ine koma imfa ndiyo Rute 1:16-17**

### MAU OYAMBA

M'baibulo muli mabuku awiri omwe atchulidwa maina a azimayi. Mabukuwa ndi Rute ndi Estere. M'phunziro lino tiphunzira za bukhu la Rute, mkazi wa amitundu yemwe anatumikira Mulungu pakati pa anthu a Chiyuda. Ndipo m'chaputala chotsatiracho tiphunzira za Bukhu la Estere, mkazi wa Chiyuda yemwe anatumikira Mulungu pakati pa anthu Amitundu. Musanapilire ndi phunziro lino werengani machaputala anayi a Bukhu la Rute.

### DZINA

Bukhuli likutchulidwa kuti Rute, mpongozi wa Naomi. Rute anali m'Moabu Naomi anali Myuda. Amoabu anali mtundu wa anthu omwe anachokera ku ana a Loti ndipo anali osakhulupirira Mulungu. Rute ndi m'modzi mwa akazi anayi omwe akutchulidwa pa Mateyu 1 ngati makolo ake a Yesu, Mesiya. Atatu enawo ndi Tamara, Rahab, ndi Bathsheba.

### WOLEMBA

Amene analemba bukhuli sakudziwika mpaka pano.

## NTHAWI

Nthawi ya zochitikachitika za m'bukhuli yatchulidwa mu vesi loyamba la chaputala choyamba chomwecho. Nkhaniyi inachitika nthawi ya oweruza yomwe inali nthawi ya mavuto kwambiri mu mbiri ya anthu a Mulungu, Israel. Munalibe mfumu mu Israel ndipo anthu anachoka pamaso pa Mulungu nakhala moyo wa chitayiko:

> **Masikuwa panalibe mfumu m'Israeli, yense anachita chomuyenera m'mso mwache. Oweruza 17:6**

Bukhu la Oweruza limafotokozera zomwe zinachitika mu nthawi ya mdima imeneyi. Anthu anachimwira chimwirabe, nalandira chilango cha Mulungu, natembenukira kwa Mulungu kuti awamasule. Ndipo kuti nthawi zonse Mulungu amadzutsa woweruza (mtsogoleri wa Umulungu) kuti awamasule.

## ZOMWE ZINACHITIKA

Zomwe ziri m'bukhuli zinachitika malo awiri:

Ku Moabu, komwe Naomi ndi banja lake anathawira chifukwa cha njala mu Israel (chaputala 1:1-18).

Ku Betelehemu ku Israel, komwe nkhani ina yonse inachitikira (chaputala 1:19-22 mpaka chaputala 4).

## WOLEMBEREDWA BUKHULI

Bukhuli linalemberedwa Israel ngati limodzi mwa mabuku awo a mbiri. Linalemberedwanso okhulupirira ubale wopulumutsa wa Yesu Khristu.

## ANTHU OPEZEKA MU NKHANIYI

Anthu akupezeka m'bukhu la Rute ndi awa:

Naomi: Mkazi wa Chiyuda yemwe anapita ku Moabu ndi mwamuna wake pamodzi ndi ana awo awiri kuthawa njala mu Israel.

Elimelech: Mwamuna wake wa Naomi yemwe anafera ku Moabu komweko.

Maloni ndi Kilioni: Ana a Naomi omwe anaferanso ku Moabu.

Olipa: Mpongozi wa Naomi yemwe anali m'Moabu ndipo anasankha kukhalabe ku Moabu.

Rute: Mpongozi wa Naomi yemwe anali m'Moabu ndipo anasankha kupita ku Israel pamodzi ndi Naomi.

Boazi: Mwana wa Rahab ndipo ndi amene anaombola Rute nakhala mkazi wake.

Wachibale wosatchulidwa: Munthu uyu satchulidwa dzina m'bukhuli ndipo ndi amene amayenera kuombola katundu wa Naomi ndi kutenga Rute kukhala mkazi wake, koma sanankhe kutero.

## CHOLINGA

Bukhu la Rute liri ndi zolinga zingapo:

1. Limaonetsera chikondi cha Mulungu pa anthu a mtundu uli wonse. Rute anali wamitundu wa Chimoabu, koma Mulungu anasankha mkazi wa mtundu wosakhulupirira ameneyu kukhala wa m'badwo umene Yesu Khristu anabadwira. Rute anali gogo wamkulu wa Mfumu Davide, kholo la Mesiya.
   Ichi ndi chithunzithunzi cha momwe Mulungu amatengera anthu amitundu kukhala mbali imodzi ya banja lake kudzera m'mwazi wa Mwana wake, Yesu Khristu.
   Mulungu sayang'ana nkhope: Komatu mu mtundu uli wonse iye amene amvera Iye ndi kuchita chilungamo, amalandiridwa pamaso pake (Machitidwe 10:34-35).
2. Limatipatsira m'badwo wake wa Yesu Khristu. Chaputala chomaliza chimafotokozera za mbiri ya banja ya Mfumu Davide.
3. Ubale wa pakati pa Rute ndi Naomi ndi chithunzithunzi cha kudzipereka komwe kukuyenera kukhalapo pakati pa Mpingo ndi Khristu.
4. Moyo wa Naomi ukufotokozera momwe Mulungu amatengera nyengo zowawa za moyo uno ndi kuzisandulitsa kukhala zabwino.
5. Ubale wa Rute ndi Boazi ndi chithunzithunzi cha maomboledwe a pakati pa Yesu Khristu ndi Mpingo.

## MLOZO WA BUKHU LA RUTE

## CHAPUTALA 1

### ULENDO WA KU MOABU (1:1-2)

Vesi 1 ikufotokozera za nthawi ya zochitika za m'bukhu la Rute mu nthawi ya Oweruza. Imaonetseranso kuti zochitika mu chaputala 1:1-18 zinachitikira ku Moabu. Moabu anali pa mtunda wa makilomita okwana 80 kuchokera ku Betelehemu moyang'anana Nyanja Yakufa. Elimeleki anatenga mkazi wake pamodzi ndi ana ake awiri nathawira nawo kumeneku chifukwa cha njala ku Israel.

Njala inali njira imodzi imene Mulungu amagwiritsa ntchito m'Chipangano Chakale ngati chilango pa Israel akachimwa natumikira milungu yachilendo (onani 2 Mafumu 8:1; Yeremiya 16:3-13; ndi Ezekiel 5:11-17).

Elimeleki samayenera kuthawira ku Moabu popeza kuti zimatanthauza kuthawa kulanga kwa Mulungu. Dziko la Mulungu, ngakhale nthawi ya njala, liri bwino kuposa Moabu, ngakhale akhale ndi chakudya chochuruka. Anthu a ku Moabu amatumikira mulungu wotchedwa Kemosi yemwe ankamulemekeza popereka ana awo nsembe (Onani Oweruza 11:24).

## MAVUTO M'MOABU (1:3-5)

Adakali ku Moabu, Elimeleki anamwalira ndipo ana ake anakwatira akazi a Chimoabu otchedwa Olipa ndi Rute ngakhale kuti maukwati a pakati pa Ayuda ndi Amoabu anali oletsedwa ndi Mulungu (Deuteronomy 7:3; Nehemiah 13:23, 25). Mavuto anagweranso nyumbayi pamene ana onse a Naomi anamwalira. (Zitha kutheka kuti anawa anali odwaladwala monga mwa dzina lakuti "Maloni" lomwe likutanthauza "kudwala" ndipo "Kilioni" amatanthauza "kukhumba.")

## KUBWELERA KU BETELEHEMU (1:6-18)

Pamene njala mu Israel inatha, Naomi anaganiza zobwerera kunka kwao ku Betelehemu. Ndipo anauza apongozi ake awiri, Olipa ndi Rute, kuti akhalire ku Moabu. Chisaganizo chimene anawapatsa chinali chauzimu. Akanatha kubwelera kwa abale awo nakapitiriza kutumikira milungu ya makolo awo akanafuna. Naomi sanafune kuti Olipa ndi Rute amutsatire ku Betelehemu chifukwa cha ubale wa chipongozi kupatula kupanga chisankho chauzimu cha pa Mulungu.

Iye anawauza azipongozi akewa kuti atha kuchita bwino atakhalira ku Moabu ndikupeza mabanja ena nkukhazikika. Nthawi zina munthu akatsata njira ya Mulungu pamaoneka ngati palibe tsogolo, komano muona kuti Rute anadalitsika chifukwa anasankha njira yokhala ndi mwayi wochepa.

Olipa anapanga chisankho chakuti akhale ku Moabu ndipo anatsanzikana ndi Naomi. Anthu ambiri ena amakhala ndi chikondi cha pa Yesu koma chifukwa chokanika kusiya za moyo wao wakale, amakanika kupeza chipulumutso. Monga ngati Olipa amabwerera ku dziko kuti apeze mpumulo. Naomi anapereka mwayi kwa Rute wobwelera pamodzi ndi Olipa, koma Rute anakakamira Naomi ndi lonjezano lokoma la kudzipereka kwake osati kwa Naomi yekha, ngakhalenso kwa Mulungu wake. Vesi 18 imafotokozera chisankho cha Rute chomwe chikutseka khomo la moyo wake wakale. Kudzipereka kweni kweni kwa Yesu kumatanthauza kutseka khomo la moyo wako wakale wa uchimo.

Onani zomwe ziri mu kudzipereka kwake kwa Rute komwe ndi chithunzithunzi cha ubale wanu ndi Khristu:

1. **Kubvomereza:** Rute akubvomereza njira ya Naomi. Apita naye limodzi. Njira yoyamba pa kudzipereka kwa Yesu ndiko kubvomereza njira yake ya chipulumutso.
2. **Kukhala:** Adzakhala ndi Naomi nakhazikika. Mutatha kulandira Yesu, mukuyenera kupitirirabe mu ubale wanu ndi Iye.

3. **Kudzibweretsa pafupi:** Rute anadzibweretsa yekha pafupi ndi Naomi pamodzi ndi anthu ake, malo ake, chikhulupiriro chake komanso mabvuto ake.
- *Anthu*: Rute anadzibweretsa yekha pafupi ndi azibale ake a Naomi monga momwe ifenso tingadzibweretsere pafupi ndi okhulupirira ena m'banja la Mulungu.
- *Chikhulupiriro*: akudzibweretsa yekha pafupi ndi chikhulupiriro cha Naomi. Mulungu amene amamkhulupirira. Monga okhulupirira, mukuyenera kudzibweretsa nokha ndi Mau a Mulungu.
- *Malo*: Komwe Naomi akakhale, ndi komwenso Rute akakhale. Mukuyeneranso kudzibweretsa nokha pa malo omwe pakuchitika utumiki wa Khristu.
- *Mabvuto*: Adzakhala ndi Naomi nthawi ya mabvuto ndi nthawi ya mtendere, ngakhale mu imfa. Kudzipereka kwanu kwa Yesu kukuyenera kukhala kofikira mpaka ku imfa osati mu nthawi zokhazo zabwino ayi.

## KUFIKA KU BETELEHEM (1:19-22)

Pakufika ku Betelehemu, anzake akale a Naomi sanamzindikire nafunsa, "Kodi uyu ndi Naomi?" Mwina zaka za chisoni ku Moabu zinapangitsa maonekedwe ake kusintha. Samaonekanso momwe ankaonekera ali ku Israel. Onani kusiyana komwe kunalipo:

1. Anachoka mokondwera koma anabwera momvetsa chisoni. Anauza anthu kuti asamutchulenso kuti "Naomi" kutanthauza "chimwemwe" koma "Mara" kutanthauza "chisoni."
2. Anachoka wolemera koma anabwera wosauka. Naomi sanaloze chala satana kuti ndi amene wayambitsa mavuto ake. Iye anazindikira kuti kudzudzula kwa Yehova kumene kunampeza m'dziko la chilendo la anthu osakhulupirira komwe anapita. Nthawi zambiri sitipita chitsogolo muuzimu chifukwa chakuti timatanganidwa kuloza chala satana pamene tikulandira chilango kuchokera kwa Mulungu pa zoipa zomwe tikuchita. Tikungoyenera kusintha njira zathu za uchimo. Cholinga cha kudzudzula kwa Mulungu kwaperekedwa pa Hosea:

   > **Tiyeni, tibwrere kunka kwa Yehova pakuti wang'amba nadzatipoletsera wakantha, nadzatimanga. Hosea 6:1**

   Kudzudzula kunam'bweretsa Naomi chifupi ndi Ambuye. Sinatenge nthawi kuti Mulungu achotse chisoni cha Naomi ndi kumpanga kuti akhale mbale imodzi ya dongosolo lake lodabwitsa la pa anthu onse.

   Pamene Naomi anagwiritsa ntchito mau akuti "Ambuye" (El Shaddai mu Chihebri) amaonetsera kuti sanataye chikhulupiriro chake mwa Mulungu. Mau akulankhula za kukwaniritsidwa mwa Ambuye. Ngakhale anali wowawidwa mtima ndi wosauka, anakhulupirirabe kuthekera kwake kwa Mulungu kukwaniritsa chosowa chake. Mu njira ina amanena kuti, "Ndine wosauka, koma Mulungu ali nako kuthekera."
3. Anachoka nthawi ya njala koma anabwera nthawi ya khololа lalikuru. Werengani vesi 22. Naomi anachoka ku Israel kuli njala, koma anabwerera nthawi ya kholola lalikuru kuthupi ngakhale kuuzimu.

## CHAPUTALA 2

## RUTE KU MINDA YA BOAZI

Rute anapita kukakunkha ku munda wa Boazi zomwe sizinali za chilendo pakati atsikana nthawi imeneyo. Mulungu analamulira anthu achuma kuti azisiyako kadera kena pokolola kuti anthu osauka azipezako thandizo pamene akukunkha.

Rute anaonetsa kutengapo udindo popita kukakunkha. Simungangokhala ndi kudikira Mulungu kuti akugwirireni ntchito pa moyo wanu, koma mugwirane naye manja limodzi. Rute anachita chomwe chimayenera kuchitika. Mulungu amakondwera tikamapeza zosowa zathu zomwe zimalemekeza dzina lake (1 Akorinto 10:31).

Mkhristu sakuyenera kukhala womadzimvera chisoni. Rute sanadzimvera chisoni koma kupita kukagwira ntchito m'munda wa Boazi yemwe anali m'bale wake wa Naomi. Mulungu amakutsogolerani nthawi zonse kuti mukafikire ku zinthu zomwe zingakuthandizeni pa moyo wanu mu nyengo zanu zovuta. Boazi anamkomera mtima Rute namuuza kuti akhale ku munda komweko kufikira kutha kwake kwa kholola. Ndipo amamkozera dongosolo lapadera nthawi ya chakudya.

## RUTE ABWELERA KWA NAOMI (18-23)

Rute anabwerera kunyumba kwa Naomi namufotokozera zonse zomwe zachitika masana a tsiku limenelo. Ndipo Naomi anaona kuti dzanja la Mulungu linali pa Rute. Popeza kuti Boazi anali wachibale wa Naomi, iye anali ndi udindo pa zinthu zina m'moyo wa Rute ndi Naomi.

## CHAPUTALA 3

## DONGOSOLO LA NAOMI (1-5)

Pozindikira dzanja la Mulungu, Naomi anamuuza Rute dongosolo la kachitidwe ka zinthu. Pokhala wachibale wapafupi, Boazi anali ndi udindo woombola katundu wa Naomi, kukwatira Rute, ndi kukhala ndi ana ndi kusunga dzina la mtundu (Deuteronomo 25). Koma asanamuuze kapena kumkakamiza za udindo umenewu, Rute anadzipereka yekha mwachinsinsi usiku, kumpatsa mwayi womubvomereza ndi kumtenga kapena kumkana.

## ZOTSATIRA (6-13)

Rute anali ndi ufulu wopempha Boazi kuti "amuombole" pakumkwatira. Boazi anali wokonzeka kukwaniritsa udindo wake, koma anapereka mwayi kwa wachibale yemwe anali wapafupi kwambiri kuposa iye kuti akhale woyamba kutenga udindo umenewu. Samafuna kuoneka ngati waphangira. Si kokwanira kungogwira ntchito ya Mulungu, ntchitoyo ikuyenera kugwiridwa molingana ndi dongosolo lake. Ndipo Boazi amayenera kupita kwa wachibale uja

kumfotokozera za dongosolo limeneli kotero anamuuza Rute kuti adikire kaye kufikira m'mawa kuti alongosole zinthu.

### KUBWELERA KWA NAOMI (14-18)

Rute anabwelera kwa Naomi namfotokozera zonse zimene zachitika. Ndipo Naomi anamuuza kuti afatse popeza anadziwa kuti Boazi sakhala chete kufikira nkhaniyi itadziwika mutu wake. Mulungu sanapume kufikira chiombolo chitachitika kudzera mwa Khristu. Mulungu sakhala pansi kufikira inuyo moyo wanu utaomboledwa. Onani kuti Rute sanapite kwa Boazi chimanjamanja (18). Masiku okhala opanda kanthu omwe Naomi amanena mu chaputala 1 ali pafupi kutha.

## CHAPUTALA 4

### DONGOSOLO LA MAOMBOLEDWE

Boazi anakumana ndi wachibale uja yemwe dzina lake silinatchulidwe. Ndipo kukumana kwao kunachitikira ku chipata chachikulu pamaso pa akulu akulu. Kuchipataku ndi komwe zinthu zambiri zokhuzana ndi kayendetse ka mzinda zimachitikirako. Wachibale uja anakana kutenga udindo wake katundu wa Naomi popeza kuti amene aombole katundu wa Naomi amayeneranso kukwatira Rute ndipo ngati abereke mwana wa mwamuna ndiye kuti theka la chuma chawo lipita ku banja la Elimeleki m'malo mwa ana ake ake.

Boazi anapeza mwayi woombola Rute molingana ndi mwambo wao, ndipo izi zinachitikira pamaso pa mboni. Maomboledwe a Rute ndi chithunzithunzi cha maomboledwe athu ndi Khristu Yesu. Molingana ndi chilamulo, woombolayo amayenera:

1. Akhale wachibale (Deuteronomo 25)
2. Akhale nako kufuna (Yohane 10:18; Yesaya 53:7; Agalatiya 2:20)
3. Kukhala nako kuthekera koombola (10:11-18)
4. Akhale mfulu payekha, monga Yesu analibe uchimo.
5. Akhale ndi mtengo wake wa maomboledwe, pokhala wachibale. Tinaomboledwa ndi mwanzi wa Yesu (1 Petro 1:18-19; Levitiko 17:11; Ahebri 10:4).

Monga momwe Boazi anakwaniritsira zofunika za maomboledwe a kuthupiwa, Khristu Yesu anakwaniritsanso ndondomeko za maomboledwe athu kuuzimu.

### KULUMIKIZIKA KWA RUTE NDI BOAZI

Rute ndi Boazi anakwatirana ndipo anali ndi mwana. Naomi sanalinso wa chisoni koma wodalitsika ndi Ambuye. Mtundu wake unapitirizidwa ndipo katundu wake anaomboledwanso. Iye anatenga mwana uja namlera. Amene akutchulidwa kwambiri ku mapeto a bukhuli si Rute koma Naomi. Moyo wake wasinthika kuchokera ku chisoni kufikira ku chimwemwe.

Kaya nyengo ya moyo wanu ndi yovuta motani, Mulungu akufuna atakusinthani kuchokera ku chisoni kufikira ku chimwemwe. Akufuna atasintha dzina lanu, kuchokera ku “Mara” kuti likhale “Naomi.” Akugwira ntchito yobwezeretsa zinthu zonse zomwe zatayika ndi kukugwiritsani ntchito ngati mbali imodzi ya dongosolo lake.

## M’BADWO WA DAVIDE (18-22)

Bukhu la Rute likufika ku mapeto ndi kulumikizitsa m’badwo wa Rute ndi Davide, yemwe anali mbali imodzi ya m’badwo umene Mesiya, Yesu Khristu, anabadwirako. Izi zikuonetsera dongosolo ndi cholinga cha Mulungu pa mbiri ya dziko lapansi ndi kuti palibe chimene chimangochitika popanda cholinga. Mulungu akugwira ntchito mu nyengo zonse za pa moyo wa munthu kuti abweretse chipulumutso cha anthu a dziko lapansi.

## MAKHALIDWE A RUTE

Pali makhalidwe okoma angapo omwe aonekera m’moyo wake Rute. Werengani ndime zotsatirazo kuti muone chikhalidwe chokoma chomwe mkazi wa Mulunguyi wachionetssera. Pemphani Mulungu kuti aumbe makhalidwewa m’moyo wanu.

| **NDIME** | **CHIKHALIDWE** |
|---|---|
| 1:16-17 | Chikondi, kudzipereka |
| 1:18 | Kukhala wolimba |
| 2:2 | Kudzichepetsa, machawi, ulemu |
| 2:14 | Kudziletsa |
| 2:18-19 | Kuchita zinthu poyera |
| 2:23 | Kukhulupirika |
| 3:5 | Kumvera |
| 3:10 | Kugonjera ku lamulo la Mulungu |
| 3:14 | Kupewa maonekedwe a choipa |
| 3:18 | Kufatsa (anasiyira Mulungu zonse) |

**KUDZIYESA NOKHA**

1. Onani maina ali mu mndandanda umondi m'musimu. Ndipo mutenge nambala ya chiganizo chimene chikufotokozera munthuyo mu mndandanda winawo ndi kulemba m'malo omwe aperekedwa mu mndandanda woyambawo. Onerani chitsanzo chomwe chaperekedwacho.

| | DZINA | | KUFOTOKOZERA |
|---|---|---|---|
| 3. | Maloni ndi Kilioni | 1. | M'Israel yemwe anapita ku Moab ndi ana ake |
| | Naomi | 2. | Mwamuna wa Naomi yemwe anafera ku Moabu |
| | Elimeleki | 3. | Ana a Naomi omwe anafera ku Moabu |
| | Rute | 4. | Wachibale yemwe anaombola Rute |
| | Olipa | 5. | Mpongozi wa Naomi yemwe anatsala ku Moabu |
| | Boaz | 6. | Mpongozi wa Naomi yemwe anapita nawo ku Israel |

2. Lembani zolinga zitatu za bukhu la Rute
   a. ____________________
   b. ____________________
   c. ____________________
3. Kodi zochitika za m'bukhu la Rute zinachitika mnthawi iti?
   ____________________
   ____________________
4. Kodi ndi malo awiri ati omwe zochitika za m'buku la Rute zinachitikira
   a. ____________________
   b. ____________________
5. Kodi amene analemba bukhu la Rute ndi ndani?
   ____________________
6. Lembani Vesi Lotsogolera osaonera
   ____________________
   ____________________
7. Werengani ndime ziri m'musizi ndipo muzilemba "I" (inde) ngati mukugwirizana nacho chiganizocho ndipo lembani "A" (ayi) ngati simukugwirizana nacho chiganizocho m'malo aperekedwawo.
   a. ___ Njala inagwiritsidwa ntchito ngati njira yolangira Israel
   b. Naomi amatanthauza "kuwawidwa"
   c. Mara amatanthauza "chimwemwe"
   d. Boaz ndi yemwe anali ndi udindo woyamba wowombola Rute.
   e. Wachibale amene sanatchulidwe anakanika kuombola Rute chifukwa chakuti sanamkonde.

f. Ubale wa pakati pa Boaz ndi Rute ndi chithunzithunzi cha ubale wathu wa maomboledwe pakati pa Yesu ndi okhulupirira.

(Mayankho a mafunso awa ali kumapeto kwa bukhu lino)

## KUPITIRIZA KUPHUNZIRA

1. Werengani nkhani ya Rahab pa Yoshua 2. Kenako pitani ku Ahebri 11:31 ndipo onani kuti ali m'gulu la anthu a m'Chipangano Chakale omwe Paul akuwayamikira powonetsera chikhulupiriro chachikulu.
   Rahab anali mai wake wa Boaz, ndipo ali m'gulu la makolo a Yesu Khristu. Sizodabwitsa kodi kuti Mulungu akuphatikizapo mitundu yonse ya anthu (Rute anali m'Moabu) ndi makhalidwe awo osiyanasiyana (Rahab yemwe anali mkazi wa chigololo) kukhala makolo a Yesu ku dziko lapansi?
   Ndi chimodzi modzinso m'banja lauzimu la okhulupirira. Sizikutengera mtundu, chikhalidwe kapena mbiri ya munthu. Aliyense atha kubwera kwa Yesu napeza chipulumutso kukhala m'modzi wa banja la Mulungu.
2. Kuti mudziwe zambiri za nthawi yomwe nkhani ya Rute inachitikira, werengani Bukhu la Oweruza. Onani kuti maulendo asanu ndi awiri omwe Israel analowa mu uchimo kulapa ndi kubwerera kwa Mulungu. Pamene mukuwerengani malizani tchati chiri m'musimu koma ulendo woyambawo takupatsani monga chitsanzo:

## MAULENDO 7 A OWERUZA

**Ulendo Woyamba: Oweruza 3:7-11**

Tchimo: Kupembedza mafano

Nthawi ya chilango: Zaka 8

Oweruza ndi Mpulumutsi: Otiniel

**Ulendo Wachiwiri: Oweruza 3:12-31**

Tchimo: ________________________________

Nthawi ya chilango: ______________________

Oweruza ndi Mpulumutsi: _________________

**Ulendo Wachitatu: Oweruza 4 ndi 5**

Tchimo: ________________________________

Nthawi ya chilango: ______________________

Oweruza ndi Mpulumutsi: _________________

**Ulendo Wachinayi: Oweruza 6-8:32**

Tchimo: ______________________________

Nthawi ya chilango: _____________________

Oweruza ndi Mpulumutsi: ________________

**Ulendo Wachisanu: Oweruza 8:33-10:5**

Tchimo: ______________________________

Nthawi ya chilango: _____________________

Oweruza ndi Mpulumutsi: ________________

**Ulendo Wachisanu ndi Chimodzi: Oweruza 10:6 mpaka chaputala 12**

Tchimo: ______________________________

Nthawi ya chilango: _____________________

Oweruza ndi Mpulumutsi: ________________

**Ulendo Wachisanu ndi Chiwiri: Oweruza 13-16**

Tchimo: ______________________________

Nthawi ya chilango: _____________________

Oweruza ndi Mpulumutsi: ________________

# CHAPUTALA 5

# BUKHU LA ESTERE

## ZOLINGA

Pomaliza pa phunziro lino mukuyenera kumakwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera
- Kufotokozera mwachidule nkhani ya Estere
- Kuzindikira cholinga cha Bukhu la Estere
- Kuzindikira kuti Mulungu ali ndi dongosolo lapadera pa moyo wanu.

## VESI LOTSOGOLERA

> **Pakuti ukakhala chete konse tsopano lino, chithanidzo ndi chipulumutso zidzafuma kwina koma iwe ndi nyumba ya tatate wako mudzaonongeka ndipo kaya kapena walowera ufumu chifukwa cha nyengo yonga iyi. Estere 4:14**

## MAU OYAMBA

Mu chaputala chapitachi, mwasanthula Bukhu la Rute, mkazi Wamitundu yemwe anakhala pakati pa Ayuda. Chaputala chino chikhala chikukamba za Estere, mkazi Wachiyuda yemwe anatumikira ngati mfumukazi pakati pa Amitundu. Bukhuli, lomwenso linatchulidwa dzina lake limafotokozera za chiwembu chofuna kuononga mtundu wonse wa Chiyuda womwe kumapeto kwake kumayenera kubadwa Mesiya, Yesu Khristu. Musanapirize phunziroli, yambani mwawerenga kaye Bukhu la Estere.

## DZINA

Bukhuli linatchulidwa kuti Estere, popeza kuti ndiye mwini wa nkhani. Dzina lake la Chihebri ndi Hadasa ndipo limatanthauza “nyenyezi ya kum’mawa.”

## WOLEMBA

Amene analemba Bukhu la Estere sadziwika.

## NTHAWI

Nkhani ya Estere inachitika m’nthawi ya mfumu yomwe imadziwika kuti Ahaswero. Ndipo bwalo la milandu komanso miyambo ya chikhalidwe yomwe ikupezeka mu nkhaniyi, zikuchitira umboni kuti zinachitikadi mu nthawi ya Mfumu Ahaswero yomwe ndi cha m’ma 473 B.C.

## MALO OCHITIKIRA ZINTHU

Nkhaniyi inachitikira ku nyumba ya mfumu ku Susani, yomwe inali mu mzinda wa Elamu pa mtunda wa makilomita 241 kum'mawa kwa Babulo. Ayuda pafupifupi zikwi zitatu anali kukhala kumeneko pa nthawiyi.

## WOLEMBEREDWA BUKHULI

Zitha kutheka kuti bukhuli linalemberedwa Ayuda omwe anali omwazikana Perezi yense ndi Palestina kuwafotokozera momwe Mulungu anawapulumutsira ku imfa. Kwa Mkhristu, likuonetsera dzanja la Mulungu likugwira ntchito m'malo mwa ana ake.

## ANTHU OPEZEKA MU NKHANIYI

**Ahaswero**: Mfumu yolamulira madera okwana 127 kuchokera ku India kufika ku Ayitopia.

**Vashiti**: Mfumukazi yomwe idakana zomwe mfumu inalamula ndipo inachotsedwa pa mpando wa ufumukazi.

**Estere**: Mfumukazi yatsopano, mkazi wa Chihebri.

**Modekayi**: Malume ake a Estere omwe anamulera kuyambira ali wamng'ono.

**Haman**: Mdani wa anthu a Mulungu yemwe anakonza chiwembu chofuna kuononga Ayuda.

## ZOLINGA

Zolinga za Bukhu la Estere:

1. Bukhuli liri ndi nkhani yofunika kwambiri mu mbiri ya Ayuda yomwe inapereka chitsimikizo kwa Ayuda okhala ku Perezi ndi Palestina pofotokozera momwe dzanja la Mulungu linawapulumutsira.
2. Bukhuli limaonetsera momwe Mulungu amagwirira ntchito m'malo mwa ana ake. Amalowerera mu nyengo za anthu kukwaniritsa chifuniro chake komanso kuika anthu m'malo oyenerera mu nthawi yonerera pofuna kukuza Ufumu wake.

## MLOZO WA BUKHU LA ESTERE

## CHAPUTALA 1

### PHWANDO LALIKURU (1-9)

Ahaswero anakonzera akalonga ndi antchito ake phwando lalikuru lomwe linatenga miyezi isanu ndi umodzi (6). Nthawi yonseyi, Mfumukazi Vashiti nayenso anali akuchita phwando ndi azimayi m'zipinda zina za nyumba yachifumu.

### VUTO (10-12)

Pa tsiku la chisanu ndi chiwiri la phwando, mfumu inayitana Mfumukazi Vashiti kuti ibwere kudzaonetsera kukongola kwake kwa azibambo. Vashiti anakana ndipo mfumu inakwiya kwambiri.

### LAMULO LACHIFUMU (13-22)

Amuna anzeru analangiza mfumu kuti ichotse Vashiti pa udindo wa mfumukazi ndi kuikapo munthu wina.

## CHAPUTALA 2

### KUSAKASAKA MFUMUKAZI (1-4)

Mfumu inayamba kusakasaka mfumukazi. Anamwali anabweretsedwa kuchokera madera onse a ufumu nakonzekeretsedwa pamaso pa mfumu.

### ESTERE ALOWA NAWO MU MPIKISANO (5-11)

Munthu wina wa Chiyuda wotchedwa Modekayi anali kulera mdzukulu wake wotchedwa Estere popeza anali wamasiye. Iye analo nawo mu mpikisano wa ufumukazi. Modekayi anauza mtsikanayo kuti asauze wina aliyense kuti iye anali wa fuko la Chiyuda, kenano anadikira kuona chomwe chichitike kwa iye.

### ESTERE APAMBANA MPIKISANO (12-21)

Atsikana onse anaonekera pamaso pa mfumu payekha payekha. Pamene Estere anakaonekera, iye anapambana ndipo phwando lapadera linakonzedwa pokondwerera kupambana kwake.

### CHIWEMBU CHOFUNA KUPHA MFUMU (22-23)

Amuna awiri, Bigitana ndi Teresi, anakonza chiwembu chofuna kupha mfumu. Mordekai atadziwa za chiwembu anauza Estere kuti adziwitse mfumu ndipo amunawo ananyongedwa.

## CHAPUTALA 3

### KUKWEZEDWA KWA HAMAN (1-6)

Mfumu Ahasuero anakweza Haman, m'modzi mwa antchito ake, pa udindo woyang'anira akalonga ndi akapolo onse. Aliyense amampatsa ulemu kupatula Mordekai, ndipo Haman anakwiya.

### CHIWEMBU CHA HAMAN (7-15)

Podziwa kuti Mordekai anali Myuda, Haman anapita pamaso pa mfumu namnyengerera kuti aike tsiku loti Ayuda onse aphedwe. Ndipo Mfumu inavomereza kukhazikitsidwa kwa lamulolo nalengeza dziko lonse za chinthuchi.

## CHAPUTALA 4

### KULIRA KWA AYUDA (1-11)

Pamene Ayuda anamva nkhani yomvetsa chisoniyi, anayamba kulira. Mordekai anavala ziguduli nadzola phulusa ngati munthu wachisoni monga mwa chikhalidwe chawo pamene munthu akubuma.

### NKHANI IMPEZA ESTERE (9-12)

Popeza anali mkati mwa nyumba yachifumu, Estere sanamve konse za lamulo latsopanolo. Koma atamva kuti Mordekai wavala ziguduli komanso wadzola phulusa, anamtumizira zovala.koma Mordekai anakana zovala zokongolazo, ndipo anamtumizira chikalata cha lamulolo.

### DONGOSOLO LA MAMASULIDWE (10-17)

Estere ndi Mordekai anakonza dongosolo la chipulumutso. Dongosolo linali lakuti Ayuda onse asale kudya ndi kupempherera Estere ndipo iye apita pamaso pa mfumu kukafuna thandizo la chipulumutso cha anthu ake.

Munthu aliyense akafika pamaso pa mfumu osayitanidwa amaphedwa, koma Estere analolera kupereka dipo ngati kunali kotero. Iye anati, "Ngati ndikafe, ndikafe."

Vesi lotsogolera, Estere 4:14, ikupereka phunziro lofunikira. Mulungu anali ndi dongosolo la chipulumutso. Estere akanalephera kukwaniritsa udindo wake, chipulumutso cha Ayuda chikanachokera kwina.

Mulungu ali ndi dongosolo lapadera kwa wina aliyense wa ife mu dongosolo lake lofikira dziko lapansi ndi Uthenga Wabwino. Chokhumba chake ndi chakuti inu mupeze gawo lanu mu

dongosolo limeneli kuti mukakwaniritse cholinga chake. Koma ngati simupeza malo anu mu Ufumu wa Mulungu, Iye apirirabe ndi dongosolo lake pogwiritsa ntchito anthu ena.

Monga Estere, mwabwera mu ufumu wa Mulungu ndi cholinga chapaderadera. Ichi nchifukwa chake nkofunika kupeza gawo lanu mu utumiki wa Thupi la Khristu.

## CHAPUTALA 5

### KUITANIDWA KU PHWANDO (1-8)

Estere anakaonekera pamaso pamfumu ndipo iye inamulandira. Estere anakonzera mfumu ndi Haman chakudya kumene anakawaitanira ku phwando lapaderadera tsiku lotsatiralo.

### KUDZIKUZA KWA HAMANI (9-14)

Haman atangochoka pamenepo ananka nauza anzake onse mwa matama kuti waitanidwa ku phwando lapadera ku nyumba yachifumu. Zonsezi sizinabweretse chimwemwe m'moyo wake popeza Mordekai anakanisitsabe kumpatsa ulemu. Mkazi wa Haman ndi anzake ena anamuuza kuti akonze mitengo yoti apachikepo Mordekai. Haman anakondwera ndi ganizolo ndipo mitengo inakonzedwa yoti ampherepo Mordekai.

## CHAPUTALA 6

### MORDEKAI ACHITIRIDWA ULEMU

Usiku umenewu mfumu sinagone tulo ndipo amawerenga mabukhu a kubwalo la mfumu. Iye anapeza kuti Mordekai anaulula chiwembu chakupha mfumu. Mfumu inafunsa za mphoto yomwe Mordekai analandira pa ntchito yaikulu yomwe anagwira ndipo anazindikira kuti sanachitiridwe kena kali konse.

### HAMAN ACHITITSIDWA MANYAZI (12-14)

Kutacha m'mawa, Haman anapita kwa mfumu kukapempha chilolezo chofuna kupha Mordekai. Koma asanalankhule, Mfumu inalamula Haman kuti akonze dongosolo lochitira ulemu Mordekai pa ntchito yomwe anagwira. Haman anali wokhumudwa kwambiri kuti mdani wake analemekezedwa koma anachitabe monga mwa lamulo la mfumu.

## CHAPUTALA 7

### PHWANDO LA ESTERE (1-6)

Estere anakonzera mfumu phwando ndipo anaulura kuti iye ndi Myuda komanso chiwembu cha Haman chofuna kupha anthu a mtundu wake.

## HAMAN ALANDIRA CHILANGO (7-10)

Mfumu inalamula kuti Haman apachikidwe pa mitengo yomwe anakonza kuti apachikepo Mordekai.

## CHAPUTALA 8

## LAMULO LATSOPANO LOCHOKERA KWA MFUMU (1-14)

Estere anapempha mfumu kuti itulutse lamulo lopulumutsa anthu ake. Ndipo mfumu inatumiza lamulo loletsa kuphedwa kwa Ayuda onse.

## MORDEKAI ALANDIRA ULEMU (15-17)

Mordekai analandira ulemu wina kuchokera kwa mfumu, ndipo Ayuda a m'madera onse anakondwera nachita mapwando. Lamulo loyamba lomwe limabweretsa imfa kwa Ayuda ndi chithunzithunzi cha imfa yomwe inabwera pakati pa anthu chifukwa cha uchimo. Baibulo limati, "Moyo wochimwawo, udzafa."

Lamulo lachiwiri linabweretsa moyo osati imfa, monga momwe kubwera kwa Khristu Yesu kunabweretsa moyo pakati pathu. Lamulo lachiwiri silichotsa loyambalo lomwe ndi la imfa koma, monga momwe lamulo la Ahasuero, limapereka mpaka wothawa.

## CHAPUTALA 9

## KUPULUMUTSIDWA KWA AYUDA (1-11)

Ayuda anamasulidwa ku imfa. Ndi chilolezo cha mfumu, anamenyana ndi adani awo nawagonjetsa.

## NYUMBA YA HAMAN IONONGEDWA (12-16)

Maomboledwe a Ayuda anafika pachimake pamene banja lonse la Haman linaonongedwa.

## PHWANDO LA PURIM (17-32)

Phwando lapadera lokondwerera kuomboledwa kwa Ayuda linakonzedwa ndipo anakhazikitsa tsiku lakuti azikondwerera ichi chaka ndi chaka.

## CHAPUTALA 10

Mordekai anasankhidwa kuti akhale wotumikira pafupi ndi amfumu ndi kulankhula mavuto a Ayuda pamaso pake. Mordekai ndi Haman akupereka kusiyana pa kagwiritsidwe ntchito ka mphamvu munthu akakhala pa udindo. Wina anagwiritsa ntchito udindo wake kutumikira anthu ena pamene wina anagwiritsa ntchito udindo wake pofuna kuononga anthu.

## MAKHALIDWE A ESTERE

Estere anaonetsera makhalidwe abwino angapo. Werengani mavesi omwe ali m'musimu. Mpempheni Mulungu kuti aikize makhalidwewa m'moyo wanu:

| NDIME | CHIKHALIDWE |
|---|---|
| 2:15 | Wongokola, wodzisunga |
| 2:9-17; 5:1-3 | Wa maonekedwe okoma |
| 2:10 | Womvera |
| 2:15 | Wokhala bwino ndi anthu |
| 2:22 | Wosafuna za iye mwini (anapempha za chipulumutso cha anthu ake) |
| 4:16 | Wodzichepetsa |
| 4:16; 7:6 | Wolimba mtima |
| 2:22; 8:1-2; 7:3-4 | Waulemu |

## PHUNZIRO LOFUNIKIRA

Mfundo yofunikira kwambiri m'phunziro lino ndilakuti ngakhale kuti oipa atha kuoneka kuti akuchita bwino, mapeto ake, anthu adzapambana.

Davide analankhula za ichi m'Masalimo. Anakhala ngati waumba mkota wa zomwe zinachitika m'Bukhu la Estere.

Masalimo 37:35-40

## KUDZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi Lotsogolera osaonera
   ______________________________________________________________________
   ______________________________________________________________________
   ______________________________________________________________________
   ____________________
2. Tchulani zolinga ziwiri za Bukhu la Estere
   a. ______________________________________________________________________
   b. ______________________________________________________________________
3. Onani mndandanda wa maina mu gawo loyamba. Pezani chiganizo chomwe chikufotokozera bwino dzina limenelo. Ikani nambala ya chiganizocho kumayambiliro kwa dzina loyenerera:

| | **DZINA** | | **CHIGANIZO** |
|---|---|---|---|
| | Vashiti | 1. | Mfumukazi yatsopao, mkazi wa Chihebri |
| | Estere | 2. | Malume a Estere omwe anamulera |
| | Mordekai | 3. | Mdani wa mtundu wa Ayuda |
| | Haman | 4. | Mfumukazi yonyozera ulamuliro wa mfumu, nichotsedwa |

4. Yemwe analemba Bukhu la Estere ndi ndani?
   ______________________________________________________________________
5. Kodi nkhaniyi inachitikira kuti?
   ______________________________________________________________________

(Mayankho a mafunso onsewa ali ku mapeto kwa bukhu lino)

**KUPIRIZA KUPHUNZIRA**

M'machaputala a Rute ndi Estere, ndinaonetsera kafukufuku wa makhalidwe awo. Kusanthula makhalidwe abwino a anthu a m'Chipangano Chakale kumakupatsani inu kuthekera kofuna kukhala nawo makhalidwe otero. Ndipo kusanthula makhalidwe oipa a anthu a m'Chipangano Chakale kumakupatsani kuthekera kodziwa makhalidwe omwe mukuyenera kupewa.

Kuti muonjezere chidziwitso chanu cha Bukhu la Estere, ndi kukhala nalo luso panokha losanthula makhalidwe a anthu a m'Baibulo, unikani zikhalidwe za Haman ndi Mordekai. Amuna awiri awa akusiyana kutali kwambiri m'makhalidwe awo. Werengani Bukhu la Estere ndipo muonenso chikhalidwe cha munthu wina aliyense. Lembani mu tchati chiri m'musichi zomwe mupeze:

Chikhalidwe cha Mordekai:

Ndime Chikhalidwe

____________________________________________________________

____________________________________________________________

________________________________________________________

Chikhalidwe cha Haman

Ndime Chikhalidwe

____________________________________________________________

____________________________________________________________

________________________________________________________

## CHAPUTALA 6

## UBALE WA YESU NDI AZIMAYI

### ZOLINGA

Mukamaliza phunziro mutha kukwanitsa kuchita zinthu izi:

- Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera.
- Kufotokozera momwe Yesu anachitira ndi azimayi mu utumiki wake pa dziko lapansi.
- Kuzindikira ubale wanu ndi Yesu monga mwa chifuniro chake.

### VESI LOTSOGOLERA

> **Pakuti aliyense amene adzachita chifuniro cha aAtate wanga wa kumbamba yemweyo ndiye mbale wanga ndi mlongo wanga ndi amai wanga. Mateyu 12:50**

### MAU OYAMBA

Mu chaputala chino musanthula ubale wa Yesu ndi azimayi. Mu chaputala chinacho mupitiriza kuona mozama momwe Yesu anachitira ndi azimayi mu utumiki wake.

Mu chikhalidwe cha Mulungu, muli kuphatikizana kwa makhalidwe a tate komanso mayi. Yesaya akulankhula Mau a Mulungu moonetsa umayi:

> **Kodi mkazi angaiwale mwana wache wa pabere kuti iye sangachitire chifundo mwana wombala iye? Inde awa angaiwale koma Ine sindingaiwale. Yesaya 49:15**

> **Monga munthu amene amache amtothoza mtima, momwemo ndidzatothoza mtima wanu; ndipo mudatothozedwa mtima m'Yerusalemu. Yesaya 66:13**

Yesu akuonetsera makhalidwe a mayi pamene analankhula kuti:

> **Ha, Yerusalemu, Yerusalemu, amene umapha aneneri, ndi kuwaponya miyala iwo otumidwa kwa iwe! Ine ndinafuna kangati kusonkhanitsa pamodzi ana ako, inde monga thanzi lisonkhanitssa anapiye ache m'mapiko ache koma inu simunafuna ai! Mateyu 23:37**

Chiphunzitso cha Yesu chinali chosasankha kuti azibambo kapena azimayi. Palibe pamene anapereka malangizo a azimayi okha kapena azibambo okha. Pali malangizo ochepa chabe omwe analankhula kwa ophunzira ake ongofunika azibambo (onani mwachitsanzo Mateyu 5:28, 32 ndi 23:8)

## AZIMAYI NDI KUKHALA WOPHUNZIRA WA YESU

Yesu amaphatikizapo azimayi nkuphunzitsa kwake. Pa Marko 7:10-11 analankhula za kulemekeza makolo, ndipo anabwerezabwereza mai oti "atate" ndi "amayi" kanayi m'mavesi awiri okha. Anali nako kuthekera kogwiritsa ntchito mau a Mchigriki okamba za "makolo" koma amafuna kutsindika kuti amayi ndi abambo onse akufunika ulemu wofanana.

Pokamba za kukhala wophunzira, anaphatikizapo azimayi:

> **Kodi muyesa kuti ndinaddzera kudzapatsa mtendere pa dziko lapansi Ndinena w ainu iaitu, komatukutsutsan.**
>
> **Adzatsutsana atate ndi mwana wache ndi mwana ndi atate wache; amache adzatsutsana ndi mwana wamkazi ndi mwana wamkazi ndi amache mpongozi adzatsutsana ndi mkazi wa mwana wache ndi mkaziyo ndi mpongozi wache. Luka 12:51, 53**

Ndime yina yokamba za kukhala wophunzira anatchulaponso azimayi:

> **Yesu nati, ndinena ndi inu ndithu, palibe munthu anasiya nyumba kapena abale kapena alongo kapena ami kapena atate kapena ana kapena minda chifukwa cha ine ndi chifukwa cha uthenga wabwinowo.**
>
> **Amene sadzalandira makui khumi tsopano nthawi yino, nyumba ndi abale ndi alongo ndi amai ndi ana ndi minda pamodzi ndi mazunzo ndipo nthawi irinkudza moyo wosatha.Marko 10:29-30**

Pa malo ena, Yesu akulankhula ku khwimbi la anthu, amayi ndi abale ake anabwera kuti adzamuone. Atamuuza kuti akufunidwa panja, Yesu anati:

> **Pamene iye anali chilankhulire ndi makamu onani amache ndi abale ache anaima panja nafuna kulakhulana naye.**
>
> **Ndipo munthu nati kwa iye onani amai wanu ndi abale anu aima pabwalo nafuna kulankhula nanu.**
>
> **Koma iye anayankha nati kwa iye wonenayo, ami wanga ndani? Ndi abale anga ndi ayani?**
>
> **Ndipo anatambalitsa dzanja lache pa ophunzira ache nati penyani ami wanga ndi abale anga**
>
> **Pakuti ali yense amene adzachita chifuniro cha Atate wanga wa kumwamba yemweyo ndiye mbale wanga ndi mlongo wanga ndi amai wanga. Mateyu 12:46-50**

Ndime iyi ikulankhula chinthu chofunika kwambiri tikakamba za ubale wanu ndi Yesu. Ubale wanu sukutengera kuti ndinu wam'muna kapena wamkazi, wamkulu kapena wamng'ono, wa banja kapena woti sali pa banja. Ubale wanu ukutengera pakuchita chifuniro chake cha Mulungu.

Ndipo mbali imodzi ya kuchita chifuniro cha Mulungu ndi kulandira Yesu monga Mbuye ndi Mpulumutsi wa moyo wanu popeza Mulungu…

**….safuna akaonongeke koma kuti onse afike kukulapa (2 Petro 3:9)**

## YESU ATETEZA AZIMAYI

Malo okwana awiri, Yesu anateteza azimayi. Azimayi ena atabwera ndi ana awo kwa Yesu kuti awadalitse, ophunzira anawadzudzula koma Yesu anati:

> **Koma pamene Yesu anaona anakwiya ndipo anati kwa iwo lolani tiana tidze kwa ine, musatiletse pakuti ufumu wa Mulungu uli wa totere. Marko 10:14**

Pamene Mariya wa ku Betaniya anadzodza Yesu ndi mafuta a mtengo wapatali, ophunzira ake anamdzudzula kuti akuononga. Koma Yesu ananena kuti zimene anachita Mariya zikhala zikutchulidwa kuli konse kumene Uthenga Wabwino udzalalikidwa popeza anamvetsa dongosolo la imfa ndi kuikidwa kwake m'manda ndipo anankozekeretsa ku chimenecho.

## AZIMAYI KUYENDA LIMODZI NDI YESU

Yesu sanayitane mzimayi wina aliyense kuti akhale wophunzira mwa khumi ndi awiri aja pamene amayamba utumiki wake. Kukhala ndi munthu wamkazi ngati wophunzira wake sichikanakhala chinthu choyenera popeza panali ubale wa ponda apa mpondepo. Komabe Baibulo limafotokozera za azimayi ena amene anali kuyenda ndi Yesu kukatumikira:

> **Ndipo kunali katapita kamphindi anayendayenda kumidzinda ndi kumidzi kulalikira ndi kuwawuza Uthenga wabwino wa Ufumu wa Mulungu, ndipamodzi naye khumi ndi awiriwo,**
>
> **Ndi akazi ena amene anachiritsidwa mizimu yoipa ndi nthenda zao ndiwo Mariya wonenedwa magadalene amene ziwanda zisanu ndi ziwiri zinaturuka mwa iye.**
>
> **Ndi Yohana mkazi wache wa kuza kapitao wa Herode ndi Suzana ndi ena ambiri amene anawatumikira ndi chuma chawo. Luka 8:1-3**

Anthu ena amakhulupirira kuti popeza Yesu analibe wophunzira wamkazi pa gulu lake lija, ndiye kuti mzimayi sakuyenera kutenga gawo mu utsogoleri wa mpingo. Tisaiwale kuti sanankhe Wamitundu wina aliyense kukhala wophunzira wake koma Uthenga Wabwino unafalikira kufikira kwa Amitundu ndipo takhalapo ndi atsogoleri amphamvu kumeneko. Tisayiwalenso kuti Yesu sanamange tchalitchi komwe anthu amasonkhana koma lero tiri

tamanga matchalitchi, tiri ndi azibusa okhazikika pamalo, makomiti komanso ma Sande Sukulu ndi zina zotero sitizitenga kukhala vuto.

## ULEMU WA KWA AZIMAYI

Khristu anali munthu amene amalemekeza azimayi koposa. Samawalankhula mowanyanzitsa kapena mwaukali. Ali ndi zaka khumi ndi ziwiri, Yesu anapita ku Yerusalemu ndi makolo ake ku Phwando la Pasaka. Pobwerera kunyumba, makolo ake sanamuone pa gulu la anthu opita kwao, ndipo anabweranso ku Yerusalemu kukamuyang'ana. Kenako anampeza ndi atsogoleri a chipembedzo ku kachisi. Amayi ake atamudzudzula, anayankha pongofotokozera mwaulemu, basi natengana nawo ulendo wopita kwao ndipo anakhala womvera makolo ake (Luka 2).

Pali malo ena omwe anthu atha kunena kuti Yesu sanalankhule mayi ake mwaulemu. Uku kunali ku ukwati wa ku Kana. Eni ukwati atazindikira kuti vinyo watha, makolo a Yesu anamdziwitsa ndipo Iye anayankha nati:

> **Ndipo Yesu yembwyo ndi akumphunzir ache anaitanidwa ku ukwatiwo. Yohane 2:4**

Izi sizikutanthauza kuti sanalemekeze maganizo a mayi ake kuti sachitapo kanthu ayi. Mau oti "mkazi iwe" sakusonyeza mwano konse. Mu nthawi yake Yesu anachita zimene mayi ake ananena nasandusa madzi kukhala vinyo mozizwitsa. Mariya sanakhumudwe ndi yankho la Yesu ndipo anauza anyamata ake kuti:

Chiri chonse akakuuzani kuti muchite, chitani (Yohane 2:5)

Mai ake a Yakobo ndi Yohane atabwera kwa Yesu ndi pempho lodzikonda, kupempha Yesu kuti akalole ana ake kukhala pafupi ndi Iye mu Ufumu wake – wina kumanja wina kumanzere, Yesu sanayankhe mwachipongwe. Iye anati:

> **Pomwepo anadza kwa iye amache ana a zebedayo ndi ana ache omwe anamgwadira ndi kumpempha kanthu. Mateyu 20:20-23**

Werengani Mateyu 15:21-28 pomwe mzimayi wamitundu anapempha kuti mwana wake alandire machiritso, Yesu anagwiritsa ntchito mau oti "galu." Mau awa sakusonyesa chipongwe popeza ndi mau omwe anthu ankagwiritsa ntchito paliponse ponena za Amitundu. Kumapeto kwa nkhaniyi, Yesu anayamikira mzimayi koposa chifukwa cha chikhulupiriro chake.

Pali malo atatu m'Baibulo omwe tikuona Yesu akutumikira kwa akazi achigololo. Wonani ndime izi:

a. John 8:2-11 Mkazi wogwidwa ndi chigololo
b. Luka 7:38-39 Mkazi wachigololo akusambitsa mapazi a Yesu.
c. Yohane 4:5-30 Mkazi pa chitsime cha Yakobo

Mu nkhani zonsezi, Yesu akuonetsera ulemu woposa, chikondi ndi mtima wokhulululukira.

Nkhani ya Yesu ndi mkazi mkazi wa ku Samariya pa chitsime ndiyochititsa chidwi tikamasanthula za momwe Yesu anakhalira ndi azimayi. Asamariya anali adani a Ayuda ndipo amatengedwa kukhala osaphunzira ndi amwano. Kuonjezera apo, mkaziyu anali wachigololo.

Koma Yesu anasankha mkazi uyu molingana ndi Mau a Mulungu, kudziulula yekha koyamba kuti Iye ndi Mesiya wolonjezedwa. Anamtenga kukhala munthu amene amaoneka kuti akumvetsa zinthu zauzimu mwamsanga. Nthawi yomweyo anakhala mlaliki nathamangira ku mzinda kukaitanira anthu kwa Khristu. Zotsatira zake zinali zakuti:

**Ndipo ambiri oposa anakhulupira chifukwa cha mau ache.**

> **Ndipo ananena kwa mkazi kuti Tsopano sitikhulupira chifukwa cha kulakhula kwawo pakuti tamba tokha ndipo tidziwa kuti mphulumutsi wa dziko lapansi ndi Iyeyu ndithu. Yohane 4:41-42**

Nthawi yomwe Yesu anapita kukayendera Marita ndi Mariya, Marita anali wokwiya kuti Mariya samamthandiza ntchito namangokhala pa mapazi a Yesu. Ndipo Yesu anamyankha kuti:

> **Koma Ambuye anayankha nati kwa iye Marita, Marita uda nkhawa nubvutika ndi zinthu zambiri. Luka 10:41**

Mkazi wamasiye atayika tindalama tiwiri m'mbale ya chopereka ku kachisi, Yesu anayamikira koposa pomwepo za kupereka kwakukuru kotero. Anati:

> **Ndipo anaitana ophunzira ache nati kwa iwo ndithu ndinena ndi inu mkazi wamasiye amene waumphawi anaponya zambiri koposa onse akuponya mosungiramo.**
>
> **Pakuti anaponyamo onse mwa zochuruka zao koma iye anaponya mwa kusowa kwa zonse anali nazo inde moyo wache onse. Marko 12:43-44**

Mabuku a Uthenga Wabwino amaonetsa kuti Yesu amawatenga azimayi monga anthu oti atha kulankhula nawo, okhala ndi kuthekera komvetsa zinthu zakuya zauzimu, okhala ndi chikhulupiriro chachikulu, komanso opereka chitsano chabwino cha kutumikira modzipereka nsembe.

## YESU AMACHITIRA CHIFUNDO AZIMAYI

Chikhalidwe chapadera cha Yesu pa azimayi tingati chinali chifundo. Pamene aukitsa mwana wa mkazi wamasiye ku Naini, anaonetsa kuti anachita ichi mwachifundo chake pa mkaziyu:

**Ndipo pamene Ambuye anamuona anagwidwa ndi chifundo chifukwa cha iye nanena naye Usalire. Luka 7:13**

Chinali chifundo chake pa azimayi chimene chinadzutsa mkwiyo pa iwo amene amapemphera m'makwalala ndi kuba nyumba za amasiye:

**Chenjerani nao alembi amene afuna kuyendayenda obvala minjiro nkonda kulankhulidwa m'misika ndi mipando yaulemu m'sunagoge ndi malo awulelmu pamapwando**

**Amene aononga nyumba za akazi amasiye ndipo monga achita mapemphero atali amenewo adzalandira kulanga koposa. Luka 20:46-47**

Atadyetsa anthu mazana mazana, kuphatikizapo azimayi, ndi chifukwa chakuti anali ndi chifundo pa iwo. Werengani za nkhani imeneyi pa Marko 6 (makamaka vesi 34) ndi Marko 8 (makamaka vesi 2).

Pamene Yesu amalankhula za kuonongeka kwa Yerusalemu mtsogolo, anaphatikizapo chenjezo la chifundo iri:

**Koma Tsoka iwo akukhala ndi pakati ndi akuyamwitsa masiku awo ndipo pempherani kuti kusakhale m'nyengo yachisanu**

**Pakuti masiku aja padzakhala chisautso chonga sichinakhala chinzache kuyambira chiyambi cha chilengedwe chimene Mulungu anachilenga ndi kufikira tsopano ndipo sichidzalaponso ndipo sichidzakhalanso thawi zonse. Marko 13:17-18**

Yesu ali panjira yonka ku Gologota atanyamula mtanda, panali azimayi ambiri omwe anazunguliridwa ndi asilikari komanso andende. Azimayiwa amalirira Yesu. Iye anaoneka wokhuzika kwambiri ndi iwo osati Iye mwini. Iye anati:

**Koma Yesu anawapotolokera nati ana akazi inu a Yerusalemu musandilirire ine, koma mudzilirire nokha ndi ana anu.**

**Chifukwa taonani masiku alinkudza pamene adzati odala ali owuma ndi mimba yosabala ndi mawere osayamwitsa. Luka 23:28-29**

Kumapeto kwa utumiki wake wa pano pa dziko lapansi, pakatikati pa mazunzo ake, chifundo chake cha pa azimayi sichinazilare.

## KUDZIYESA NOKHA

1. Ubale wanu ndi Yesu wagonera pa: ______________________________________________
2. Lembani Vesi Lotsogolera osaonera ______________________________________________
3. Werengani maina omwe ali mu gawo loyamba. Sankhani chiganizo mu gawo lachiwiri chomwe chiri ndi mau omwe analankhula kwa munthu kapena gulu la m'gawo loyamba. Ikani nambala ya chiganizo ku mayambiliro a dzina loyenerera:

| | DZINA | | MAU OLANKHULIDWA NDI YESU |
|---|---|---|---|
| | Azimayi okhala ndi ana | 1. | Ichi chidzanenedwa pokumbukira za iye |
| | Mariya, make wa Yesu | 2. | Yesu anadziulula kwa iye kuti ndi Mesiya |
| | Mkazi wa chigololo wotsuka mapazi a Yesu | 3. | "Lolani ana adze kwa Ine" |
| | Mkazi wamitundu wofuna machiritso kwa Yesu | 4. | Yesu anamuyamikira popereka |
| | Marita | 5. | Mariya wasankha dera lokoma |
| | Mkazi wamasiye | 6. | "Chikhulupiriro chako n'chachikulu" |
| | Mkazi wa pachitsime | 7. | "Mkazi, ndili nawe chiyani ine" |

(Mayankho a mafunso awa ali ku mapeto a bukhu lino)

**KUPITIRIZA KUPHUNZIRA**

Kuti mupitirize kuphunzira za ubale wa Yesu ndi azimayi, santhulani ndime izi zomwe zikuonetsera momwe Yesu analankhulira ndi azimayi.

| | Mateyu | Marko | Luka | Yohane |
|---|---|---|---|---|
| **MAI AKE** | | | | |
| Ali mwana | | | 2:41-50 | |
| Ku kana | | | | 2:1-11 |
| Pa mtanda | | | | 19:25-28 |
| **MARITA** | | | | |
| Kutumikira | | | 10:38-42 | |
| Kuukitsidwa kwa Lazaro | | | | 11:1-44 |
| **MARIYA WA BETANIYA** | 26:6-13 | 14:3-9 | | 12:1-9 |
| **MARIYA MAGADALA** | 28:9-10 | | 8:2 | 14:14-18 |
| **MKAZI WA KU SAMARIYA** | | | | 4:1-42 |
| **MKAZI WA CHIGOLOLO** | | | | 8:1-11 |
| **WOCHIMWA** | | | 7:36-50 | |
| **MKAZI WA KU FONIKE** | 15:22-28 | 7:24-30 | | |
| **MWANA WA JAIRO** | | | | |
| **MKAZI WODWALA** | | | | |
| **ZAKA 12** | 9:20-25 | 5:25-42 | | 8:43-56 |

| | | | | |
|---|---|---|---|---|
| **MPONGOZI WA PETURO** | 8:14-15 | 1:30-31 | | 4:38-39 |
| **MWANA WA MKAZI WASIYE** | | 7:11-15 | | |
| **MKAZI WA MSANA** | | | 13:11-13 | |

# CHAPUTALA 7

## UTUMIKI WA YESU KWA AZIMAYI

**Zolinga:**

Mukamaliza chaputalachi muzikwanitsa kuchita izi;

- Kulemba vesi yotsogolera.
- Kukambirana mafanizo a Yesu okhudza azimayi pa nkhani ya anthu, mavuto ndi ndondomeko.
- Kugwiritsa ntchito ma fanizo pa utumiki ndi moyo wanu.
- Kukambirana zozizwa za Yesu zokhudzana ndi azimayi pa anthu, mavuto ndi machitidwe awo.

**Vesi Lotsogolera**

> **Koma palinso zina zambiri zimene Yesu anazichita, zoti zikadalembedwa zonse phe, ndilingalira kuti dziko lapansi silikadakhala nao malo a mabuku amene akadalembadwa. Yohane 21:25**

### MAU OYAMBA

M'chaputala chapitachi, tinaphunzira za ubale pakati pa Yesu ndi azimayi. Yesu anali ndi zinthu zofunika kwa azimayi ndi zina zokhudza azimayi. Anawaphuzitsa pa mitu yosangalatsa ndipo anawaikanso m'mafanizo ena. Anawatumikiranso mnjira zodabwitsa pamene anali padziko lapansi. Chaputalachi chikuyang'ana mbali ya utumiki wa Yesu kwa azimyi.

### MAFANIZO A YESU

Mafanizo ndi njira yophunzitsira imene Yesu anaigwiritsa ntchito mu utumiki wake ali padziko lapansi. Fanizo ndi "Nkhani ya padziko yokhala ndi tanthawuzo la kumwamba." Fanizo limabweretsa chowonadi mwankhani imene omvera atha kuyimvetsetsa mosavuta.

Yesu anagwiritsa ntchito mafanizo anayi kuti awonetse chowonadi chauzimu. Musanapitirire ndi phunziroli werengani fanizo lirilonse m'Baibulo. Mukuyenera kuwona fanizo lirilonse pogwiritsa ntchito mbali izi:

> **Munthu**: Amene fanizo likumukhudza.

**Vuto:** Nyengo imene anthu akumana nayo m'fanizo (Nkhani ya padziko)

**Mfundo**: Chowonadi chofunika chimene Yesu amaphuzitsa. (Tanthauzo la Kumwamba)

Tsopano werengani mafanizo:

**NDALAMA YOTAIKA (LUKA 15: 8-10)**

**Munthu:** Mai amene anali ndi ndalama za siliva khumi.

**Vuto:** Ndalama imodzi inataika

**Mfundo:** Yesu anagwiritsa ntchito fanizoli ndi mafanizo ena awiri kufotokozera mfundo ziwiri zowonadi komanso zofanana. Werengani fanizo la nkhosa yotaika imene ikutsatira fanizo la ndalama yotaika (Luka 15: 3-7). Kenako werengani fanizo la mwana wolowerera imene ikutsatira (Luka 15: 11-13).

Cholinga cha Yesu popereka tsatanetsatane wa mafanizo ndi kuyankha zimene afalisi amanena kuti iye akulandira anthu ochimwa ndikumadya nawo zinali zoletsedwa kwa m'yuda monga mwa chikhalidwe (Onani ndime 1-2)

Yesu anafotokozera ubwino ofikira miyoyo yotaika. Zinali zofunika kulandira ochimwa ndikumalumikizana nawo ndicholinga chowafikira ndi uthenga wa chipulumutso. Anagwiritsa ntchito fanizo la nkhosa yotaika, ndalama yotaika, ndi mwana wolowerera kufotokozera choonadi ichi. Katundu, ndalama, ndi banja zinali zinthu zimene afalisi amazilemekeza ndipo anakwanitsa kulumikizana nawo ndi mafotokozedwe amenewa.

Yesu anagwiritsa ntchito chitsanzo cha mzimayi wofuna ndalama yotaika komanso kuyang'ana nkhosa yotaika. Azimai ali ndi ntchito yawo pofikira miyoyo yotaika. Monga mzimai m'fanizoli, tikuyenera kuwalitsa zowunikira za uzimu ndikufunafuna otaika. Pamakhala chimwemwe pamalo pamene angelo ali, pamene tabwereta kwa Yesu amene anataika. Kodi munakhala mukufunafuna otaika?

**MAYI WAMASIYE WOKAKAMIRA: Luka 18:1-8**

**Munthu:** Mzimai wamasiye amene amafuna chilungamo kwa oweruza osalungama amene samaopa Mulungu kapena munthu.

**Vuto:** Amafuna chilungamo kwa mdani wake. Fanizo silikuwonetsa kuti mdani wake anali ndani kapena kuti choipa chimene anachita ndi chani. Oweruza oipa sakanachita chirichonse kwa mzimayi wamasiye koma chifukwa anakakamirabe kupita kwa iye, anaganiza kuweruza mlandu wake momukomera kuti asamuvutitsenso.

**Mfundo:** Yesu anafotokozera kuti kukakamira kumabweretsa yankho kuchokera kwa Mulungu. Yesu anapereka chitsanzo ichi kuti alimbikitse ophunzira kuti asasiye kupephera (ndime 1). Ngati oweruza osalungama anayankha, Mulungu olungama amachitapo kanthu pakukamira kwa anthu ndipo amapereka yankho ku pempho lawo:

**Pemphero la munthu wolungama likhoza kwakukulu m'machitidwe ake (Yakobo 5:16b)**

**ANAMWALI KHUMI Mateyu 25:1-13**

**Munthu:** Azimayi asanu ochenjera, azimayi asanu opusa, ndi munthu kapena kagulu ka anthu kamene kakuchejeza zakubwera kwa mkwati.

**Vuto**: Azimayi khumi akudikirira kubwera kwa gulu loperekeza mkwati. Azimayi asanu anali ochenjera ndipo anabweretsa zosungira mafuta a nyali zao. Azimai asanu anali opusa ndipo sanabweretsa mafuta owonjezera.

Akazi onse anagona pamene amadikirira. Mwadzidzi, mfuwu unaveka owonetsa kuti mkwati akubwera ndipo akazi onse anadzuka nayatsa nyali zao. Akazi opusa anazindikira kuti mafuta awo anagwiritsidwa ntchito ndipo nyali zao zinazima. Anayesera kubwereka mafuta kwa akazi ochenjera amene anali ndi mafuta koma anakanizidwa.

Pamen akazi opusa anapita kukagula mafuta, mkwati anafika ndipo akazi ochenjera analowa ku mphwando la ukwati kuti akadye naye. Pamene akazi opusa anabwera ndi mafuta, chitseko chinali chitatsekedwa ndipo sakanatha kulowa chifukwa anali atachedwa. Anadikira kwambiri kuti adzikozekeretse okha.

**Mfundo:** Fanizo iri linaperekedwa ndi Yesu pamene amakambirana ndi akuphuzira ake zokhudzana ndi nthawi yakutha kwa dziko. Werengani kumayambiriro kwa kumbirana pa Mateyu 24.

Nkhani ikupitirira pa Chaputala 25. Yesu anawawuza akuphuzira ake kuti masiku otsiriza moyo wauzimu udzafanizidwa ndi fanizo la anamwali. Anthu ena adzakhala okonzeka kukumana ndi Ambuye koma adzakhala akugona koma ali atcheru ndi kubweranso kwake. Awa ndiwo anamwali ochenjera.

Ngakhale kuti anapulumutsidwa koma sakuchita kalikonse pochenjeza anthu amene awazungulura zakubweranso kwa mkwati pamene akukumana ndi chitsitsimutso ndikukonzekera kukumana naye.

Anamwali opusa akufotokoza za gulu lina la anamwali amene akudziwa za kubweranso kwa Yesu. Anakonzekera. Anazidikira mochedwa kuti adzaze zotengera zao za uzimu ndipo sakupita ndi Yesu pakubweranso kwake.

Amayesetsa kuchita zinthu podalira ndi kukhazikika pa makozekeredwe anamwali ochenjera, koma izi ndi zosatheka. Sizingatheke kulowa mufumu wa Mulungu pokhazikika pa chidziwitso cha wina. Mukuyenera pa inu nokha kukonzekera kukumana naye.

Pali gulu lina lachitatu mufanizoli. Ngakhale kuti onse anagona, anamwali opusa ndi ochenjera, koma wina anali watcheru kupereka mfuwu kuti nkwati akubwera. Padzakhala gulu la anthu a Mulungu amene adzakhala atcheru ndikubweranso kwake posachedwapa. Odzuka muuzimu ndi atcheru pakubweranso kwake. Adzakhala akudziwitsa anthu a Mulungu amene akugona amene sakudziwa kuti yatsala nthawi yochepa kuti Yesu abwere.

Kodi inu muli mbali iti? Kodi ndinu okonzeka muzimu kukumana ndi ambuye koma osakhala atcheru kuti akubweranso posachedwapa? Kodi mukugona m'malo mopereka mfuwu kwa ena kuti akonzeke zakubweranso kwake?

Kodi mulingati anamwali opusa? Mwina musanakonzeke muzimu kuti mukumane ndi Yesu. Mulibe mafuta munzotengera zanu. Mwauzimu mukugona ndipo mulibe kanthu. Imvani mfuwu wakubweranso kwake posachedwapa ndipo konzekerani tsopano, nthawi isanathe.

Kodi muli mbali imodzi ya guli lachitatu limene silinatchulidwe dzina, amena anali atcheru kukonzekera kubweranso kwa mkwati ndipo amachenjeza ena kuti akumane naye? Kodi imu muli mbali iti mwa magulu atatuwa.

**MKAZI AMENE ANALI NDI CHOTUPITSA: Mateyu 13:33; Luka 13:20-21**

**Munthu:** Mkazi amene sanatchulidwe dzina.

**Vuto:** Akukoza nkate ndipo akugwiritsa ntchito pang'ono, chotupitsa mikate pophika miyeso itatu ya chakudya. Muyeso umodzi unali ngati chimodzi ndi theka lachakudya.

**Mfundo:** Fanizo iri ndi limodzi mwa mafanizo ambiri a Yesu amene anawagwiritsa ntchito pofotokozera chilungamo chokhudzana ndi ufumu wake otchedwa "Ufumu wa Mulungu."

Nthawi zambiri m'Baibulo chotipita chimagwiritsidwa ntchito ngati chitsanzo cha choipa. Chimagwiritsidwa ntchito kuwonetsa kuti choipa chochepa chimadzichulukitsa ndikukhala chachikulu monga chotupitsa chimafalikira ntanda onse mufanizoli. Komabe, chotupitsa chimagwiritsidwanso kufotokozera kuti mufumu wa Mulungu, chochitika chaching'ono chikhoza kuchuluka ndikukhala nazo zotsatira zambiri.

Monga chotupitsa chaching'ono chimafalikira kuchakudya chonse pamene mtanda ukukonzedwa pophika mkate, chomwechonso chotupitsa cha mau a Mulungu chimadzichulukitsa. Iyi ndi mfundo imene imatchulidwa kuti "chotupitsa monga kufalitsa". (Harvestime International Institute) imapereka maphuziro pa mutu umenewu oima kwambiri pa kufalitsa kumene kumadzichulukitsa kokha kudzera m'mawu.

Fanizo likufotokozera mfundo zambiri zofunika. Choyamba, muthakukhala ndi chotupitsa (mau) ndi nyali imene ikufunika chotupitsa (dziko), koma palibe chingachitike pokhapokhapo (mau) akhazikika m'mitima ya anthu adziko (nyali).

Chachiwiri, munthu ndi chipangizo chimene Mulungu amachigwiritsa ntchito poika chotupitsa mu nyali. Mulungu amagwiritsa nchito anthu ngati iweyo kuti afalitse mawu kudziko lapansi.

Chachitatu, zinthu zazing'ongo zimachuluka kukhala zazikuru m'chuma cha Ufumu wa Mulungu. Kuyesera kwakung'ono pa chotupitsa cha kufalitsa kumapitirira ndi kudzichulukitsa kokha pa nyali yonse ya dziko. Monga m'neneri Zakaliya anati:

> **Pakuti wapeputsa tsiku la tithu tating'ono ndani? Pakuti adzakondwera, asanu ndi awiri awa nadzaona chingwe cholungamitsira chiri m'dzanja la Zerubabele, ndiwo maso a Yehova; ayendayenda mwa dziko lonse. (Zakaliya 4:10)**

## KUMANGIRIRA MAFANIZO

Yesu anagwiritsa ntchito azimayi kufotokozera chowondadi china mufumu wake. Mkazi wamasiye akufotokozera ubwino wokakamira popephera kuti zinthu zidzaikidwe m'chimake mufumu, adani adzagonja, ndi anthu a Mulungu adzabwezeredwa. Azimai ndi chotupitsa akufotokozera ubwino ochitapo kanthu mufumu wa Mulungu. Mukuyenera kufesa chotupitsa cha mau mu nyali ya dziko.

Koma kufesa sichokwanira. Mukuyeneranso kuphunzira kukolola. Izi zinafotokozeredwa mfanizo la mzimayi wa ndalama yotaika. Anayang'ana ndalamayo mpaka anayipeza. Simukuyenera kufesa chabe chotupitsa cha mau, koma mukuyeneranso kukolola ndikufikira azimayi ndi abambo otayika.

Chomaliza, fanizo la anamwali lawonetsa kuti m'masiku akutha kwa nthawi ya pansi pano, ena adzakhala okonzeka kulowa Ufumu wa Mulungu ndipo ena ayi. Mtundu wa chinthuzithunzi cha azimayi amene Yesu akuwonetsa m'mafanizowa ndi cha iwo amene ndi amachitachita mufumu wa Mulungu, amene adzapirira m'mapemphero, nafesa mbewu ya mau, nakolola otayika, ndikupereka mfuwu kuchenjeza amene akugona muuzimu.

## ZODABWITSA ZA YESU

Yesu anachita zodabwitsa zambiri zimene zinawakhudza azimayi nthawi ya Utumiki wake pansi pano. Mulembe mfundo zanu pa phuziloli. Onaninso mayalidwe a zinthu m'mafanizowa, ndipo tsatirani izi mukamaphuzira zodabwitsa za Yesu zokhudza akazi. Lembani phuziro lanu poyang'ana izi:

**Anthu:** Amene chodabwitsa chinawakhudza.

**Vuto:** Chofunika chimene Yesu anakumana nacho.

**Machitidwe:** Zimene iye anapanga poyang’ana chofunikacho. Chodabwitsa chake chinali chani ndipo anachichita bwanji? Nanga zotsatira za chodabwitsachi ndi chani?

**APONGOZI AKE A PETRO:**

Mateyu 8:1-15; Mark 1:30-31; Luke 4:38-39.

**Anthu:**

**Vuto:**

**Machitidwe:**

**Vuto:**

Nkazi wa nthenda ya magazi:

Mateyu 9:20-22; Marko 5:25-29; Luka 8:43-48.

**Anthu:**

**Machitidwe:**

Mwana wa mzimayi wa ku Kannani:

Mateyu 15:21-28; Marko 7:24-30.

**Anthu:**

**Vuto:**

**Machitidwe:**

Luka 13:11-13.

**Anthu:**

**Mavuto:**

**Machitidwe:**

Mwana wa Yayilo:

Mateyu 9:18-19, 23-25; Marko 5:22,24, 38-42; Luka 8:41-42, 49-56.
76 **Anthu:**

**Vuto:**

**Machitidw:**

Mwana wankazi wa masiye wa ku Nine:

Luka7:11-15.

**Anthu:**

**Vuto:**

**Machitidwe:**

Nchimwene wa Mariya ndi Marita:

Yohane 11:1-44. **Anthu:**

**Mavuto**

**Machitidwe:**

## MAWU OTSIRIZA PA ZODABWITSA

Kukhudzika ndi chizindikiro chachikulu cha Yesu chimene chimawonekera mzodabwitsa zonse zimene iye anazipanga zokhukhudza azimayi onse. Yesu anawonetsa kukhudzika posatengera kuti nthenda inali ya kanthawi kochepa ngati ya mpongozi wake wa Petro kapena nthenda yotenga nthawi yaitali monga nkazi wa thenda ya magazi ndi mzimai wamsana wopeteka.

Ndizosangalatsa kuti zodabwitsa zake zimatsatira ndondomeko. Choyamba anathana ndi nthenda yosakhalitsa ngati malungo. Kenako anathana ndi nthenda yokhalitsa monga nkhazi wa nthenda ya mwazi, ndi mkazi wa msana wopeteka. Ngakhale kuwukitsidwa kwa wakufa kunali ndi ndondomekonso. Choyamba anadzutsa mwana wamamuna wa nkhazi wa masiye ndi mwana wankazi wa Yairo, onsewa panali patapita nthawi yochepa atafa. Kenako anadzutsa Lazaro amene anakhala m'manda masiku ambiri.

Yesu andadzutsa mwana wankazi wa Yairo munyumba atangofa. Mwana wa mwamuna wa mzimayi wamasiye anadzuka kwakufa panjira ya kumanda. Lazaro anadzutsidwa m'manda atakhala m'menemo masiku ambiri. Sizimatengera kuti ndi liti Yesu walowa mumvuto la moyo wanu. Mphavu yake ndi yokwanira pa mulingo uliwonse wa chofuna chanu.

## MAU A YESU KWA AZIMAYI KOMANSO OKHUZA AZIMAYI

Kuwonjezera pa mafanizo ndi zodabwitsa zokhudza akazi, Yesu anali ndizonena pa mitu yokhudzana ndi akazi. Izi ndikuphatikiza zida pa nkhani ya ukwati, chimasomaso, ana, ndi zina. Yesu analankhulanso mwachinduji kwa akazi nthawi zambiri.

M'gawo la "kupitiliza kuphunzira" m'chaputalachi mupeza ndandanda wa mitu yokhudza azimayi imene Yesu analankhulapo. Magawo anapangidwa kuti amalizitse cholinga chimodzi mwa zolinga zazikuru za Harvestime Institute, izi ndikupitiliza kuphunzira kwa Mau a Mulungu. Tikufuna inu kuti mukhale nako kuthekera kounika chowonadi cha Mau a painu nokha. Gawo ili limakupatsani kuthekera kochita izi pamene mukupitiliza kuphunzira utumiki wa Yesu kwa azimai.

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani ndime yotsogolera osaonera.

________________________________________________________________________________

________________________________________________________________________________

________________________________________________________________________________

2. Lembani m'ndandanda wa mafanizo osachepera anayi amene Yesu ananena okhudza azimai.

(1)______________________________________________________________________

(2)______________________________________________________________________

(3)______________________________________________________________________

(4)______________________________________________________________________

3. Lembani m'ndandanda wa zodabwitsa zosachepera zinayi zimene Yesu anachita zokhudza azimayi

(1)______________________________________________________________________

(2)______________________________________________________________________

(3)______________________________________________________________________

(4)______________________________________________________________________

"Mayankho amafusowa ali machaputala chomalizira kumapeto kwa bukuli"

## KUPITILIZA KUPHUNZIRA

Yesu analakhula zambiri pa mitu ina yokhudza azimayi monga ukwati, kutha kwa banja, ndi ana. Kuti chidziwitso chanu chichuluke pa utumiki kwa azimayi komanso utumiki wake pankhani yokudza azimayi, fufuzani mau a Yesu pa….

**Ukwati**

Mateyu 19:4-6; 22:30

Marko 10:6-9; 12:25

Luka 20:34-35

**Ana:**

Mateyu 9:14; 18:3-5, 6, 10, 14; 21:16

Marko 9:37, 42; 10:14-15;

Luka 9:48; 18:17

**Kutha kwa ukwati:**

Mateyu 5: 27-28; 31-32; 15:19; 19:8-9; 11-12; 17-18

Marko 7:21-22; 10:3, 5,11-12, 19

Luka 16:18; 18:20

**Kukumbutsa azimayi:**

Mateyu 5:28; 9:20, 22; 11:11; 13:33; 14:21; 15:38; 19:8; 22; 24:41; 26; 27:55; 28:5

Marko 5,7, 10:12; 12:22; 14:3; 15:40,41

Luka 1:28,42; 4:26-27; 7:8; 8:2,43,47; 10:38; 11:27; 13:11,12,16,21; 15:8; 17:27,35;

20:32; 22:57; 23:27, 49, 55; 24:10, 22,24

Yohane 2:4; 4:7,9,11,15,17,19,20,21,25,27,28,39,42; 8:3,4,9,10; 16:21; 19:26; 20:13,15

## CHAPUTALA 8

## AZIMAYI M'BUKU LA MACHITIDWE ATUMWI

**Zolinga:**

Mukamaliza phunziro iri muzikwanitsa:

1. Kulemba Vesi Lotsogolera osaonera.
2. Kupeza utumiki wa azimayi mumpingo woyambirira.
3. Kupitirira kuphuzira pa mutu wa azimayi m'buku la machitidwe.

**Vesi Lotsogolera:**

> **Ndiponso pa akapolo anga ndi pa adzakazi anga m'masiku awa ndidzathira cha Mzimu wanga; ndipo adzanenera (Machitidwe 2:18)**

### MAU OYAMBA

M'chaputalachi muphunzira za azimayi m'buku la Machitidwe. Popeza bukuli limanena za okhulupirira oyamba amene amaika zinthu m'malo mwake mumpingo, phunziroli lipereka chidziwitso mbali ndi utumiki wa azimai mu mpingo oyamba.

Kuvetsetsa mbali ya azimayi mu mpingo oyamba ndikofunika chifukwa kumayala maziko a utumiki wa azimayi mumpingo walero. Muthandizidwa kuzindikira mbali ya utumiki wa Mulungu kwa inu mu mpingo.

### MALO AMENE ZIMAPEZEKA

Pali malo osiyanasiyana amene azimayi amapezeka m'buku la machitidwe. Mavesi asanu ndi imodzi akutanthawuza za azimayi odziwika amene akukhudzidwa ndi phunziro la mpingo oyamba.

-Mwana wamkazi wa Farao. Machitidwe 7:21

-Kandake amene mwa utumiki wake eunuch anatembenuka mtima kudzera mwa umboni wa Filipo: Machitidwe 8:27

-Drusila, mkazi wa Mfumu Felike: Machitidwe 24:24

-Bemike, mchemwali wa Mfumu Agripa: Machitidwe 25:23

-Kamulungu kakakazi Diana, opembedzedwa ngati make wa milungu ndi anthu, amene tchalitchi chake chinali kwa Aifeso, chimodzi mwa zodabwitsa zokwanira zisanu ndi chimodzi padziko lapansi. Machitidwe 19:27.

**-**Mchemwali wake wa Paulo. Machitidwe 23:16

Malo ena amene amanena azimayi amayikidwa pansi pa mutu waukulu umene umawonetsa mbali nd utumiki wao mu mpingo.

**CHIWERENGERO CHA ANTHU MU TCHALITCHI**

M'malo ambiri amene uthenga wabwino unalalikidwa, azimayi (Ayuda ndi Amitundu) amatchulidwa kukhala ena mwa amene anakhulupirira. Ku Yerusalemu, anthu ambiri, akazi ndi abambo omwe anakhulupirira. (Machitidwe 5:14: Ku samaliya, amuna ndi akazi anakhulupiira chifukwa cha kulalikidwa uthenga kwa Filipo (Machitidwe 8:12). Ku Yopa, Dorika ndi akazi ena anali ma membala a mpingo woyamba (Machitidwe 9: 36-43). Ku Lustra kumakhala mai ake a Timoteo Eunice ndi agogo ake akazi amene anali okhulupiriranso (Machitidwe 16:1).

Ku Filipo, Lydia anakhala mkhristu oyamba  ku Ulaya ndipo analiponso azimayi ena amene sanatchulidwe maina koma anali mbali imodzi ya mpingo kumeneko (Machitidwe 16:13-15).

Ku Atesalonika ndi Bereya akazi ambiri amafumu anakhulupirira (Machitidwe 17:4, 12). Nambala yaikulu ya azimayi okhulupirira anatchulidwa ku Makedonia. Ngakhale ku Atene kumene ochepa anachitapo kanthu potsatira kulalikira kwa Uthenga Wabwino ndi Paulo, mkazi otchulidwa Damarisi ndi ena anakhulupirira (Machitidwe 17:34).

Akazi awa sanali anthu wamba chabe mu mpingo. Anali okhulupiriradi Uthenga Wabwino ndipo anali obatizidwa mu mpingo.

> **Koma pamene anakhulupirira Filipo wakulalikira Uthenga Wabwinowu Ufumu wa Mulungu ndi dzina la Yesu Khristu, anabatizidwa, amuna ndi akazi. (Machitidwe 8:12)**

**OPEMBEDZERA**

Akazi mu mpingo woyamba wa Mulungu anali opembedzera. Mariya, amayi ake a Yesu, anabwera pamodzi ndi abambo amene amapemphera kudikirira kubwera kwa Mzimu Woyera;

> **Iwo onse analikukangalika m'kupemphera, pamodzi ndi akazi, ndi Mariya, amache wa Yesu, ndi abale ache omwe. (Machitidwe 1:14)**

Petro ataponyedwa m'ndende ndi Herode, okhulupirira amapemphera kunyumba kwa Maria, mai ake a Yohane Marko. Rhoda, m'modzi mwa akazi amene amapemphera, anakumana ndi Petro

pa chitseko m'ngelo wa Mulungu atawamupulumutsa ku ndende nanyamula uthenga wa chipambano kwa ena msonkhano wa mapemphero (Machitidwe 12:12-16)

M'zinda wa Filipo, gulu la azimai linakumana mbali mwa mtsinje kuti apemphere.

> **Tsiku la Sabata tinaturuka kumudzi kunka ku mbali ya mtsinje, kumene tinaganizira kuti amapempherako: ndipo tinakhala pansi ndi kulankhula ndi akazi amene adasonkhana,(Machitidwe 16:13)**

Mau akuti (sanapange) atanthawuza kuti linali khalidwe lao azimai kukumana pamenepo kuti apemphere.

## OLANDIRA MZIMU WOYERA

Machitidwe 2:1, Luka akulemba kuti "anali" onse a mtima umodzi pa malo amodzi. Awa "onse" anali anthu omwewo amene atchulidwa m'chaputala 1:14-15 amene amadikirira kubwera kwa mzimu woyera. Kutanthawuza kuti pamene Mzimu Woyera anabwera pa "onse" kuphatikizapo akazi. Ngati owonerera anafunsa kuti chikuchitika ndi chani, Petro anafotokoza za kubwera kwa Mzimu woyera potsindika uneneri wa Yoweli. Zinatsimikikika kuti mphamvu ya Mulungu itha kuthilidwa pa akazinso:

> **Pakuti awa sanaledzera monga muyesa inu; pakuti ndi ora lachitatu lokha la tsiku (Machitidwe 2:15:18)**

Zaka mazana Mzimu Woyera asanafike, Mulungu anaphatikizirapo akazi powonetsera mphamvu yake.

## ANENERI AKAZI

Machitidwe analemba za m'mene akazi anakwaniritsira uneneri wa Yoweli:

> **Ndipo atawalankhula iwo, anawafotokozera chidzimodzi chimodzi zimene Mulungu anachita kwa amitundu mwa utumiki wache. (Machitidwe 21:9)**

Chifukwa cha nkhani iyi, uneneri operekedwa ndi Yoweli, ndi zimphuzitso zina za Paulo zimene mudzaziphuzilabe mphuziroli, ndibwino kuti muvetsetse tanthawuzo la mau akuti "uneneri". Mabuku ofotokozera Baibulo monga Konkodansi (wamkulu ndi wamng'ono), ndi Vine akupereka matanthawuzo awa:

-Kulankhula molimbikitsidwa.

-Kuwulula chifuniro, maganizo, upangiri ndi njira za Mulungu.

-Kufotokozera bwino pagulu.

Mau akuti “uneneri” amatanthawuzanso kuphunzitsa kapena kulalikira molimbikitsidwa ndi Mulungu komanso pogwiritsa ntchito Mphatso yakunenera, imodzi mwa Mphatso ya Mzimu woyera. Mudzaphunzirabe za izi mukamaphunzira za ntchito ya akazi pa Mphatso za uzimu.

## KUTHANDIZA NTCHITO YA MULUNGU

Akazi m’buku la Machitidwe anapereka zinthu zothandizira ku ntchito ya Mulungu. Lidiya anapereka malo ogona kwa gulu la anthu ofalitsa uthenga la Paulo. Dorika anali ndi utumiki wa akazi amasiye umene umaperekanso zinthu ngati zovala. Ku Akolinto. Paulo ankakhala kunyumba ya Priscilla, amene sikuti amachita naye malonda chabe, komanso kuti anali ndi ntchito yaikulu ku mpingo wa kwa Akolinto. Anamulola Paulo kuchita naye malonda pamodzi.

## ONZUZIKA NDI ONZUNZA

Akazi anakhudzidwanso ndi chinzunzo chimene mpingo oyamba unakumana nacho. Mtumwi Paulo asanatembenuke mtima, Baibulo limanena kuti amalowa m’manyumba ndi mkachisi wopembedzeramo ndi kumanga amuna ndi akazi ndikuwantenga kupita nawo ku Yerusalem kuti akaweruzidwe (Machitidwe 8:3 ndi 9:2). Kenako, anavomereza:

> **Ndipo ndinalondalonda Njira iyi kufikira imfa, ndi kumanga ndi kupereka kundende amuna ndi akazi. (Machitidwe 22:4)**

Akazi anazuzanso mpingo woyambirira. Ku Antiokeya ndi Pisidia, Akazi ena achiyuda amene amatchulidwa kuti (odzipereka olemekezeka) anazuza Paulo ndi Banabasi.

## OCHIMWA ODZIWA UDINDO WAWO

Akazi amayenera kuyankhapo za tchimo. Itha kukhala nkhani yovuta kwambiri m’buku la Machitidwe 5:1-11 ya nkazi otchulidwa Safila amene anagwirizana ndi mwamuna wake kupanga dongosolo la chinyengo la ndalama. Mukawerenga nkhaniyo, onani kuti ikusiyanapo ndi nkhani ya Adam ndi Hava. Apa Satana anaika dongosolo muntima wa mwamuna ndipo Safila anavomereza. Safila anachimwabe chifukwa anali ndi chidziwitso chonse cha tchimo la mwamuna wake ndipo iye anavomereza. Pachikhalidwe, nkazi sangagonjere mwamuna wake ndikugwiritsa ntchito mau akuvera ngati chifukwa chokanira tchito.

Mulingo omwewo wa chiyero umayembekezeredwa kwa otsatira khristu aliyesnse, kaya ndi mwamuna kaya ndi nkazi.

## MAYESO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi lotsogolera

______________________________________________________________

______________________________________________________________

______________________________________________________________

2. Lembani ndandanda wa mautumiki 4 amene akazi anachita m'buku la Machitidwe.

(1)________________________________________________________

(2)________________________________________________________

(3)________________________________________________________

(4)________________________________________________________

3. Werengani ziganizo izi. Ngati chiganizo chiri chowona, lembani T m'mizere yosalembapo. Ngati sichowona, lembani F m'mizere yosalembapo.

_____a Akazi amakaniziwa kunenera mumpingo woyamba

_____b Machimo akazi samawerengaedwa ngati mwamuna wawuza kuti achimwe

_____c Akazi samaloledwa kupemphera ndi kulandira Mzimu Woyera.

_____d Palibe pamene panalembedwa kuti akazi anali mbali imodzi ya mapephero mumpingo.

(Mayankho a mafusowa aperekedwa kumapeto kwa chaputala mbukulino)

**KUPITIRIZA KUPHUNZIRA**

1. Machitidwe analemba kuti akazi anali aneneri mu mpingo oyambirira.

   Chipangano chakale chikuwonetsa kuti anatumikiranso Khristu asanabwere. Werengani mabuku otsatirawa kuti mupeze uthenga ochuluka wa aneneri akazi m'chipangano chakale.

   Mariamu: Exodo 15:20

   Deborah: Oweruza 4:4

   Huldah: 2 Mafumu 22:14; II Mbiri 34:22

   Noadiah: Nehemiya 6:14

   Nkazi amene sanatchulidwe dzina: Yesaya 8:3

2. Malo onse amene mukupezeka nkhani ya akazi mbuku la Machitidwe alembedwa m'musimu. Pitilizani phunziro lanu pogwiritsa ntchito ndandandawu. Malo ena sakunena mwachindunji koma akukamba za magulu akazi. Malo aperekedwa kuti inu mulembe maganizo anu pa malo aliwonse. Awiri oyambirira apangidwa kukhala chitsanzo.

| Malo M'buku la Machitidwe | Nkazi | Maganizo anu |
|---|---|---|
| Acts 1:14 | Mary | Anapempherabe ndi Atumwi |
| 2:17 | Mwana wa Nkazi | Uneneri |
| 2:18 | | |
| 5:1-11 | | |
| 5:14 | | |

6:1

7:21

8:3

8:12

8:27

9:2

**Malo M'buku la Machitidwe** **Nkazi** **Maganizo anu**

Acts 9:14

12:12-16

13:50

16:1

16:13

16:14-40

17:4

17:12

17:34

18:2

18:18

18:26

19:27

21:5

22:9

22:4

23:16

24:24

25:13

25:23

## CHAPUTALA 9

## AZIMAYI M'MAKALATA: MAUTUMIKI A PADERADERA

**Zolinga:**

Mukamaliza phuziroli muyamba kukwanitsa:

1. Kulemba vesi lotsogolera.
2. Kupeza azimayi autumiki amene ananenedwa m'makalata.
3. Kulemba mwachidule mautumiki amene azimaiwa anagwiramo ntchito.
4. Kupitiriza kuwerenga mabuku amakalata pa inu nokha.

**Vesi Lotsogolera:**

> **Pamenepo ndipo iwo akubalalikakitsidwa anapitapita nallikir mauwo (Machitidwe 8:4)**

### MAU OYAMBA

Monga m'mene kunalembedwera m'buku la Machitidwe tinaphuzira poyamba mbali ya azimayi mumpingo woyamba. Gulu la mabuku lotchulidwa kuti "Makalata" limaperekanso chidziwitso chowonjezera chokhudza utumiki wa azimayi mu mpingo woyamba.

Chaputala chino ndi chotsatirachi kamba za kwambiri za "Azimayi m'mabuku a makalata." Chaputala chino chifotokoza za azimayi amene ali ndi mautumiki okhazikika amene atchulidwa m'mabukuwa. Chaputala chotsatira chifotokoza mbali ya azimayi onse mu mpingo woyambirira zimene zinaphuzitsidwa m'makalata. Chaputala chomalizira chimene chimakhudzana ndi "Azimayi m'makalata" chikuima kwambiri pamagulu ena azimai amene mabukuwa anakambapo, (monga osakwatiwa, amasiye, okwatiwa, ang'ono, okalamba, ana, ndi ena) ndi malangizo ena okhudzana ndi mavalidwe komanso makhalidwe azimayi

### MAKALATA

Chipangano chatsopano chiri ndi magulu akulu akulu. Izi zikuphatikiza mabuku a wuthenga wabwino, amene ndi mabuku monga Mateyu, Marko, Luka, ndi Yohane amene amafotokoza za moyo ndi utumiki wa Yesu Khristu.

Machitidwe ndi gawoso lina limene limafotokoza uthenga wakukhazikika kwa mpingo woyamba. Pali buku la uneneri limene ndi lomalizira m'chipangano chatsopano. Limatchulidwa kuti Chivumbulutso.

Mabuku ena onse a chipangano chatsopano amatchulidwa kuti makalata chifukwa chakuti analembedwa kwa anthu ngati makalata. Ndimbali imodzi ya mau a Mulungu ndipo amagwira ntchito kwa okhulupirira onse kuwonjezera amene sanalembedwa kwa iwo.

M'musimu muli ndandanda wa Makalata ndi maina amene analembedwa motsogozedwa ndi mzimu woyera.

Makalata awa analembedwa ndi Mtumwi Paulo

Aroma

1 Akolinto

2 Akolinto

Agalatiya

Aifeso

Afilipi

Akolose

1 Atesolonika

2 Atesalonika

1 Timoteo

2 Timoteo

Tito

Filipo

Filimoni

Ahebeli

Mabuku awa anatchulidwa potsatira amene analemba

Yakobo

1 Petro

2 Petro

1 Yohane

2 Yohane

3 Yohane Yuda

## AZIMAYI AMENE ANALI NDI MAUTUMIKI M'MABUKU A MAKALATA

## AZIMAYI AKU AROMA

M'buku la Aroma, Febe anatenga mau a chiphuzitso kwa okhulupirira akwa Aroma. M'malembo oyambirira a chigiriki, Febe atanthauza kuti "diakonos". Mau awa mapezeka kokwanira ka 22 m'chipangano chatsopano. Kokwanira ka 18 amatanthawuziridwa "woyang'anira mpingo" ndipo katatu **"**ntumiki**".** Tanthawuzo la Febe, linasithidwa kukhala kapolo, mwina chifukwa cha kukondera kumbali ya omasulira.

Pomuwonetsa Febe kwa okhulupirira aku Aroma, Paulo akuti:

> **Kuti mumlandire iye mwa Ambuye, monga kuyenera oyera mtima, ndi kuti mumthandize m'zinthu zili zonse adzazifuna kwa inu; pakuti iye yekha anali wosungira ambiri, ndi ine ndemwe. (Aroma 16:2)**

Ena pankhaniyi anaganiza kuti Febe anathandiza Paulo ngati mlendo, kumudyetsa, kuchapa ndi kusita zovala zake, ndi zina. Koma mau akuti "succourer" amatanthauza kuti othandiza kuwonjezera patanthawuzo lakuti "amene amaima pamaso pa mtsogoleri". Chimene Paulo akupempha ndichomwecho, akupempha atsogoleri ndi akulu ampingo pa 1 Atesalonika 5:12-13 ndi 1 Timoteo 5:17.

Pa Aroma 16, Paulo akufotokoza za mzimayi wina wa kwa Aroma, Prisca amene anakwatiwa ndi Aquila. Ameneyu ndi mzimayi yemweyo amene akutchulidwa ndi Luka kuti "Priscilla". Dzina lake limadziwika kwambiri kuti Prisca. Tinaphuzira kale za mzimayi ameneyu m'chaputala 8.

Mau akuti "othandiza" amene Paulo anagwiritsa ntchito pofotokozera amatanthawuza "ogwira naye ntchito." Paulo akutsimikiza kuti Prisca ndi Aquila sanangoika moyo wao pa chiswe koma anagwira nao ntchito mutumiki wa pakati pa mipingo ya amitundu.

Azimayi ena pa ndandanda wa Paulo ndi monga Marita, amene anagwira ntchito molimbika chifukwa cha okhulupirira; Narcissus, amene anali mtsogoleri wa banja; Tryphena and Tryphosa, amene maina ake atanthauza "kusangalatsa kapena kukoma"; ndi "Persis Okondedwa amene anagwira ntchito molimbika mwa ambuye. Pali mzimayi wina dzina lake Julia amene sizinanenedwa za iye, ndi azimayi ena awiri amene maina awo sanatchulidwe, amayi a Rufus ndi

mchemwali wa Nereus. Junia, anatchulidwaponso pa Aroma 16:7, anadziwika ndi atumwi chifukwa cha chikhulupiriro chake, ndipo anali kapolo mzao ndi Paulo chifukwa cha Khristu.

**AZIMAYI M'MAKALATA ENA:**

Chloe akutchulidwa pa 1 Akolingo 1:11. Anatumiza reporoti kwa Paulo lokhudza zinthu zina zosokoneza zimene zimachitika mu'mpingo. Kwa Akolinto, M'buku la Filimoni Paulo akulankhula ndi Apphia, nkhazi wa Filimoni. Banja iri linali ndi mpingo kunyumba kwao mongao Lydia ndi Nympha.

Euodiya and Suntuke anatchulidwa pa Afilipi 4:2 anatha kugwira ntchito yakulalikira, kuyambira pamene Paulo anafotokozera kuti "azimayi amenewa anagwira ntchito kuvutika ndi ine muthenga wabwino…ndi ogwira ntchito azanga".

Paulo akuperekabe moni kwa 'Klaudiya ndi abale ena onse" pa 2 Timoteo 4:21 ngakhale sitikuwuzidwa chirichonse chokhudzana ndi mzimayi ameneyu.

## MAU OTSIRIZA

Kawuniwuni wa azimayi amene anatchulidwa m'makalata akuwonetsa kuti azimayi mumpingo woyamba sanali ongokhala chabe. Anavutika pamodzi ndi amuna amene amkafalitsa uthenga wabwino.

Azimayi awumulungu anagwira ntchito ngati ogwira ntchito azao amuna, anali ndi udindo waukulu, kuika zinthu m'malo mwake m'mipingo imene inali m'manyumba mwawo ndipo anamangidwanso chifukwa cha chikhulupiriro chawo. Monga okhululupirira ena onse, azimayiwa anazuzikanso chifukwa cha chikhulupiriro chawo. Ndipo izi zinawakakamiza kuti aturuke mu Yerusalem, ndipo analalikira uthenga kulikonse kumene anapita.

> **Pamenepo ndipo iwo akubalalitsidwa anapitapita nalalikira mauwo. (Machitidwe 8:4)**

Azimayi amenewa amapereka chilimbikitso kwa akhristu achizimayi amene amafuna malo awo autumiki mukholola limene liri pa dziko lapansi.

**MAYESO AKUDZIYESA NOKHA**

1. Lembani vesi lotsogolera

____________________________________________________________

____________________________________________________________

____________________________________________________________

2. Onani ndandanda wa maina m'musimu. Pezani chiganizo m'ndandanda wachiwiri umene ukufotokozera bwino dzina lirilonse. Lembani nambala ya chiganizo chimene chikufotokozera dzina limene liri m'ndandanda.

| | |
|---|---|
| ___ (Febe) | 1. Kuika moyo wake pa chiswe chifukwa cha Paulo |
| ____ (Junia) | 2. Anatenga buku la Aroma kuchokera kwa Paulo kupita nalo ku mpingo wa kwa Aroma |
| ____ (Lidiya) | 3. Anatumiza reporoti kwa Paulo lokhudza mpingo wa ku Akolinto. |
| ____ (Kloe) | 4. Kapolo mzake wa Paulo |
| ______ Priska | 5. Anali ndi Mpingo ku nyumba kwake |

(Mayakho a mafusowa aperekedwa m'chaputala chomaliza mbukuli)

## KUPHUZIRA ZAMBIRI

Kuwonjezera ntchito za pamoyo wa anthu zimene azimayi ali nazo zimene ma chaputalawa akuimapo, makalata amaphuzitsanso zinthu zambiri zofunika pa miyoyo ya okhulupirira. Kuti mukulitse chidziwitso chanu pa mfundo zimenezi, komanso kuti muwoneso phunziro la azimayi m'makalata, tikuganiza kuti muwerenge buku lililonse mwa mabuku awa. Kugwiritsa ntchito ma pepala apadera, konzani tchati cha buku lililonse. Pa ndandanda wa tchati uliwonse:

**Dzina la buku:** Lembani dzina la buku

**Olemba:** (Izi zaperekedwa nkati mwa chaputalachi)

**Kulembedwa ku:** Mukuyenera kupeza kuti Kalata ikulembedwa kwa ndani m'chaputala choyambirira. Kubukirani, ngakhale buku lilironse likupita kwa okhulupirira enieni mumpingo woyamba, lirilonse ndi lowuzilidwa ndi mpweya wa Mzimu woyera ndipo atha kugwira ntchito kwa okhulupirira aliyense.

Mukamawerenga Chaputala chirichonse, lembani uthenga uwu pa tchati chanu:

**Nambala ya Chaputala:** Nambala ya Chaputala chimene mukuwerenga.
**Kumangirira Chaputala:** Mukamamangirira mulembe mwachidule ndi mau anu uthenga umene uli mu ntchaputala.

**Ndime yotsogolera m'chaputala:** Vesi lotsogolera ndi mau amene mwasankha kuchokera m'chaputala imene imamangirira mfundo zikulu zikulu m'chaputalacho.
**Kugwiritsa ntchito pa Munthu:** M'mene mukagwiritsire ntchitio zimene zaphuzitsidwa pa moyo wanu? Fotokozani m'mene chaputala chikukukhudzirani.

**Kalata yaifupi ya Yuda ikuwunikidwa m'musimu ngati chitsanzo m'ndondomeko ya m'chaputalachi:**

**Dzina la buku:** Yuda

**Olemba:** Yuda (ndime 1)

**Kulemba kwa:** Amene ali opatulidwa ndi Mulungu Atate, kusungidwa mwa Yesu

Khristu, ndi kuitanidwa. (Ndime 1)

Nambala ya Chaputala: 1

**Kumangirira:** Yuda akuchenjeza okhulupirira kuti achenjere ndi onyenga ndikukakamira chikhulupiriro chowona.

**Ndime yotsogolera:** Koma abale, kumbukirani mau amene analankhulidwa ndi atumwi a Ambuye wanthu Yesu Khristu. Ndime 17.

**Kagwiritsidwe ntchito:** Ali onyenga amene atha kuyesera kukuchotsani kuchikhulupiriro chowona mwa Yesu Khristu. Ndikuyenera kutsatira malangizo kuyambira pa ndime ya 20 mpaka 21 pewani kunamizidwa.

## CHAPUTALA 10

## AZIMAYI M’MAKALATA: MAUDINDO MU MPINGO

**Zolinga:**

Mukamaliza phuziro iri muzikwanitsa:

1. Kulemba Vesi lotsogolera
2. Kufotokoza nkhani zimene zinalembedwa ndi Paulo zokhudza azimayi
3. Kulemba mwachidule mbali ya azimayi mu mpingo wakele monga zimaphuzitsidwira m’makalata.

**Vesi lotsogolera:**

> **Muno mulibe Myuda, kapena Mherene, muno mulibe kapolo, kapena mfulu, muno mulibe mwamuna ndi mkazi;(Agalatiya 3:28)**

### MAU OYAMBA

Chaputala chapitachi chinafotokozera za azimayi ndi mbali yawo yeniyeni imene inanenedwa m’makalata. Tsopano timphuzira mbali chabe ya azimayi mu mpingo monga zikuwonekera m’mabuku omwewo.

Ziphuzitso zina ntumwi Paulo zokhudza azimayi ndizovuta kuzivetsetsa. Ngakhale ntumwi Petro ananenapo kuti ndikovuta komasulila zonse zimene Paulo anagawana nafe motsogozedwa ndi mzimu woyera:

> **Mongaso m’makalata ache onse pokamba momwemo za izi; m’menemo muli zina zovuta kuzizindikira, zimene anthu osaphuzira ndi osazindikira apotoza monganso atero malembo ena ndi kudziononga tsogolo la iwo eni. (2 Petro 3:16)**

Petro akunena kuti pali zinthu zina zimene ndizovuta kuzivetsetsa, koma okhawo amene ndi osaphunzira ndi osakhazikika amatsutsana nazo. Kutsutana uku kumabweretsa chiwonongeko chawo. Kutsutsana pa zinthu zimenezo sikuthandiza aliyese ndipo zimawononga amene akutsutsa.

Anthu odziwa mau a Mulungu ambiri anafotokozera chiphuzitso cha Paulo kwa azimayi mjira zambiri. Kumbukirani kuti pamene mamasulidwe akusiyana, mtsutso suyenera kubuka pakati pa okhulupirira.

Ngati chiphuzitso mbuku lino chikusiyana ndi m’mene inu mumamasulira kapena cha mpingo wanu, chonde kumbukirani kuti sichinali cholinga kupangitsa magawano. Ngati muli ndi

kukhudzika kwina pokhudzana ndi mbali ina, mukuyenera kukhazikikamo chifukwa cha chikumbu ntima chanu, monga Paulo akunenera. Ndibwino kukumbukira kuti malamulo onse m'malata a Paulo, komanso makalata ena, anaperekedwa popeza azimayi mumpingo anali amachitachita mutumiki. Taphuzira kale za machitachita awo m'machaputala a m'Machitidwe ndi Makalata. Palibe nkhani m'Makalata itha kugwiritsidwa ntchito kukaniza azimayi mpata wa utumiki monga azimayi mumpingo woyamba.

**KUPHUZITSA NDI KULALIKIRA**

Imodzi mwa mkhani m'makalata imene imasokoneza ntchito ya azimayi mu mpingo iri pa 1 Akolinto:

> **Pakuti Mulungu Sali Mulungu wa chisokonezo koma wanntenedere; monga mwa Mipingo yonse ya oyera mtima. Akazi akhale chete m'Mipingo. Pakuti sikuloledwa kwa iwo kulankhula, koma akhale omvera, monganso chilamulo chinena, koma ngati afuna kuphunzira kanthu afunse amuna awo aiwo okha kwao; pakuti kunyazitsa mkazi kulankhula mau mpingo. (1 Akolinto 14:33-35)**

Ndime zimenezi zimagwiritsidwa ntchito pokaniza azimayi kulalikira kapena kuphuzitsa mu mpingo. Paulo sakutanthawuza kuti azimayi akuyenera kukhaliratu chete. M'machaputala ambuyomu, akupereka tsatanetsatane wa kuti chifukwa chani mzimayi akuyenera kufunditsa mutu wake akamapephera kapena kunenera. (Tikambirananbe za ndime zimenezi kutsogolo kwa chaputalachi). Chifukwa chani tikuyenera kutaya nthawi kukambirana ngati samayenera kulankhula mu mpingo?

Mphuziro lanthu la ku Machitidwe, munaphuzira za kubwera kwa Mzimu Woyera Petro ananena ngati kukwaniritsa uneneri wa Yoweli. Uneneri umati mzimu woyera udzafika pa ana akazi, amuna, ndi adzakazi ndipo adzanenera.

1 Akolingo 14 itha kukhala imodzi mwa ndime zimene Petro amati "ndizovuta kuvetsetsa" m'makalata a Paulo. Chothandiza kwambiri ndi kuti tivetsetse tanthawuzo la mau a Chigriki omasuliliridwa "kulankhula" ndime 34. Apapa mau sakufotokoza za kulankhula pagulu, koma kucheza, kufusa ndi kutsutsana."

Werengani 1 Akolinto 14 m'Baibulo lanu. Muwona kuti cholinga cha Paulo m'chaputalachi ndikupewa chisokonezo mumpingo. Chokhumba chake ndi chakuti chilichonse chichitika mwadongosolo nthawi ya chipembedzo. Ndichifukwa chake akuwuza azimayi kuti asafuse kapena kucheza pamene chipembedzo chili nkati koma kudikira ndikufusa azimuna awo kunyumba.

Chikhalidwe cha anthu amene malangizowa akupita ndichofunika kulingaliranso. M'mipingo ya chiyuda, azimayi amakhala mbali imodzi, ndipo abambo amakhalaso mbali ina. Azimayi sikuti amangocheza chabe koma amafusa mafuso mokweza kwa azimuna awo mbali ya azibambo.

Munthu m'modzi amene amagwira ntchito pakati pa Ayuda akuti ngakhale lelo anava Wankhulu wa tchalitchi akumenya pa gome akuwuza azimayi kuti akhale chete.

Dongosolo ndi chimene Paulo akufuna nkhaniyi ndipo sikuti pali kutsutsana ndi zimene iye akufotokozera pa dongosolo la mapephero. (1 Akolinto 14:26-27, 29-31)

Machitidwe amapephero amene Paulo akufotokoza akuwoneka kuti ndi misonkhano yokhazikika. Akuwuza aliyese amene ali ndi masalimo, chiphuzitso, malilime, vumbulutso kapena mamasulidwe kuti achite mwa dongosolo. "Aliyese kuphatikiza azimayi". **BATA**

Nkhani ina ya m'makalata tikuyenera kukambirana pano chifuka ndiyofanana ndi nkhani ya Akolinto.

> **Mkazi aphunzire akhale wawchete m'kumvera konse. Koma sindilola ine kuti mkazi aphunzitse, kapena kulamulira mwamuna; komatu akhale chete. Pakuti Adamu anayamba kulengedwa, pamenepo Heva; (1 Timoteo 2:11-14)**

Mau awa akuti "bata" sakutanthawuza kuti azimayi asalankhule. Ngati amayenera kuphunzira mwa bata, sakanafusa mafuso kapena kukambirana zimene amaphunzira. Ndi mau akuti "bata" Paulo akufuna kudekha, ndi nzimu wosasokoneza wa kuphunzira.

Mau akuti "kutenga mphavu" akutanthawuza kuti kunena zochita kapena kulamulira abambo, kuchita zinthu pogwiritsa ntchito ulamuliro. Aliyese wa ife sakuyenera kuchita zinthu mwa mphavu zake. Mukamaphuzira tikamakambirana pa mutu wa kugonjera, tonse tikuyenera kugonjera kwa mzake, mwamuna ngakhalenso mkazi chimodzimodzi. Koma m'nkhani iyi, Paulo akuchenjeza azimayi, kuti sakuyenera kukhala ndi maganizo akulamulira azimbambo.

## UCHIMO OGONANA

M'ndime izi Paulo sakudzudzula azimayi kumbali yawo yogwa m'tchimo limeneli kapena kuwonetsa kuti kumbali ya kugonana ndi ochimwa kwambiri. Akungowonetsa kuti chimene Heva atachita mwa chifuniro, ndi mphavu yake ananyengedwa. Mumadziyika nokha pa chiopsezo chonamizidwa mukalankhula, kapena kuchita zinthu molamula, ndi ulamuliro, kapena kuwuza anthu zinthu mwa ulamuliro wa inu nokha**.**

Pakhani ya kugwa, Paulo sakuchotsa mwamuna pa udindo wake. Hava ananyengedwa naganiza kuti akhala ngati Mulungu. Adam sananamizidwe koma anachimwa akudziwa bwino zotsatira za zimene amapanga.

## KUTCHINGA

Nkhani ya nkhazi ndi chotchinga, imene yatchulidwa m'mwambamu ndi imodzi mwa mitu imene anthu amakambirana kwambiri. Nkhani iyi imapezeka pa 1 Akolinto chaputala 11: 3-16.

Tisanapirile kukambirana pa mutuwu werengani ndime ya 3 kulekeza 16.

Mau aku “mutu” ndime zimenezi ena amawamasulila kuti mwamuna ndimtsogoleri wa mkazi. Mau achi Hebeli amene anagwiritsidwa ntchito atha kutanthawuza “mtsogoleri” komanso kuyamba. Paulo amatanthawuza za kukhala oyambirila kapena mtsogoleri wa mpingo, monga mwamuna analengedwa koyamba m’chifanizo cha Mulungu, ndiwoyambirira kwa nkazi amene akuchokera kwa iye. M’chaputala chotsatirachi, tiphunzira za “utsogoleri” ndi kugonjera timawerenga malangizo m’mabuku a makalata opita kwa akazi. Nkhawa yathu ndi gawo ili, pa m’mene azimayi ayenerera kupempherera kapena kunenera.

Ena amaganiza kuti malangizo amenewa akuwonetsa kuti akazi akuyenera kukhala ndi tsitsi lalitali ndipo asamamete chifukwa limapangitsa kukhala chophimba. Ena amakhulupirira kuti zimatanthawuza kuti nkazi ayenera kuvala chisoti akamapita ku mapemphero ndi cholinga chomphimba mutu wake. Choyenera kukumbukira mukamamasulira nkhani imeneyi ndizimene Paulo analakhula pamapeto pake ndime ya 16:

> **Koma akaoneka wina ngati wotetana, tiribe makhalidwe otere kapena ife, kapena Eklesia wa Mulungu (1 Akolinto 11:16)**

Ananena kuti sipakuyenera kukhala kulimbana kapena mtsutso pa mutu umenewu. Ndime ya 18 akuwonetsa nkhawa yake pa magawano amenewa mumpingo wa ku Akolinto. Nkhawa yaikulu ya Paulo inali dongosolo ndi umodzi mumpingo. Kumasulira kulikonse kumene kungaperekedwe sikukuyenera kubweretsa magawano.

Nkani imeneyi ikuwonetsa kuti mwamuna ndamene anayamba kupangidwa kenako nkhazi. Ikunena kuti aliyese siwokwanira payekha.  Amuna andi akazi analengedwa kuti akhale chitonthozo ndi mdalitso kwa wina andi mzake osati wina kapolo ndipo wina olamulira mwankhaza. Monga mkazi anapangidwa koyamba kuchokera kwa mwamuna, kuyambira kale mwamuna sanapangidwe kuchokera kuthupi la nkhazi. Monga m’mene chiliri chifuniro cha Mulungu kuti nkazi avomereze mbali yake ya kugonjera mwamuna, chomwechonso ndi chifuniro cha Mulungu kuti mwamuna asagwiritse ntchito udindo wa utsogoleri wake.

Paulo akulankhula za ubwino wakuti nkazi azipemphera ali ndi chophimba chenicheni pa mutu wake. Nthawi ya Paulo, nkazi wapabanja akavala chophimba zimatanthawuza kuti amagonjera kwa mwamuna wake. Linali khalidwe lakunja lokhala ndi tanthawuzo lankati. Paulo akuti tsitsi la nkhazi litha kukhala chizindikiro cha kuphimba (ndime 15). Sizinali zofunika kwenikweni kuti mwamuna avale chophimba chifukwa anali ophimba wankazi, oyikidwa ndi Mulungu kuti atsogolere mwachikondi ndi kumusamalira.

Nkhani sikunena kuti akazi osakwatiwa sangapephere kapena kunenera mumpingo. Tanthawuzo ndi la kuti pamene akazi akupephera ndi kutumikira,  akuyenera kupanga choncho ndi maganizo akugonjera kwa Mulungu ndipo ngati ali pa baja, kwa mwamuna wake.  Maganizo amabweretsa phavu ya Mulungu ndi angero kukhazikika pa iye. Kupephera kapena kunenera ndi maganizo

owukira sikothandiza. Ubale wabwino ndi Mulungu ndi mzanu wapabanja ndiwofunika pa utumiki wamphavu.

Ena amasungabe chikhalidwe chovala chisoti kapena chotchinga nthawi yamapephero kukhala chizindikiro cha mawonedwe abwino azinthu. Ena amalolabe kuti azimayi azikhalabe ndi tsitsi lalitali ndi cholinga chomwecho. Izi ndi zinthu zolamulidwa ndi chikhalidwe kapena kutsimikizika kwa ntima ndipo zikuyenera kulemekezeka koma osati zikhale zinthu zotigawanitsa.

Mfundo yofunika pa chiphuzitso cha Paulo ndi iyi: Nkazi wa chikhristu akuyenera kukhala pa ubale wabwino ndi mwamuna wake powonetsa maganizo achikondi ndi kugonjera kwa iye monga m'mene amachitira kwa Yesu Khristu. Utumiki opanda mawonedwe amenewa azinthu sungachitike bwino. Kaya izi ziwonetseredwa ndi chikhalidwe chovala (velo) kapena tsitsi lalitali ngati nthawi ya Paulo sizofunika.

**KUMANGIRIRA**

Pankhani zonse zimene takambirana mphuziloli, palibe nkhani imene ikuletsa utumiki wa azimayi mumpingo. Ngati azimayi amayenera kukhalalilatu chete osaphuzitsa kapena kulalikira nanga chifukwa chani azimayi achipangano chatsopano amakhala ndi mipingo m'makomo mwawo? Chifukwa chani Paulo akupereka mwatsatanetsatane malangizo ngati anali olakwitsa potenga udindo wautsogoleri umenewu mumpingo? Chifukwa chani anapereka mwatsatanetsatane malangizo am'mene akuyenera kunenerera (kulakhula) mu tchalitchi pakukhala ndi chophimba choyenera?

Tikuyenera kuwona nkhani zimenezi monga m'mene Paulo amawonera mutu wa azimayi. Mau ake otsiriza ndi:

> **Muno mulibe Myuda, kapena Mhelene, muno mulibe kapolo, kapena mfulu, muno mulibe mwamuna ndi mkazi;(Galatiya 3:28)**

Zotchinga zonse zokhudzana ndi chikhalidwe zawonongedwa mudzina la Yesu. Zotchinga zonse zokhudzana ndi magulu anthu zasungunuka tikamalowa munthupi la Khristu ngati okhulupirira owona. Kaya kapolo (womangidwa) kapena mbuye (waufulu), tiri amodzi mwa Khristu. Chofunika kwambiri kwa azimayi, palibe mwamuna kapena nkhazi mwa khristu. Monga mwa masankhidwe,ndi madzozedwe a Mulungu aliyese atha kusankhidwa posatengera kuti ndi mwamuna kapena nkazi akamawakozekeretsa ku ntchito yake.

## KUDZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi lotsogolera

___________________________________________________________________________

___________________________________________________________________________

___________________________________________________________________________

2. Werengani ziganizo m'musimu. Ngati chiganizo chiri chowona lembani T panzere umene uli koyambirira. Ngai chiganizo sichiri chowona lembani F panzere umene uli koyambirira.

a____ Petro anati zolemba za Paulo ziri ndi zinthu zina zimene ndizovuta kuzivetsetsa. b____ Azimayi akuyenera kukhaliratu chete mu tchalitchi. c____ Azimayi sakuyenera kuphuzitsa kapena kulalikira mu tchalitchi d____ Uneneneri wa Yoweli ukuwonetsa kuti azimayi adzanenera kapena kulankhula mwakudzoza kwa Mzimu woyera.

e____ Mau akuti "bata" amena angawiritsidwa ntchito ndi Paulo amafuna kudekha, osati mzimu wachisokonezo. f____ Paulo akuwonetsa akazi ngati ochimwa kwambiri pakhani ya kugonana. g____ Adamu ananamizidwa ndichifukwa chake anachimwa. h____ Palibe mwamuna kapena nkazi mwa Yesu Khristu.

(Mayankho amafusowa apatsidwa m'chaputala chomalizira kumapeto Kwa bukuli)

## KUPITILIZA KUPHUZIRA

M'musimu muli ndandanda wa malo onse amene amene khani kapena mutu wa azimayi ukupezeka m'mabuku a Makalata. Gwiritsani ntchito ndandandawu kuti mupitilize kumphunzira zakuti Makalata amaphuzitsa kuti chani zokhudzana ndi azimayi. Onani malo aliwonse ndipo lembani mwachidule m'malo amene mwapatsidwa.

## KUMANGIRIRA

**Malo**

**Aroma** 1:26

______________________________________________________________

1:27

______________________________________________________________

7:2

______________________________________________________________

7:3

______________________________________________________________

7:4

______________________________________________________________

16:13

______________________________________________________________

**I Akolinto** 5:1

______________________________________________________________

7:1

______________________________________________________________

7:2

______________________________________________________________

7:3

7:4

7:8

7:9

7:10

7:11

7:12

7:13

7:14

100

7:16

7:27

7:28

7:29

7:32

7:33

7:34

7:36

7:38

7:39

9:5

11:3

11:5

11:6

11:7

11:8

11:9

11:10

11:11

11:12

11:13

11:15

101

14:34

14:35

**Agalatiya** 1:15

4:4

4:22

4:23

4:26

4:30

4:31

**Aifeso** 5:23

5:24

5:25

5:28

5:31

5:33

6:2

**Filipo** 4:3

**Akolose** 3:19

**I Atesalonika** 5:3

**I Timoteo** 1:9

2:9

2:10

102

2:11

2:12

2:14

3:2

3:11

3:12

4:3

4:7

5:2

5:9

5:11

5:14

5:16

**2 Timoteo** 1:5

3:6

**Tito** 1:6

2:3

2:4

**Ahebeli** 7:3

**I Petro** 3:1

3:5

3:7

103

## CHAPUTALA 11

## AZIMAYI M'MABUKU A MAKALATA: MALANGIZO APADERA

**Zolinga:**

Mukamaliza phuziroli muyamba kukwanitsa kuchita izi:

1. Kulemba Vesi lotsogolera
2. Kuwonetsa kuti mukuvetsetsa malo osiyanasiyana m'makalata amene akukamba za:

    -Azimayi amasiye

    -Azimayi amene ali ndi ana

    -Azimayi amene Sali pa banja -Akazi okalamba

    -Azimayi ochepa m'nsikhu

    -Azimayi okwatiwa

    -Amene mabaja awo anatha

3. Kulemba mwachidule chiphuzitso cha m'baibulo chokhudzana ndi mavalidwe, ndimakhalidwe ena onse azimayi.

**Vesi lotsogolera:**

**Ndi kumverana wina andi mzake m'kuopa Khristu. (Aifeso 5:21)**

### MAU OYAMBA

Mabuku a makalata amalankula ndi azimayi apanja, sali pa banja, amasiye, okalamba, ndi azimayi achichepere. Mchaputalachi muphunzira malangizo amene akuperekedwa kwa azimayi amenewa ndi amagulu ena. Muphunziranso za mavalidwe ndi machitidwe azinthu oyenera azimayi.

### MABANJA

Okhulupiria aku Akolinto anamufusa Paulo za maukwati ndi kukhala osakwatira (kukhala osakwatira chifukwa chakudzipereka kuntchito ya Ambuye). Maganizo a Paulo ngati munthu anali akuti osakwatiwa komanso azimayi amasiye atha kukhala osangalala ngati atakhalabe paokha:

**Koma ndinena kwa osoakwatira, ndi kwa akazi amasiye kuti kuli bwino iwo ngati akhala monganso ine. (1 Akolinto 7:8)** Anaperekanso maganizo ake:

> **Chotero iye amene akwatitsa mwana wake wamkazi achita bwino ndipo iye wosamkwatitsa achita koposa. (1 Akolinto 7:38)**

Paulo anati pa 1 Akolinto 7:2 ukwati umapereka zosowa za pa moyo wakuthupi komanso ntendere wa anthu:

> **Koma chifikwa cha madama munthu yense akhale naye mkazi wa iye yekha, ndi mkazi yense akhale naye mwamuna wa iye yekha. (1 Akolinto 7:2)**

Munthu aliyese amene Sali pa banja, mwamuna kapena nkazi, amene ali ndi chilakolako chakugonana akuyenera kukwatiwa. Paulo akunena kuti chifukwa chake pakupereka chifukwa chimene anthu angaganizire kusakhala pa banja.

> **Koma ichi ndinena mwa kupindula kwanu kwa inu nkha; sikuti ndikakuchereni msampha, koma kukuthandizani kuchita chimene chiyenera, ndi kutsata chitsatire ambuye, opanda chocheukitsa. (1 Akolinto 7:35)**

Okhulupirira akuyenera kukwatira nkhristu. Sitikuyenera "kukhala pa goli" ndi anthu osakhulupirira pankhani ya banja.

## AKAZI AMASIYE

Nkhani ina m'makalata ikunena za azimayi amasiye:

> **Asawerengedwe wa masiye ngati sanafikire zaka makumi asanu ndi limodzi,**
>
> **atakhala mkazi wa mwamuna m'modzi, wa mbiri ya ntchito zabwino; ngati walera ana, ngati wachereza alendo, ngati adasambitsa mapazi a nzeru mtima, ngati wathandiza osautsidwa, ngati anatsatadi ntchito zonse zabwino. (1 Timoteo 5:9-10)**

Nkazi wamasiye amene akufuna kukhala osakwatiwa ndikudzipereka ku umiki akuyenera kukhala osachepera zaka makumi asanu ndi limodzi, anakwatirapo kamodzi, ndipo ali ndi mbiri yabwino pa ntchito yake ya chikhristu. Akazi amasiye ang'ono sakuyenera kukhala ma membala agulu limeneri chifukwa atha kuganiza kukwatiwanso ndikuwononga  pangano lawo lakusakhala pabanja chifukwa cha ntchito ya Mulungu. 1 Timoteo 5 ikutsogolera mpingo kuti mpingo upereke zofunika kwa azimayi amasiye amene alibe mabanja amene  atha kuwasamalira.

## AZIMAYI ANG'ONO NDI OKALAMBA

Paulo akulangiza azimayi ang'ono ang'ono kuti:

**Chifukwa chache nditi akwatiwe amasiye ang'ono, nabale ana naweruzire nyumba osapatsa chifukwa cha mdaniyo chakkulalatira; (1 Timoteo 5: 14)** Azimayi okalamba akupatsidwanso malangizo:

> Momwemonso akazi okalamba akhale nao makhalidwe oyenera anthu oyera, osadierekeza, osakondwa nacho Chikondi cha pavinyo akumphuzitsa zokoma; kuti akalangize akazi ang'no ome akonde amuna awo, akonde ana awo akahale odziletsa, odekha ochita m'numba mwao, okoma, akumvera amuna a iwo okha, juti mau a Mulungu angachitidwe mwano. (Tito 2:3-5)

Pa zothitika za mumpingo azimayi akulu achikhristu akuyenera kuphuzitsa azimayi ang'ono. Utumiki uwu umaiwalidwa m'mipingo yambiri masiku ano.

## AZIMAYI A PABANJA

Pamene Mulungu analenga Adamu ndi Hava kumayambiriro adziko, anakhazikitsa banja. Dongosolo lenileni la Mulungu linali lakuti mwamuna m'modzi ndi nkazi modzi kwa moyo wao onse. Kutha kwa banja sikunali mbali imodzi ya dongosolo lenileni la Mulungu koma zimachitika chifukwa cha kuuma mtima kwa muthu. Tchimo linawumitsa ntima ndikubweretsa chimasomaso, chigololo, ndi kusiyidwa, zonsezi ndi zifukwa za kutha kwa banja monga mwa malembo.

Chimasomaso ndi ntchitidwe uliwonse wakugonana chitsanzo kugonana amuna kapena akazi okha okha, kapena kugonana pachibale. Chigololo ndi kugonanana ndi muthu amene sali nkazi wako. Paulo akuti:

> **Pakuti mkazi wokwatidwa amangidwa ndi lamulo kwa mwamuna wache wamoyo; koma mwamunayo akafa, iye amasulidwa ku lamulo la mwamunayo. Ndipo chifukwa chake ngati iye akwatiwa ndi mwamuna wina, pokhala mwamuna wache wamoyo, adzanenedwa mkazi wachigololo; koma mwamunayo akafa, iye amasulidwa ku lamuloli; chotero sakhalanso wachigololo ngati akwatiwa ndi mwamuna wina. (Aroma 7:2-3)**

Ngakhale kuti ndime zimenezi ziri ndi tanthawuzo lapabanja zitha kukhalanso ndi tanthawuzo lina. Paulo anafotokoza chitsanzo ichi pofuna kuwonetsa kuti ndi chifukwa chani tikuyenera kufa ku lamulo ndi zotsatira zake ndi kukwatiwa naye Yesu Khristu.

Posatengera tchimo limene tachita, zotsatira zobwera ndi chilamulo cha m'chipangano chale zimachepetsedwa pamene tabwera kwa Yesu. Sitilinso pansi, kapena kukwatiwa ndi, chlamulo. Mphavu imene inatigwira inagwetsedwa. Tirinso ndi ubale watsopano ndi Yesu Khristu. Ngakhale munasiyidwa pabanja pa zifukwa zosagwirizana ndi malemba, sitchimo lakuti simungakululukidwe. Litha kukhululukidwa ndi Mulungu monga tchimo lililonse.

Banja ndi lolemekezeka, koma kuchita ntchitidwe ogonana kunja kwa banja ndi koipa:

**Ukwati uchitidwe ndi ulemu ndi onse, ndi pogona pakhale posadetsedwa; pakuti adama ndi achigololo adzawaweruza Mulungu. (Ahebeli 13:4)** Atesalonika analemba:

**Yense wa inu adziwe kukhala nacho chotengera chache m'chiyeretso ndi ulemu (1 Atesalonika 4:3)**

Malangizo ena anaperekedwanso m'makalata okhudzana ndi azimayi amene ndi atumiki mu mpingo:

**Momwemonso akazi akhale olemekezeka, osadierekezsa, odzisunga okhulupirika m'zonse. (1 Timoteo 3:11)**

Petro analemba lonjezo labwino la akazi amene anakwatiwa ndi anthu osakhulupirira:

**Momwemonso, akazi inu, mverani amun anu ainu nokha; kuti, ngatiso ena samvera mau, akakondwe opanda mau mwa mayendedwe a akazi; pakuona mayendwe anu oyera ndi kuopa kwanu. (1 Petro 3:1-2)**

Nkazi amene mwanuna wake sanapulumutsidwe, opanda mau atha kumutengera kwa Mulungu pa kugonjera mwachikondi. Mwamuna akawona khalidwe la chiyero la umulungu ndi kuwopa Mulungu kwake. Awona kusintha kumene Khristu wapanga m'moyo wake kudzera ku chitsanzo chake amakokedwa kwa mpulumutsi.

Paulo anati ngati mwamuna osakhulupirira akufuna kukhala ndi nkazi wake, akuyenera kukhala ndi iye.

**Ndipo nkazi amene ali naye mwamuna wosakhulupiria, nabvomera mtima iye akukhala naye pamodzi, asalekane naye mwamunayo.**

**Koma, monga Ambuye wagawira kwa yense, monga Mulungu waitana yense, momwemo ayende. Ndipo kotero ndiika m'Mipingo yonse. (1 Akolinto 7:13 ndi 15)**

Chifukwa chimene Paulo akunenera kuti nkazi akhalebe ndi mwamuna osakhulupirira:

**Pakuti udziwa bwanji mkazi iwe, ngati udzapulumutsa mwamunayo: kapena udziwa bwanji, mwamuna iwe, ngati udzapulumutsa mkazi? (1 Akolinto 7:16)**

Popereka uphungu funso limafusidwa ngati nkazi amene akuzunzidwa ndi mwamuna wake kapena kuzuza ana akuyenerabe kukhala ndi iye. Ngati kuzunza kuli kugonana, ichi ndi chimasomaso ndipo ali ndi chifukwa monga mwa malembo kuthetsa banja. Koma nanga kunzuza kwa pathupi…..Mwachitsanzo, kumenya?

Mau a Mulungu amanena kuti thupi ndi “nyumba ya Mzimu Woyera”. Umenewu ndi wa Mulungu, ndipo aliyese amene adetsa kachisi, Mulungu adzamuwononga iye. Pamene nkazi wakhalabe ndi mwamuna wake amene akumuzuza pomumenya iye ndi ana ake, akuika mwamunayo kuti awonongedwe ndi Mulungu. Akuyenera kudzichotsa yekha ndi ana ake pamaso pake mpaka atapatsidwa malangizo ndikuthetsa vuto lake.

Tagwiritsa ntchito mawu ambiri kuchokera pa 1 Akolinto 7 pa mfundo imeneyi m’chaputalachi. Imani tsopano ndipo werengani chaputala chonse cha 1 Akolinto chimene chikuthana ndi mutu wa kusakwatira ndi mawukwati.

**KUGONJERA**

Pali nkhani zina zambiri m’makalata zimene zimathana ndi ubale pakati pa akazi ndi abambo;

> **Akazi inu, muzimvera amuna anu, monga kuyenera mwa Ambuye. Amuna inu, kondani akazi anu, ndipo musawawire mtima iwo. (Akolose 3:18-19)**
>
> **Akazi inu, mverani amun anu ainu eni, monga kumvera Ambuye.**
>
> **Pakuti mwamuna ndiye mutu wa mkazi, monganso Krsitu ndiye mutu wa Eklesia, ali yekha Mphulumutsi mwa thupilo.**
>
> **Komatu monga Eklesia amvera Khrsitu, koteronso akazi amvere amuna awo m’zinthu zonse.**
>
> **Amuna inu, kondani akazi anu, monganso Khristu anakonda Eklesia, nadzipereka yekha m’malo mwache;**
>
> **Kuti akampatule, atamyeretsa ndi kumsambitsa madzi ndi mau;**
>
> **Kuti iye akadziikire yekhakha Eklesia wa ulemerero, wopanda banga, kapena khwinya, kapena kanthu kotere; komatu kuti akhale woyera, ndi wopanda chilema.**
>
> **Koteronso amuna azikonda akazi awo a iwo okha monga ngati matupi a iwo okha. Wokonda mkazi wa iye yekha adzikonda yekha; Pakuti tiri ziwalo za thupi la che.**
>
> **Chifukwa ichi munthu azasiya atate ndi amai nadzaphatikizana ndi mkazi wache; ndipo iwo awiri adzakhala thupi imodzi.**
>
> **Chisisi ichi nchachikuru; koma ndinena ine za Khristu ndi Eklesia. Komasno inu, yense pa yekhal, yense akonde mkazi wache wa iye yekha, monga adzindona yekha; ndipo mkaziyo akumbukire kuti aziopa mwamuna (Aefeso 5:22-33)**

Nthawi zina ma vesi amenewa amagwiritsidwa ntchito molakwika kuti akakamize azimayi kugonjera. Amuna atha kuyesera kupanga akazi awo kuchita zoipa ponena kuti azimayi akuyenera kuvera. Amaikanso ntchito yambiri ndikuyembekezera kuti azimayi achite ngati antchito kapen akapolo.

Mfundo yowona ya kugonjera imene ikutchulidwa ndi chifanizo cha ubale pakati pa mpingo, umene umatchulidwa kuti mkwatibwi ndi Yesu Khristu. Paulo akunena kuti akuyankhula za ubalewu pa ndime ya 32. Yesu sakanayembekezera kufunsa nkwatibwi kuchita zinthu zosayenera kapena mwamuna kutero.

M'buku la Machitidwe, munaphunzira zimene zinachitika kwa Safila pamene anagwirizana ndi mwamuna wake kuti akhale mbali imodzi ya dongosolo losayenera. Zinthu zimene ziri zosayenera zosiyana ndi malamulo a Mulungu, nkazi sakuyenera kugonjera. Ali ndi udindo kwa Mulungu ndipo adzayankha mulandu.

Paulo akufotokoza zambiri pa Akolose:

**Akazi inu, muzimvera amun aanu, monga kuyenera mwa Ambuye. (Akolose 3:18)**

Mukuyenera kugonjera zinthu zokhazo zovomerezeka pamaso pa Ambuye. Kugonjera kuchita ntchito zoipa siziri "mwa ambuye" ndipo sizoyenera.

Pali mfundo zina zofunika kwambiri zokhudzana ndi ubale pakati pa mwamuna ndi nkazi zimene ndizofanana ndi ubale pakati pa Khristu ndi Mpingo. Mpingo uli pansi pa Yesu mosakakamizidwa. Mwamuna sakuyenera kukakamiza nkaziwake kuti amugonjere. Akuyenera kuvera mosakakamizidwa chifukwa cha Chikondi cha khristu chowonetsedwa ndi mwamuna.

Amuna akuwuzidwanso kuti akonde akazi awo monga Khristu anakonda mpingo. Ngati abambo atakondandi modzipereka monga m'mene Khristu anakondera mpingo, nkazi adzalakalaka kumugonjera ndi kumukondweretsa nkazi wake munzinthu zonse monga m'mene okhulupirira owona amafunira kumukondweretsera.

Kumbukirani: Yesu ali ndi Chikondi chopanda chilema kwa mpingo ngakhale kuti mpingo sumamugonjera ndi Chikondi chanicheni. Mwamuna akuyenera kuwonetsa Chikondi chomwecho kwa nkazi wake ngakhale nkazi samamugonjera bwinobwino. Nkazi amene ndi okhulupirira weniweni, komabe amene mwamuna wake amamukonda chonchi, adzayesetsa kumukonda ndikugonjera utsogoleri wake, monga m'mene amachitira kwa Khristu.

Ndibwino kuvetsetsa kuti nkhani imeneyi sikukamba za ukwati wa mwamuna amene Sali wa umulungu. Ikuyankhula za moyo wa ukwati pakati pa anthu amene anadzazidwa ndi mzimu amene ali ndi ubale wa chilengedwe ofanana ndi umene ulipo pakati pa Khristu ndi mpingo. Paulo akuti ngati munakwatiwa ndi mwamuna wa chikhristu amene ali ndi Chikondi chimenechi kwa inu, pamenepo mukuyenera kumuvera ndi kumugonjera iye.

Mwamuna akuyenera kumuchengetera ndi kumuthandiza nkazi wake chifukwa ali thupi limodzi ndipo onse ndi ziwalo za thupo la Khristu. Nkazi akuyenera kukhala munthu ofunika kwambiri m'moyo wa nkazi. Akuyenera kusiya, bambo ake, amayi ake, ndi zonse ndikuphathikana ndi nkazi wake ngati munthu m'modzi. Akuyenera kukonda nkazi wake ngati m'mene amakondera thupi lake. Izi zimapanga kugonjera ndi mantha kwa iye kosangalatsa kwa nkazi wake. Atha kumugonjera iye monga m'mene angagonjere kwa Ambuye.

Onani ndime yapambuyo pake mu nkhani imene timayiwunika:

> **Ndi kumverana wina ndi mnzache m'kukkopa Khristu. (Aefeso 5:21)**

Okhulupirira, nkazi komanso mwamuna amene ali pabanja, akuyenera kugonjerana ndi kufunitsitsa kukondweretsana mwa Ambuye.

Petro akupereka maganizo ake okhudzana ndi akazi a chipangano chatsopano ndi nkhani ya kugonjera.

> **Pakuti koteronso kale akazi oyera mtima, akuyembekezera Mulungu, anandzikomestera okha, namvera amuna awo a iwo okha; monga Sara anamvera Abrahamu, namucha iye mbuye; ameneyo mukhala ana ache ngatimuchita bwino, osaopa coopsa chiri chonse. (1 Petro 3:5-6)**

Pamene Sarah analankhula mwaulemu ndi Abraham ndikumuvera, sizitanthawuza kuti sanamasuke kupereka maganzo ake. Nthawi ina, pamene anafusa Abraham kuti achotse Ishuael ndipo Abrahamu anakana, Mulungu analankhula ndi Abrahamu:

> **Ndipo Mulungu anati kwa Abrahamu, Usaipidwe nao, chifukwa mnyamatayo, ndi chifukwa cha mdzakazi wako; momwe monse akunenera iwe Sara umvere iwe mau ache; chifukwa kuti mwa Isake zidzaitanidwa mbeu zako. (Genesis 21:12)**

Mulungu anathandiza maganizo a Sarah chifukwa anazindikira Abraham anakakamirabe Ishumael. Dongosolo la Mulungu linali lakuti Isake akhale mlowa m'malo wa chuma cha Abrahamu ndi mwana wa pangano pakati pa iye ndi Abrahamu.

## AZIMAYI

Nkhani zambiri m'makalata zimapita kwa azimayi amene ali ndi ana. Amanena kuti uwu ndi udindo wa azimayi.

## KUCHENGETERA NDI KUSAMALA ANA:

Ku Atesalonika, Paulo akupereka chinthunzithunzi chabwino cha m'zimayi wa chikhristu pamene akuti:

> **Komatu tinakhala ofatsa pakati painu, monga mmene mlezi afukata ana ache a iye yekha; kotero ife poliralira inu, tinavomera mokokondwera kupereka kwa inu si uthenga wabwino wa Mulungu wokha komanso moyo wathu, popeza mudakhala okondwedwa kwa ife. (1 Atesalonika 2:7-8)**

Paulo akufanananitsa utumiki wake ndi chinthunzithunzi cha m'mene mzimayi wa umulungu amachititra posamalira, kuchengetera, kukonda ndi kupereka zofunika kwa ana ake.

**KUKHALA OSUNGA NYUMBA:**

Paulo akuti nkazi atsogolere nyumba ndikukhala osunga pakhomo:

> **Akhale odziletsa, ofatsa ochita m'myumba mwao, koma akumvera amuna aiwo okha kuti mau a Mulungu angachitidwe mwano. (Tito 2:5)**
>
> **Chifukwa chake nditi akwatiwe amasiye ang'ono, nabale ana , naweruzire nyumba, osapatsa chifukwa kwa mdaniyo chakulalatira. (1 Timoteo 5:14)**

Azimyi ena amachita utumiki koma atasiya nyumba zawo zowonongeka ndipo ana awo amasowa chitsogozo. Nthawi zina ana amakhala osaweruzika ndipo mabanja awo anawonongeka.

Ndime zimenezi zikuwonetsa kuti nkazi akuyenera kukhala ndi udindo osunga khomo, mtsogoleri wa ana ndi nyumba yonse. Ngati simungachite izi, zotsatira zake ndikupereka mwayi kwa satana ndyerekezi.

Izi sizitanthawuza kuti azimayi a chikhristu asachite nawo utumiki. Monga munaphuzira kuchokera m'buku la Machitidwe ndi mabuku a Makalata, azimayi apabanja anali ndi mautumiki amene amayendanso bwino. Sibwino kuchitita utumiki wa Chikhritu kapena ntchito iriyonse koma kunyumba kukuvutika sicholinga cha Mulungu.

**KUKHUPHUZITSA ANA AWO CHIKHULUPIRO**

Paulo akukumbutsa Timoteo kuti kuchokera kumwana wake wadziwa malemba" (2 Timoteo

3:15). Akuyamikira amyi ake ndi agogo ake akazi chifukwa cha chikulupiriro chawo (2 Timoteo 1:5). Mzimayi wa chikhristu akuyenera kuphuzitsa mau a Mulungu kwa ana ake. Kuchokera kumbwana, akuyenera kuika mwa iwo chidziwitsso cha Mulungu ndidongosolo lake pa moyo wawo. Chiphuzitso chao chikuyenera kuphatikiza kuwasungitsa ena mwambo monga mwa malamulo a Mulungu ndi dera lomwe mukukhala ndi kulemekeza makolo ndi ena.

**AZIMAYI NDI UBELEKI**

Nkhani ina mbuku la Timoteo ikutanthawuza za azimayi mogwirizana ndi ubeleki:

> **Pakuti Adamu anayamba kulengedwa, pamenepo Heva; ndipo Adamu sananyengedwa, koma mkaziyo ponyengedwa analowa m'kulakwa; (1 Timoteo 2:13-15)**

Ndime zimenezi takambirana kale mokhudzana ndi azimayi kukhala chete mu m'tchalitchi.

Mafuso ena nkhani imeneyi ayima patanthawuzo la kupulumutsidwa kudzera n'kubereka.

Ngakhale kuti tchimo linafika m'dziko lapansi kudzera mwa nkazi, Mulungu anapanga dongosolo lakuti kudzera mwa nkazi Yesu Khristu, mpulumutsi wa tchimo ladziko lonse lapasi akuenera kubwera. Kudzera n'kubereka, mpulumutsi anadza. Dziko lonse lapansi

(kuphatikizirapo nkazi amene anachimwa poyamba) adzapulumutsidwa chifukwa cha kubereka kumenekuku.

Paulo akutsindika ntchito ya m'zimayi yobwerentsa chipulumutso kudziko lapansi:

> **Koma pokwaniridwa nthawi, Mulungu anatuma mwana wake, wobawa ndi mkazi, wobadwa wakuvera lamulo, kuti akaombole iwo akumvera lamulo, kuti ife tikalandire umwana. (Agalatiya 4:4-5)**

Pa nthawi yake Mulungu anagwiritsa ntchito mzimayi kubereka mpulumutsi amene anapanga chothekera kubwezeretsa ubale wabwino ndi iye. Tikamati nkazi adzapulumutsidwa mwakubereka timatanthawuza zimenezi.

Sizimatanthawuza kuti ubereki umapulumutsa mzimayi. Zokhazo zochitika pa nthawi yakubadwa mwatsopano mwa kulapa ndi chikhulululukiro cha machimo zimapulumutsa. Sizimatanthawuzanso kuti azimayi amene ali osabereka sadzapulumutsidwa.

**MALO OSIYANASIYANA AMENE NKHANIYI IMAPEZEKA**

Pali malo osiyasiya m'mabuku a Makalata amene magulu osiyanasiyana a azimayi amapezekeka.

Paulo akulankhula za azimayi opusa:

> **Pakuti mwa iwo akhala akukwawira m'nyumba, nagwira akazi opusa, osenza akatundu a zoipa zao, otengedwa nazo zilakolako za mitutndu mitundu; (2 Timoteo 3:6)**

Kuyang'ana malo amene ndimeyi ikupezeka, Paulo akuchenjeza anthu amene ali nawo mawonekedwe a chipembedzo koma opanda mphavu yake.Amatchula kuti ndi okhulupirira koma samakhala moyo wachiyero kuteteza chipembedzo chawo, amalunjika ndikutsogolera azimayi ofoka ndi osalakwa kuchimo.

Gulu lina la azimayi m'makalata ndi azimayi achikhulupiriro amene ananenedwa pa Ahebri 11.

Izi ndi kuwonjezera azimayi amene analandira akufa awo mwakuka kwa akufa (ndime 35); nkazi wa Abrahamu, Sara (11); ndi Rahabe amene anachereza azondi atalowa mdziko limene Mulungu anawalonjeza. Azimayi onsewa anachitidwa umboni chifukwa cha chikhululpiriro mwa Mululungu.

Paulo akutchula akazi monga mwakuva zowawa za ubereki pofotokoza za chiweruzo pa dziko m'masiku otsiriza:

> **Pamene angonena, Mtendere ndi mosatekeseka, pamenepo chionongeko chabukapo chidzawagwera, monga zowawa mkazi wa pakati ndipo sadzapulumuka konse. (1 Atesalonika 5:3)**

Monga kuwawa kwa ubereki sikothawika pamene nkazi akubereka, momwemonso chiweruzo cha Mulungu pa dziko lochimwa sichothawika.

## MAVALIDWE NDI MACHITIDWE A ZINTHU

Maganizo amene anaperekedwa komaliza m'mabuku a amakalata ndi okhudzana ndi makhalidwe komanso mawonedwe azinthu. Paulo akuti:

> **Momwemonso, akazi adziveke okha ndi chovala choyenera, ndi manyazi, ndi chidziletso; osati ndi tsitsi lache loluka, ndi golidi kapena ngale kapena maraya a mtengo wa che wapatali; (Timoteo 2:9-10)**

Azimayi nthawi ya Paulo anali ndi makozedwe atsitsi ochititsa kaso. Ena amakoza tsitsi ndi ulusi wa golide ndi zibangiri. Paulo sakutsutsa za maonekedwa awo koma kuti zinthu zoyambirira zikuyenera khala poyamba. Akuyenera kutsindika pa ntchito zabwino osati mavalidwe, makozedwe atsitsi ena. Paulo akuperekaso maganizo ake pa zamavalidwe azimayi ndi ndi machitidwe awo:

> **Amene kukometsera kwanu kusakhale kwa kunja, kuluka tsitsi ndi kuvala za golidi, kapena kuvala chovala koma kukhale munthu wobisika wamtima, m'chovala chosaola cha mzimu wofatsa ndi wachete, ndiwo wa mtengo wache wapatali pamaso pa Mulungu. (1 Petro 3:3-4)**

Ndime izi zikufotokozera za maganizo a Paulo. Paulo sakunena kuti kukoza tsitsi ndi kuvala golide ndikolakwika, ndipo sakunenanso kuti kuvala zovala ndi kolakwika monga zanenedwa nkhaniso yomweyo. Akutanthawuza kuti Mulungu amaika chidwi pamakozedwe ankati, antima.

Azimayi ayenera kutsindika kwambiri makulidwe awuzimu kusiyana ndi mwonekedwe akunja. Paulo ndi Petro akulankula za zoyenera kuikidwa patsogolo osati malamulo amene amanena

chimene azimayi ayenera kuvala. Nkhani yaikulu yokhudzana ndi mawonekedwe amene Paulo ndi Petro akuphuzitsa ndi:

1. Mzimayi ayenera kuvala bwino.

2. Akuyenera kutsindika makulidwe awuzimu (munthu wankati wa ntima) kusiyana ndi makozedwe akunja (mawonekedwe akunja).

Tikuyenera kulingaliranso pa mfundo imene Paulo akuphuzitsa pamene akufotokoza zimene tingazitchule kuti "zochitika zopereka mafuso."

Ngakhale Paulo anati nyama itha kudyedwa ndi chiyamiko kwa Mulungu chifukwa chakuti wapereka (Aroma 14), ophunzira ena amene anakhazikika mchikhalidwe cha chiyuda anakhumudwa pamene ophuzira ena amadya nyama. Amatsatirabe malamulo a zaakudya monga mwa chipangano chakale.

Paulo anati pamene anali ndi okhulupilira amenewa, sanadye nyama kuti kapena angakhumudwe ndisalandira utumiki. Azimayi akuyenera kulola kuti maganizo awa awatsogolere pamakhalidwe awo ndi mawonekedwe awo.

Nkhani zose zimene mwaziwerenga zikunena kuti azimayi akhale odekha. Ena akhala akugwiritsa ntchito ndimeyi molakwika pakuika azimayi pamene iwo akufuna. Koma kwa abale amene anali ophunzira Yesu kuti "odala ndi akufatsa". Sitingaganize kuti kufatsa kumeneku ndikofunika kwa azimayi achikhristu okha. Amuna akuyeneranso kuwonetsa kufatsa kumeneku.

Miyambo akunena mwachidule nkhani yose ya mavalidwe ndi machitidwe azinthu pamene akuti:

> **Kukongola kungonyenga, maonekedwe okoma ndi chabe; koma mkazi woopa Yehova adzatamandidwa. (Miyambo 31:30)**

## MAFUSO ODZIFUSA NOKHA

1. Lembani ndime yotsogolera.

______________________________________________________________________________

______________________________________________________________________________

2. Ndi ubwino uti okhala osakwatira umene Paulo akunena pa 1 Akolinto 7:35?

______________________________________________________________________________

3. Werengani ziganizo zili m'musimu. Ngati chiri chowona lembani T ngati chiri chabodza lembani F kunsi kwa m'munzere umene uli koyambirira.

a._____Paulo amakhulupirira kuti kukwatira ndi chinthu cholakwika.

b._____Azimayi amasiye amene apanga pangano losakhala pa banja akuyenera kukhala a zaka zosachepera 60.

c._____ Ngati mwamuna wankazi ndi osakhulupirira akufuna kukhalabe ndi nkaziwake akuyenera kuchita choncho.

d._____Azimayi akulu nsinkhu akuyenera kuphuzitsa azimayi ang'ono.

e._____Kugonjera pakati pa nkazi ndi mwamuna ndi ubale umene umakhalapo pakati pa Yesu ndi mpingo.

f._____Azimayi akuyenera kugonjera kwa amuna awo, ngakhale atafunsidwa kuchita chinthu choyipa.

g.____ Amuna ndi azimayi akuyenera kugonjerana.

h._____ Mkazi akuyenera kukhala ndi mwana kuti apulumutsidwe mwa kubereka.

4. Lembani mfundo ziwiri zimene Paulo ndi Petro anaphuzitsa pa za mawonekedwe azimayi.

______________________________________________________________________________

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto m'chaputala chomaliza m'bukuli.)

## KUPHUNZIRA ZAMBIRI

Chaputalachi chikumalizitsa phunziro la azimayi m'mabuku a makalata.

M'chaputala 10,  ndandanda wa malo onse amene nkhani ya amayi m'makalata imapezeka unaperekedwa mgawo la "kuphunzira zambiri". Ngati munamalizitsa phunziloli, zikutanthawuza kuti muli ndi chimangirizo chokhudzana ndi azimayi m'mabuku amenewa.

Panopa mutha kufuna kuphunzira zambiri m'malo ena amene mungafune. Ngati ziri choncho, pezani mutu umene ungakusangalatseni. Mwachitsanzo, mukhoza kukhala osangalatsidwa kuwerenga nkhani zonse zimene mwasankha. Iyi ndi njira imodzi yowerengera Baibulo imene imatchulidwa kuti "njira yolondola mutu" chifukwa imalondola zimene Baibulo likunena pa mutu umodzi.

## CHAPUTALA 12

## MALO ANU MU UTUMIKI

**Zolinga:**

Mukamaliza chaputalachi muyamba kuchita izi:

1. Kulemba ndime yotsogolera.

2. Kupeza mphatso ya uzimu.

3. Kuzindikira kuti muli ndi mphatso imodzi kapena kuposera apo za uzimu.

4. Kuzindikira kuti muli ndi mphatso ya uzimu.

Ndime yotsogolera: (cholinga cha mphatso za uzimu)

> **Kuti akonzere oyera mtima; ku ntchito ya utumiki, kumangirira thupi la khristu; (Aefeso 4:12)**

### MAU OYAMBA

Pamene ziri zosangalatsa kuphuzira mbali azimayi mumpingo oyambirira, pali cholinga chachikulu kupatula kuphunzira ndi kungodziwa zinthu chabe. Cholinga chake ndi kudziwa mbali yanu yawutumiki mu nthupi la Khristu.

Mzimayi aliyese ali ndi utumiki wake mumpingo. Mphatso za uzimu zimathandiza azimayi kuti akwaniritse utumiki umenewu. Phunziro iri ndi lofunika kwambiri kufikira kuti phunziro pa mutuwu linakhazikitsidwa ku Harvesti International Institute. Pamene sitingakwanitse zonse m’chaputala chimodzi zipangizo zonse m’maphuziro a “Utumiki wa mzimu woyera,” phuziro iri liwonetsa Mphatso za uzimu, kukuthandizani kuti inu muli ndi mphatso imodzi kapena zoposera apo, ndikukuthandizani kuzindikira mphatso.

### MZIMU WOYERA

Nthawi imene Yesu anauka kwa akufa koma asanapite kumwamaba, anapereka malangizo ofunika kwa omutsatira:

> **Ndipo onani, ie nditumiza p ainu lonjezsano la Atate wanga; koma khalani inu m’mudzi muno, kufikira mwavekedwa ndi mphavu yochokera kumwamba. (Luka 24:49)**

Lonjezo limene Yesu amatanthawuza ndi Mzimu Woyera, Yesu analankhulapo kale za ichi kwa ophunzira ake;

> **Ndipo ine ndizapempha Atate, ndipo adzakukpatsani inu nkhoswe yina, kuti akhale ndi inu ku nthawi yonse,**
>
> **Ndiye Mzimu wa choonadi; amene dziko lapansi silingathe kumlandira, pakuti silimuona iye, kapena kumzindira iye. Inu mumzindikira iye; chifukwa akhalandi inu nadzakhala mwa inu.**
>
> **Sindidzakusiyani inu mukhale ana amasiye; ndidza kwa inu. (Yohane 14:16-18)**

Yesu khristu adzakhala wotonthoza, mphavu yakutsogolera, ndi mphuzitsi. Mzimu woyera udzakhala ndi ntchito zambiri, chofunika kwambiri ndi ku kukhala ndi mphavu yolalikira uthenga wabwino:

> **Komatu mudzalandira mphavmvu, Mzimu woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekero ache a dziko. (Machitidwe 1:8)**

Kutsatira malangizo a Yesu Khristu, okhulupirira anadikirira Mzimu woyera ku Yerusalemu. Werengani Machitidwe 2 pa nkhani yakubweranso kwa Mzimu woyera.

## MPATSO ZA MZIMU WOYERA

Yesu anawasiya ophuzira ake ndi ntchito yofikitsa uthenga wabwino kumalekezero adziko lapasi. Mphavu ya Mzimu Woyera inali mphatso yapadera imene inapatsidwa kwa okhulupirira kuti iwakozekeretse kutumikira ena.

## KODI MPHATSO ZA UZIMU NDI CHANI?

Mau akuti "uzimu" atanthawuza "kudziwika kapena kulamulidwa ndi mzimu woyera." Mphatso ndi chinthu chimene chimapatsidwa kwa ulele kuchokera kwa munthu kupita kwa wina. Mphatso ya mzimu ndi kuthekera kumene okhulupirira amapatsidwa ndi mzimu woyera kuti atumikire ngati mbali imodzi ya thupi la Khristu.

Pali kusiyana pakati pa mphatso za mzimu woyera ndi chipatso cha mzimu woyera. Mphatso za mzimu woyera zinachitika pa pentekoste (machitidwe 2) pamene mzimu woyera anafika potsatira lonjezo la khristu.

> **Ndipo ine ndidzapempha Atate, ndipo adzakupatsani inu Nkhoswe yina, kuti akhale ndi in ku nthawi yonse,**

**Ndiye Mzimu wa choonandi amene dziko lapansi silingathe kumlandira, pakuti silimuona iye, kapena kumzindikira iye. (Yohane 14:16-17[a])**

Mphatso ya Mzimu inaperekedwa kale poyankha lonjezo. Mphatso za mzimu woyera ndikuthekera kumene mzimu woyera amapereka kwa okhulupirira kuti ntchito igwirike bwino.

**Ndipo iwowa anaturuka, nalalikira ponse ponse, ndipo Ambuye anachita nao pamodzi, natsimikiza mawu ndi zizindikilo zakutsatapo (Marko 16:20) MPHATSO NDI MALUSO**

Pali kusiyana pakati pa mphatso za uzimu ndi maluso achilengedwe. Luso ndi kuthekera kwa chibadwidwe kumene munthu amatenga pobadwa ndipo kumakula akamachitachita. Mphatso ya mzimu ndi kuthekera kwa uzimu kumene sikumabwera pobadwa kapena kuyeserera. Ndikuthekera kwinakwake kopatsidwa ndi mzimu woyera kuti kumagwiritsidwa ntchito pa zolinga zinachake.

Ndizotheka kuti luso la chilengedwe likhoza kuvomerezedwa ndi kudalitsidawa ndi mzimu woyera pamene wina wakhala mkhristu. Izi zikachitika luso limakhala mphatso komanso luso. Mwachitsanzo, munthu atha kukhala ndi luso lachibadwidwe la utsogoleri chikufukwa cha maphuziro amene wapatsidwa. Atabatizidwa ndi mzimu woyera, luso limeneri

likhozakuvomerezedwa ndi mzimu woyera ndipo likhozakugwiritsidwa ntchito ngati mphatso ya utsogoleri.

Mphatso za uzimu zimabweretsa kuthekera kwa uzimu kwa kukulu kusiyana ndi maluso achibadwidwe. Ngakhale mukuyenera kugwiritsa ntchito maluso anu onse pogwira ntchito ya ambuye, ndizofunikabe kuti mukhale ndi mphatso za uzimu.

**Kuti akonzere oyera mtima; ku nchito ya utumiki, kumangirira thupi la Khristu;**

**Kufikira ife tonse tikafikira ku umodzi wa chikhulupiriro, ndi wa chizindikiritso cha Mwana wa Mulungu, kwa munthu wangwiro, ku muyeso wa msinkhu wa chidzalo cha Krsitu.**

**Kuti tisakhalesnso makanda, ogwedezekagwedezeka, natengeka-tengeka ndi mphepo yonse ya chiphunzitso, ndi tsenga la anthu, ndi kuchenjerera kukatsata chinyengo cha kusochoretsa;**

**Koma ndi kuchita zona mwa Chikondi tikakule m'zinthu zonse, kufikira iye amene ali mutu ndiye Khrsitu. (Aifeso 4:12-15)**

Malingana ndi nkhani imeneyi, zolinga za mzimu woyera ndi:

-Kuyeretsa oyerera ntima

-Kupititsa patsogolo ntchito ya Mulungu.

-Kutsitsimutsa Khristu ndi Mpingo

Masophenya kapena zolinga za mphatso za uzimu ndi:

-Kukhala amodzi m'chikhulupiriro.

-Kukuza chidziwitso chathu mwa khristu.

-Kukula m'chiyero, potsatira Yesu Khristu ngati chitsanzo chathu.

-Kukhala okhazikika, osanamizidwa ndi ziphuzitso zonyenga.

-Kukula muzimu mwa khristu.

## MAPEREKEDWE A MPHATSO

Okhulupirira aliyese ali ndi Mphatso yosachepera imodzi:

> **Monga yense walandira mphatso, mutumikirane nayo, ngati adindo okoma a chisomo cha mitundu mitundu cha Mulungu; (1 Petro 4:10)**

Koma chiwonetsero cha mzimu chinaperekedwa kwa munthu aliyese, kuti chipindule.

> **Koma kwa yense kwapatsidwa maonekedwe a Mzimu kuti apindule nao.**
>
> **Koma zonse izi achita Mzimu m'modzi yemweyo, nagwira yense payenkha monga afuna. (1 Akolinto 12: 7,11)**

Chifukwa chakuti okhulupirira aliyese ali ndi Mphatso yosachepera imodzi ya Mzimu, tonse tiri ndi udindo wozindikira ndi kugwiritsa ncthito Mphatso yathu. Simudzaweruzidwa chifukwa cha chiwerengero cha Mphatso zimemene mulinazo. Mudzaweruzidwa ndi kukhulupirika kwanu pogwiritsa ncthito Mphatso ya uzimu imene munapatsidwa. Faninzo la matalente pa Mateyu 25:14-30 ikutsimikiza chowonadi chimenechi.

Pali mpatso zambiri za m'zimu, koma palibe okhulupirira amene ali ndi mphatso zonse:

> **Kodi ali onse atumwi? Ali aneneri onse kodi? Ali aphuztsi onse? Ali onse achita zozizwa?**
>
> **Ali nazo mphatso za machiritso onse kodi? Kodi onse alankhula ndi malilime? Kodi onse amasulira mau? (1 Akolinto 12:29-30)**

Munthu atha kukhala ndi Mphatso zopitilira imodzi, koma palibe munthu ali ndi mpatso zonse. Akanakhala kuti alipo, sakanafuna ena m'nthupi la Khristu.

## MPHATSO ZAMBIRI KUCHOKERA MALO AMODZI

Baibulo limati pali mpatso zambiri zimene zimachokera malo amodzi. Kochokera mpatso za uzimu ndi Mzimu Woyera. Iyeyo Amapereka ndikugwira ntchito m'mitima ya okhulupirira:

> **Pakuti sindidziwa kanthu kakundiparamulitsa; koma m'menemo sindiyesedwa wolungama; koma wondiweruza ine ndiye Ambuye.**
>
> **Chifukwa chake musaweruze kanthu isanadze nthawi yache, kufikira akadze Ambuye, amenenso adzaonetsera zobisika za mdima, nadzasonyeza zitsimikizo za mtima; ndipo pamenepo yense adzakhala nawo uyamiko wache wa kwa Mulungu.**
>
> **Koma izi, abale, ndadziphiphiritsira ndekha ndi Apolo, chifukwa chainu kuti mwa ife mukhaphunzire kusapitirira zimene zilembedwa; kuti pasakhale m'modzi wodzitukumulira mnzache ndi kukana wina.**
>
> **Pakuti akusiyanaitsa iwe ndani? Ndipo Uli nacho chiani osati wacihlandira? Koma ngati wachilandira udzitamandida bwanji, monga ngati sunachilandire? (1 Akolinto 4:4-7)**
>
> **Ndipo pokhala ife ndi mphatso zosiyana, monga mwa chisomo chopatsidwa kwa ife, kapena mphatso yakunenera, tinenere monga mwa muyeso wa chikhulupiriro;**
>
> **Kapena ya kutumikira, tidzipereke kuti utumiki uwu; kapena iye wakuphunzitsa, kukuphunzitsa;(Aroma 12:6-8)**

Ngakhale kuti mphatsozi ndi zosiyanasiyana koma zimachokera malo amodzi. Palibe Mphatso yofunika kwambiri kusiyana ndi inzake. Mbali yanu m'nthupi la Khristu imafanizidwa ndi ziwalo za thupi la muthu. Monga thupi la muthu, ziwalo zing'onozing'ono monga maso, ali ndi ntchito yaikulu, zowoneka Mphatso zazing'ono ndizofunika kwambiri kuti mpingo ugwire ntchito. Mphatso zina zimakhudzana ndi udindo wawukulu, koma palibe mpatso yosiyana ndi inzake.

## ADINDO A MPHATSO

Ndinu adindo chabe a Mphatso za uzimu. Mdindo ndi amene chimene akuchigwiritsa ntchito sichake. Amagwiritsa ntchito chinthu chopatsidwa ndi munthu wina kuti chipindulire munthu amene anamupatsa:

> **Chotero munthu atiyese ife, monga atumiki a Khristu, ndi adindo a zinsinsi za Mulungu. (1 Akolinto 4:1)**

Mbali ina ya chinsisi imene inu muli adindo ndi mphatso. Zinapatsidwa kwa inu ndi mzimu woyera kuti zimutumikire bwino Yesu:

> **Monga yense walandira mphatso, mutumikirane nayo, ngati adindo okoma a chisomo cha mitundu mitundu cha Mulungu; (1 Petro 4:10)**

Ngati adindo mudzaweruzidwa potengera kukhulupiriraka kwanu pogwiritsa ntchito mpatso zimene mwapatsidwa:

> **Komatu pano pafunika za adindo, kuti munthu akahale wokhulupirika. (1 Akolinto 4:2)**

## MPHATSO ZA MZIMU

Nkhani ya mphatso za mzimu imapezeka kwambiri m'mabuku awa Aroma 12:1-8, 1 Akolinto 12:1-31, Aefeso 4:1-16, ndi 1 Petro 4:7-11. Kumbukirani kuti mphatso za Mzimu ndi kuthekera kochokera kwa Mulungu kopatsidwa kuti mutumikire njira zosiyanasiyana. Pamene patha kukhala maumboni a izi m'miyoyo yanu sizitanthawuza kuti tiri ndi mphatso ina yake. Mwa chitsanzo, okhulupirira onse akuyenera kupereka kuntchito ya Mulungu ndi chakhumi komanso chopereka, koma mphatso ya kupereka ndi kupereka mowolowa manja kodabwitsa kumene kumayambitsidwa ndi mzimu woyera.

Kuti timphuzire bwino tagawa mphatso m'magulu okwanira anayi:

-Mphatso yapadera

-Mphatso yolankhula

-Mphatso yakutumikira

-Mphatso yopanga zodawitsa.

Baibulo silimapereka magawo amenewa. Izi zachitika kukuthandizani kuti muzikumbukira mphatso zosiyanasiyana mosavuta.

### MPHATSO YAPADERA:

Gulu loyambirira la mphastso za uzimu ndi mphatso za padera. Tikugwiritsa ntchito mutuwu pa mphatso zimenezi chifukwa chakuti iriyonse ndi udindo wapadera mumpingo. Mphatso zapadera za utsogoleri ndi:

**Atumwi:**

Ntumwi ndi munthu amene ali ndikuthekera koyambitsa mipingo yatsopano m'madera ndi m'malo a zikhalidwe zosiyanasiyana ndi kuyang'anira mipingo ingapo ngati mtsogoleri. Ntumwi atanthawuza "kupereka ntchito, amena anatumidwa ndi mphavu ndi ulamuliro kukachita zinthu m'malo mwa wina." Ntumwi ali ndi ulamuliro wa padera kapena kuthekera kotumiza uthenga padziko lonse lapansi pokozanso magulu okhazikika awokhulupirira. Maina atsopano amene amagwiritsidwa ntchito m'malo mwa ntumwi ndi ofalitsa kapena odzala mipingo.

**Aneneri:**

Pali mphatso ziwiri za uneneri. Ina ndi mphatso yapadera yakukhala m'neneri. Ina ndi mphatso yolakhula. Mwachidule, uneneri umatanthawuza kuthekera kwa padera kolandira ndi kunena uthenga wa Mulungu kwa anthu ake kudzera m'mayankhulidwe odzozedwa. Mneneri ndi ntsogoleri mu tchalitchi komanso amakhala ndi mphatso yolankhula uneneri.

**Mlaliki:**

Mlaliki ali ndi kuthekera kogawa uthenga ndi anthu osakhulupirira mwa njira yakuti anthu amachitapo kanthu ndikukhala ma membala odalilika a mpingo wa Mulungu. Mau akuti olalikira atanthawuza "amene ambwera ndi uthenga wabwino."

**Abusa:**

Azibusa ndi atsogoleri amene kwa kanthawi amakhala ndi ntchito yoyang'anira moyo wauzimu wa gulu la anthu. Mwawuzimu, abusa amasamalira amene ali pansi pa ulamuliro wawo, kuwaphuzitsa mau a Mulungu ndi kuwatumikira pa zosowa zao za uzimu.

**Aphuzitsi:**

Aphuzitsi ndi anthu amene ali ndi kuthekera fotokoza mawu a Mulungu mwa njira yakuti ena amaphuzira ndikuwagwiritsa ntchito. Mphatso yakukhala mphuzitsi imasiyana ndi yolankhula mwauphuzitsi monga mphatso ya uneneri imasiyana ndi mphatso yakungonenera chabe. Okhulupirira onse sali ndi mphatso yakumphuzitsa kapena yakulankhula ngati aphunzitsi, koma akuyenera kutengapo mbali pogawana uthenga ndi ena. (Ahebri 5:12)

**MPHATSO ZA KULANKHULA**

Mphatso zokwanira zisanu zapatsidwa mutu wakuti mphatso zakulankhula chifukwa zimakhudzana ndi kulankhula mokweza. Mphatso zakulankhula ndi:

**Uneneri:**

Munthu amene ali ndi mphatso yakulankhula ndi chilimbikitso chapadera cha Mulungu kuti anene uthenga watsopano kwa anthu ake. Mphatso yakulankhula mwa uneneri yokha

sitanthawuza kuti muli ndi mphatso yapadera yakukhala m’neneri. Mulungu anaika aneneri (amene aliso ndi mphatso ya uneneri) m’maudindo ena mumpingo. Anthu amene ali ndi mphatso yakuyankhula mau a uneneri Sali ndi mphatso yawutsogoleri. Amangopereka uthenga wapadera motsogozedwa ndi mzimu woyera.

**Kuphuzitsa:**

Monga mwa chitsanzo cha aneneri, mphatso yakulankhula ngati mphuzitsi simatanthawuza kuti munthu ali ndi mphatso yapadera ya kukhala mphuzitsi. Mulungu anaika aphuzitsi (amene aliso ndi mphatso yakulankhula mwa uphuzitsi) m’maudindo apadera m’ntchalitchi. Mphatso yakulankhula mwa uphunzitsi imakhudzana ndi kunena mau a Mulungu koma sizitanthanthawuza kukhudzana ndi utsogoleri mu’mpingo.

**Chilimbikitso:**

Mphatso yakulimbikitsa imatanthawuza kusendera chifupi ndi munthu pa nthawi imene ali ndi zosowa, kupereka uphungu molondola ndi mawu a Mulungu. Kulimbikitsa kumatanthawuza “kuitana munthu pambali”, kupereka malangizo, kuvomereza, kulimbikitsa, kutonthoza komanso ku tsitsimutsa. Kulimbikitsa ndi kupereka upangiri mwa nzeru za uzimu. Anthu amene ali ndi mphatso imeneyi amatumikira mawu a chitonthozo, chilimbikitso, munjira yakuti ena amathandizika. Nthawi inu anthu amenewa ali ndi mphatso ya ulangizi.

**Mau a Nzeru:**

Mau anzeru ndi kuthekera kokhala ndi maganizo akuti nzeru ingagwiritsidwe ntchito bwanji ku zofunika zapadera za anthu. Mutapatsidwa mfundo munyengo iriyonse, munthu wa mphatso imeneyi amadziwa kugwiritsa ntchito mfundo kuti abweretse yankho la nzeru.

Mau anzeru ndi maganizo a umulungu kwa anthu ndi nyengo zao zimene siziri za chizolowezi kwa anthu wamba. Nzeru zimenezi nzochokera kwa Mulungu zimaphatikidwa ndi chidziwitso chakuti ndingachite chani nanga ndingachite bwanji. Mphatso iyi simatchiludwa kuti “mphatso ya nzeru” chifukwa simampatsa munthu nzeru zonse za Mulungu. Ndi mawu a nzeru, gawo chabe la nzeru za Mulungu. Mphastso ya mau a nzeru simabwera chifukwa cha maphuziro. Kumene imachokera ndi kwa Mulungu.

**Mau a chidziwitso:**

Mau a chidziwitso ndi kuthekera kovetsetsa zinthu zimene anthu ena samazidziwa ndipo sangathe kuzivetsetsa ndikugawana ndi anthu motsogozedwa ndi chilimbikitso cha mzimu.

Monga mawu a nzeru, simatchulidwa kuti “mphatso ya chidziwitso.” Ndi mphatso ya mau a chidziwitso chifukwa ndi kagawo chabe ka chidziwitso cha Mulungu. Mphatso ya mau a

chidziwitso ndi mau a chivumbulutso. Ndi chidziwitso chowululidwa ndi Mulungu, osati kukhala nacho chifukwa cha maphuziro kapena kuwerenga.

## MPATSO ZA UTUMIKI:

Pali mphatso zokwanira zisanu ndi zinayi zimene tizitchula kuti mphatso zotumikira. Mphatso izi zimatumikira mu mpingo popereka magawo, kuika zinthu m'malo mwake, ndikuthandiza mbali zonse za uzimu komanso zochitika zina. Mphatso za utumiki ndi monga:

### Kuzindikira mizimu:

Kuzindikira mizimu ndi kuthekera kopanga kawuniuni wa anthu, zimphuzitso, ndi nyengo kuti ngati ziri za Mulungu kapena Satana. Mphatso yakuzindikira mizimu sikuyenera kufananizidwa ndi mzimu wakutsutsa. Mphatso iyi ndi ya uzimu ndipo zinthu za uzimu sizimazindikiridwa ndi maganizo amunthu.

Mphatsoyi ndi kuzindikira mizimu, sikungo zindikira chabe. Mphatso iyi imatumikira mumpingo pozindikira anthu amene amene atha kugwa chiyanjano ndi zolinga zoipa, ziphuzitso ndi mawonedwe azinthu olakwika.

### Utsogoleri:

Mphatso ya uzimu ya utsogoleri ndi kuthekera kopanga masomphenya mongwirizana ndi zolinga za Mulungu ndikuwafotokoza kwa ena. Munthu wa mphatso imeneyi amalimbikitsa ndikutsogolera anthu kuti akwaniritse masophenya kulemerero wa Mulungu.

### Kuyang'anira zinthu:

Mphatso ya kuyang'anira zinthu imatchulidwa kuti "ulamuliro" m'Baibulo. Muthu wa mphatso ya kuyang'anira zinthu ali ndi kuthekera kotsogolera, kuika zinthu m'malo ndi kupanga zisankho m'malo mwa anzake. Tanthawuzo la mau akuti ulamuliro limafanana ndi tanthawuzo la mawu akuti oyendetsa sitima. Mau ofanana choncho agwiritsidwa ntchito m'baibulo.

Munthu wa mphatso imeneyi ali ndi udindo wakutsogolera ndi kupanga zisankho. Monga oyendetsa sitima sangakhale mwini wake wa ngalawa, koma anamudalira ndi udindo woyitsogolera paulendo.

Mphatso ya utsogoleri ndi kuyang'anira zinthu imakhudzanso kuika zinthu m'malo mwake zimene zimapangitsa kukwaniritsa cholinga cha uzimu. Nthawi zambiri okhulupirira atha kukhala ndi mphatso zonse ya utsogoleri ndi yakuika zinthu mchimake pamodzi.

Ngati munthu ali ndi mphatso yakuyang'anira zinthu koma alibe mphatso ya utsogoleri, afunika munthu wa mphatso ya utsogoleri kuti agwire naye ntchito. Munthu wa mphatso ya kuyang'anira zinthu ali ndi kuthekera kotsogolera, kuika zinthu m'malo, ndikupanga zisankho, koma opanda

mphatso ya utsogoleri Sali ndi kuthekera kolimbikitsa ndi kugwira ntchito  ndi anthu kuti akwaniritse zolinga zake.

**Chikhulupiro:**

Munthu wa mphatso ya chikhulupiro ali ndi kuthekera kwa padera kokhulupirira ndi kulimbika ntima ndikudalira Mulungu nthawi ya zovuta. Amagwiritsa ntchito chikhulupiro ngakhale pamene okhulupirira ena sangakwanitse. Baibulo limaphuzitsa kuti munthu aliyese ali ndi mulingo wina wa chikhulupiriro opatsidwa ngati mphatso (Aroma 12:13b). Limaphuzitsanso kuti tinaphulumutsidwa kudzera mwa chikhulupiriro (Aifeso 2:8). Koma mphatso ya chikhulupiro ndi kuthekera kwina kwapadera kokhulupirira Mulungu ku mbali zonse za moyo. Chikhulupiriro ichi chimakhulupirira kuti zonse ndi zotheka ndipo sichimamuyikira malire Mulungu.

**Kupereka:**

Munthu wa mphatso yakupereka ali ndi kuthekera kwa padera kopereka zinthu ndi chuma ku ntchito ya Ambuye. Mphatso yakupereka imakhudzanaso ndi kupereka nthawi, mphavu, ndi maluso ku ntchito ya Ambuye.

**Chithandizo:**

Munthu wa mphatso yakuthandiza ali ndi kuthekera kothandiza ena pa ntchito ya Ambuye, kuwathandiza kuti kulitsa magwiridwe abwino a ntchito mphatso zao za uzimu. Kuyambira mdindo kufikira kwa oyimba, chilichonse chothandizira magwiridwe a ntchito mutumiki chikhoza kutengedwa mphatso yothandiza.

**Kutumikira:**

Mau akuti kutumikira pa Aroma 12:7 amatanthawuza **"utumiki".** Kutumikira kumasiyana ndi kuthandiza kufikira kuti kumachepetsa ntchito ya wina wake. Amene akutumikira amatenga udundo wa ntchito ina kupepuza munthu wina kuchita zinthu.

**Chifundo:**

Chifundo chitanthawuza "kukhudzika". Munthu wa mphatso ya chifundo amakhala ndi kukhudzika kwina kwake ndi anthu amene akuvutika ndi kuthekera kowathandiza.

**Kuchereza:**

Mphatso ya kuchereza ndi kuthekera kwa padera kumene Mulungu amapereka kwa ma membala ena mu nthupi la khristu kuti apereke chakukudya ndi malo ogona kwa amene akuzifuna.

**Mphatso ya zizindikiro:**

Pali mphatso zinayi zimene zimatchulidwa kuti zizindikiro chifukwa ndi zizindikiro zakuti mphavu ya Mulungu ikugwira ntchito kudzera mwa okhulupirira ndi cholinga chakuti athu atsimikize mau ake. Mphatso za zizindikiro ndi:

**Zodabwitsa:**

Kudzera mwa munthu wa mphatso ya zodabwitsa Mulungu amachita zinthu zamphavu zimene zimadutsa kuthekera kochitika pa chilengedwe. Zochitika zimenezi ndi zizindikiro zakuti phavu ya Mulungu ndi yaikulu kusiyana ndi ya Satana,  ndipo Mulungu amapatsidwa ulemerero.

**Machilitso:**

Okhulupirira amene ali ndi mphatso ya machilitso ali ndi kuthekera koti mphavu ya Mulungu imayenda kudzera mwa iwo kubwezeretsa mphavu, thazi pakugwiritsa ntchito njira za chilengedwe.

**Malilime:**

Mphatso ya malilime ndi kuthekera  kolandira ndikugawa uthenga ochokera kwa Mulungu kupita kwa anthu ake kudzera m'chilankhulo chimene sanaphunzire. "Malililime" akutanthawuza zilankhulo. Chifukwa chimene tatchulira mphatsoyi zizindikiro osati mphatso yakuyankhula ndi chakuti Baiblo limati mphatsoyi imaperekedwa kuti ikhale chizindikiro.

Pamene wina alankhula m'malilime zitha kukhala mzilankhulo zodziwika ndi zozindikirika ndi anthu:

> **Koma pochitika mawu awa, unyinji wa anthuunasokhana, nusokonezedwa, popeza yense anawamba alikulankhula m'chilankhulidw chake chai ye yekha;**
>
> **Ndipo anadabwa onse, naziza nanena, Taonani, awa onse alankhulawa Sali Agalileya kodi?**
>
> **Ndippo nanga ife timva bwanji, yesne m'chilankkhulidwe chathu chimene tinabadwa nacho? (Machitidwe 2:6-8)**

Zitha kukhalaso mzilankhulo zosadziwika kwa anthu. Izi zimadziwika kuti kulankhula m'malilime osadziwika:

> **Pakuti iye wakulankhula lilime salankhula ndi anthu, koma ndi Mulungu; pakuti palibe munthu akumva; koma mumzimu alankhula zinsinzi. (1 Akolinto 14:2)**

Kulankhula malilime ndi chizindikira cha kunja chakubatizidwa ndi mzimu woyera. Koma chochitika ichi chakulankhula malilime ndichosiyana ndi mphatso yakulankhula malilime. Mphatso ya malilime  ndi kuthekera kwapadera kopereka uthenga ochokera kwa Mulungu kupita ku mpingo munchilankhulo chosadziwika ndi amene akulankhula.

**Kutanthawuzira malilime:**

Mphatso yakutanthawuzira malilime ndi kuthekera kwa padera kodziwitsa anthu m'chilankhulo chodziwika ndi overa uthenga olankhulidwa m'malilime. Kutanthawuziridwa kwa uthenga m'malilime amapereka ndi mzimu woyera ndi ena amene ali ndi mphatso ya uzimu.

Sizimatanthawuziridwa podziwa chilankhulo chimene uthenga waperekedwera. Umaperekedwa mwa vumbulutso lochokera kwa mzimu woyera.

## KUZINDIKIRA MPHATSO YANU YA UZIMU

Ngati simukudziwa mphatso yauzimu imene Mulinayo, tikupereka maganizo kuti muyambe phunziro ku Harvestime Institue lotchedwa "Utumiki wa mzimu woyera." Iidzakutengerani ku mdondomeko izi pokuthandizani kuti muzindikire mphatso zanu.

### NDONDOMEKO YOYAMBA: KUBADWA MWATSOPANO.

Mukuyenera kubadwa mwatsopano kuti mulandire mphatso za uzimu. Zimachokera kukubadwa mwatsopano monga maluso achibadwidwe amabwera pamene anthu abadwa:

> **Koma Petro anatikwa iwo, Lapani, batzidwani yense wainu m'dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhulupiriro cha machimo anu; ndipo mudzalandira mphatso ya mzimu woyera. (Machitidwe 2:38)**

### NDONDOMEKO YA CHIWIRI: KULANDIRA UBATIZO WA MZIMU WOYERA.

Ndondomeko zakuti izi zingachitike bwanji zaperekedwa mphuziloli pa "Utumiki wa mzimu woyera"

### NDONDOMEKO YA CHITATU: KUDZIWA MPHATSO ZA MZIMU.

Ngati simungadziwe mphatso za mzimu zimene ziripo simungazizindikire zimene Mulungu wakupatsani. Pangani kawuniwuni wa matanthawuzo amene mwapatsidwa mphuziloli ndipo/ pitilizani kuphuzira mphuziro la "Utumiki wa Mzimu Woyera."

**NDONDOMEKO YA CHINAYI: ONANI ZITSANZO ZA MPHATSO.**

Mukamaganizira ntundu wamphatso zimenene mutha kukhala nazo, ndibwino kuwonanso chitsanzo cha mphatso zosiyanasiyana. Chitsanzo chogwirika ndi cha okhulupirira amene wakhala akugwiritsa ntchito mphatso yake kwa nthawi yaitali.

**NDONDOMEKO YA CHISANU: FUNANAI MPHATS ZA UZIMU.**

Baibulo limatiwuza kuti tifune mphatso za uzimu:

> **Koma funitsitssani mphatso zoposa. Ndipo ndikuonetsani njira yokoma yoposatu. (1 Akolinto 12:31)**

**NDONDOMEKO YA CHISANU NDI CHIMODZI: KUSANJIKA MANJA.**

Funani atsogoleri awuzimu kuti akusanjikeni manja ndikukupemphererani kuti Mulungu awonetse mphatso yanu ya uzimu.

> **Pakuti cholengedwa chonse cha Mulungu nchabwino, ndipo palibe kanthu kayenera kutayika, ngati kalandiridwa ndi chiyamiko. (1 Timoteo 4:14)**

**NDONDOMEKO YA CHISANU NDI CHIWIRI: PANGANI KAWUNIWUNI WA MPHATSO IMENE MUMAFUNA.**

Dera limene mumasangalala mukamatumikira Mulungu ndi dela lilmene anakudalitSani nalo. Mukuyenera kukhala ndi chilakolako kapena kukhudzika ndi utumiki winawake kuti mutumikire bwino.

**NDONDOMEKO YA CHISANU NDI CHITATU: KAWUNIWUNI WA MTSOGOLERI WA CHIKHRISTU.**

Fusani mtsogoleri wa uzimu kuti awunike kuthekera kwanu kwa uzimu. Gwiritsani nthito uthenga ndi malangizo mphuNziro pa “Utumiki wa Mzimu Woyera.”

**NDONDOMEKO YA CHISANU NDI CHINAYI: UNIKANU NTCHITO YANU YA UZIMU YAKALE.**

Unikani utumiki wanu wakale wa chikhristu. Ndi magawo oti amene mwatumikirapo? Munapambana magawo at? Ndimagawo ati amene anadzetsa chimwemwe? Ndimagawo ati amene mtsogoleri wanu wa uzimu/ kapena ena anawona kuti mwachita bwino.

**NDONDOMEKO YA KHUMI: MALIZANI PEPALA LA MAFUSO OKHUDZANA NDI MPHATSO ZA UZIMU:**

Mamphuziro a “Utumiki wa Mzimu Woyera” anaphatikiza mafuso okhudzana ndi mphatso za uzimu. Fomuyi ndiyofunika kwambiri ngakhale kuti sizimatengera kuti mumalize fomuyi kuti mudziwe mphatso yanu ya Uzimu.

## NDONDOMEKO YA KHUMI NDI CHIMODZI: PEZANI NDONDOMEKO ZIMENE MUKUGANIZA KUTI MUKANAKHALA NAZO.

Pezani mphatso imene mukuganiza kuti mukanakhazikikapo:

1. Chidziwitso cha mphatso imene mwaipeza kudzera mphuziroli.
2. Chimene Mulungu wakudziwitsani kudzera m’mapephero.
3. Chimene mwachipeza potsatira kawuniwuni
4. Ndi atsogoleri oti amene awonapo moyo wanu.
5. Unikani mbali imene mukuchita bwino makamaka dela limene munatumikirapo.
6. Kumalizitsa  mafuso a mphatso ya uzimu.

## NDONDOMEKO 12: KUPEZA ZOFUNIKA ZA UZIMU.

Unikani zofunika mdela lanu, pakhomo, ndi mpingo umene mukukhala. Ndizosowa ziti zimene zikupezekakabe.

## NDONDOMEKO YA CHISANU NDI CHITATU KWANIRITSANI CHOSOWEKA CHA UZIMU

Fananitsani ndandanda wa mphatso za uzimu umene munapanga pa “ndondomeko 12” ndi ndandanda wa mphatso imene mukukhulupirira kuti Mulungu anakupatsani. Pezani chofunika cha uzimu chimene chikufanana ndi mphatso imene mukukhulupirira kuti muli nayo, ndipo pangani chisankho chokwaniritsa chosoweka chimenechi.

## NDONDOMEKO YA KHUMI NDI CHINAYI.  UNIKANI UTUMIKI WANU

Mutatumikira kwa kanthawi mbali imene ndi mphatso yanu, pangani kauniwuni wa utumiki anu. Mwazindikira ndipo khalani mdindo wabwino wa mphatso yanu ya Uzimu pamene.

-Mukupindulitsa mbali yanu limene mukutumikira. Izi zitanthawuza kuti muwona zotsatira zabwino za uzimu za utumiki wanu.

-Mukakhutitsidwa….Mukusangalala ndi utumiki wanu. Mukasokonezeka, mutha kukhala kuti mukutumikira mdela limene simunapatsidwe.

-Atsogoleri akunena kuti mukuchita bwino pa udindo umene mukutumikira.

Ngati utumiki umene muli nawo sukufanana ndi kuthekera kwanu kwa uzimu ndipo simukuchita bwino, onaniso ndandanda wanu wa mphatso ndipo fusanu Mulungu kuti akuwonetseni mbali ina imene mukuyenera kutumikira.

Musakhumudwe….Ndibwino kwambiri kuzindikira ntundu wa mphatso zimene Mulibe kuti muzindikire mphatso zimene Mulinazo. Izi zingakuthandizeni kuti musataye nthawi yanu ndi utumiki umene simukuchita bwino. Pophatikiza pemphero ndi ndondomeko mukwanitsa kuzindikira mbali yanu mutumiki umene Mulungu anakupatsani.

## MAFUSO ODZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi lotsogolera.

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

2. Lembani masophenya atatu a mphatso ya Mzimu woyera.

(1)__________________________________________

(2)__________________________________________

(3)__________________________________________

3. Lembani zolinga zisanu za mphatso za Mzimu Woyera.

(1)__________________________________________

(2)__________________________________________

(3)__________________________________________

(4)__________________________________________

(5)__________________________________________

(Mayankho a mafusowa aperekedwa pamapeto a bukuli m'chaputala chomaliza.)

## KUDZIWA ZAMBIRI

Tchati chili m'musimu chikupereka malo osiyanasiyana kuti mukulitse chidziwitso chanu chokhudzana ndi kuti azimayi anagwiritsa bwanji ntchito mphatso ndi mautumiki awo.Tchati sichili ndi azimayi okha amene ali ndi mphatso za uzimu ndi ma utumiki mumpingo, komanso amene anagwiritsidwa ntchito ndi Mulungu pogwira ntchito zosiyanasiyana komanso azimayi apakhomo.

| **Malo** | **Nkhazi** | **Mbali** |
|---|---|---|
| Genesis 24:59: 35:8 | Debola | Nesi |
| Exodus 1:15-21 | Sifra ndi Puwa | Anamwino amene anaopa Mulungu ndikupulumutsa ana a Chihebri |
| Exodus 15:20-21 | Mariamu | M'neneri wa nkhazi; anayamba gulu loyambirira la azimayi |
| Oweruza 4:14 | Debora | M'neneri wa nkazi; mtsogoleri wa dziko |
| 1 Mafumu 10:1-13 | Mfumukazi Seba | Oyang'anira zinthu |
| 2 Mafumu 4:10 | Nkazi wa ku Sunemu | Wochereza |
| 2 Mafumu 5 | Nkazi osatchulidwa dzina | Mlaliki |
| Miyambo 31:10-31 | Nkhazi wangwiro | Nkazi, oyang'anira pakhomo, wa malonda |
| Mateyu 9:20-31 | Osatchulidwa | Anawonetsa mphatso ya Mzimu |
| 2 Timoteo 1:5 | Loice/ Yunike | Anawonetsa mphatso ya chikhulupiriro |
| Luka 2:37-38 | Anna | Mneneri, mlaliki, (analalikira Yesu kwa Ayuda): opembedzera. |
| Luka 8:1-3 | Mariya, Yohana, Suzana | Mphatso yakuthandiza |
| Luka 10:40 | Marita | Wokoza pakhomo, kuchereza alendo |
| Yohane 4 | Nkazi waku Samaliya | Mlaliki (kulalikira munthu pa enakha) |
| Machitidwe 9: 36-41 | Lidiya | Nkazi wa malonda: utumiki kwa akazi a |

| | | |
|---|---|---|
| | | masiye |
| Tito 2:3-4 | Akazi okalamba | Kuphuzitsa |
| Aroma 16:1-2 | Febe | Ntumiki: otumikira |
| Aroma 16:3, 7 | Priska | Ntumwi (Ogwira ntchito ndi Paulo mutumiki wake) |
| Aroma 16:1-2 | Azimayi osiyanasiyana | Ogwira ntchito mu mpingo: mipingo ya kum'manyumba |
| Machitidwe 18:26: Afilipo 4:3 | | |

# CHAPUTALA 13

## ZOTCHINGA NDI

## ZOSIYANITSA

**Zolinga:**

Mukamaliza chaputalachi muyamba kukwanitsa kuchita izi:

1. Kupangani ndandanda wa azimayi amene anapanga zodabwitsa m'Baibulo.
2. Kuzindikirani zakikulu zimene azimayi anapanga.
3. Kuvomereza mavuto apadera azimayi.

**Ndime yotsogolera:**

> **Ambuye anapatsa mau Akazi akulalikira uthengawo ndiwo khamu lalikuru**
>
> **(Masalimo 68:11)**

## MAU OYAMBA

Azimayi anapanga zinthu zambiri zamphavu m'Baibulo. Ndipo m'chaputalachi muphuzira izi komanso mavuto apadera amene Mulungu anapereka kwa azimayi. Muphunziraso mphavu imene azimayi alinayo ubwino wake ndi kuipa kwa kuthekera kwake.

## ZIPAMBANO ZAPADERA

M'dongosolo la Mulungu, azimayi anali anthu ofunika kwambiri m'biri ya m'Baibulo.

Chipangano chakale chimawonetsa zinthu zambiri zimene azimayi monga Debora, Rute, Estere, Abigaili, ndi ena anapanga. Mwayi ophunzira zimenezi ndi azimayi ena unapatsidwa m'chaputala chomalizira mphuziroli.

Azimayi anali ofunika mzochitika zikuluzikulu mthawi ya utumiki wa Yesu ali pa dziko lapansi komanso pakufalitsidwa kwa uthenga wabwino. Tili osangalatsidwa ndi zithu zimene anapanga chifukwa zimasonyeza dongosolo la Mulungu pophatikiza azimayi ngati atumiki a uthenga wabwino:

**MAI AKE A MESIYA:**

Kudzera mwa nkazi, Hava, tchimo linalowa koyambirira padziko lapansi. Koma kudzeranso mwa nkazi, Mariya, chipulumutso chinafika padziko lapansi:

> **Ndipo adzabala mwana wa mwamuna, ndpo udzamucha dzina lache Yesu; pakuti Iyeyu adzapulumutsa anthu ake kumachimo awo. (Mateyu 1:21)**

Uthenga wabwino, mau munjira ya Yesu Khristu, anafika padziko kudzera mwa mzimayi.

**OYAMBA KULALIKIRA CHIWOMBOLO:**

Yesu ali khanda, makolo ake anamutenga ndi kupita naye kukachisi kuti akadalitsidwe monga mwa chikhalidwe cha anthu a chiyuda. Atamuwonetsa kwa ntumiki amene anatumikira mutchalitchi, anazindikira kuti anali Mesiya olonjezedwa amene adzapulumutsa dziko kutchimo. Simion anakweza maso nayamika Mulungu:

**(Luka 2:30-32)**

Nkazi amene dzina lake ndi Ana anawona izi pamene zimachitika. Baibulo limawonetsa kuti anali mneneri ndiposo nkazi wamasiye amene ankhala musunagoge napitiliza kutumikira Mulungu mwa kusala kudya ndi kupemphera (Luka 2:36-37). Ana anazindikira Yesu ngati Mesiya olonjezedwa ndipo anali oyamba kugawa uthenga wa chiombolo.

> **Ndipo iye anafikako pa nthawi yomweyo, nabvomerezanso kutama Mulungu, nalankhukula za Iye kwa anthu onse akuyembekezera chiombolo kwa Yerusalemu (Luka 2:38)**

Ngakhale kuti nkazi anali chida chobweretsa uchimo padziko lapansi, iye analiso chida mudongosolo la Mulungu popereka chipulumutso ku tchimo. Ana anali oyamba kulalikira uthenga wabwino kwa Ayuda.

**OYAMBA KULANDIRA VUMBULUTSO LA MESIYA:**

Nthawi yoyamba Yesu anavomera kuti ndi Mesiya inali thawi imene anali ndi mzimayi. Yesu amadutsa ku Samaliya kupita ku Galileya. Pamena ophunzira ake anapita kukagula chakudya, Yesu anapuma pafupi ndi Sukali wa ku Samaliya.

Nkazi wa kusamaliya anafika kudzatunga madzi ndipo Yesu analankhulana naye. Zokambirana zawo zinalembedwa m'buku la Yohane 4. Pamene amakambirana, Yesu anavomereza kwa nthawi yoyamba kuti iye ndi Mesiya:

> **Nkazi ananena ndi Iye, Ndidziwa kuti Mesiya adza (wotchedwa Khristu); akadzadza Iyeyu, adzatiuza zonse.**

**Yesu ananean naye, Ine wakulankhula nawe ndine amene. (Yohane 4:25-26)**

## OYAMBA KULALIKIRA MADERA ACHIKHALIDWE:

Nthawi ya nkhani ya pa Yohane 4, utumiki wa Yesu unali usanafalikire kumadela amakhalidwe ena. Koma atadzidziwonetsa Yekha kwa nkazi wa ku Samaliya anakhala mlaliki oyamba kulalikira uthenga wabwino kwa amitundu. Analalikira kwa Asamaliya ndipo ambiri anakhulupirira Yesu (Yohane 4:41).

Monga m'mene Ana anali oyamba kutengera uthenga wa Yesu kwa Ayuda, Nkazi wa ku Samaliya anakhala olalikira oyamba kwa amitundu. Nkazi wa ku Samaliya anali wachigololo.

Nthawi imene anakumana ndi Yesu, anali atakwatiwapo kasanu ndipo amakhala ndi mwamuna amene sanali wakeso. Koma Yesu anadziwulula yekha kwa iye ndipo anatumikira kwa anthu ake.

Sizimatengera kuti chinachitika ndi chani, Mulungu afuna adziwulule yekha kwa inu, kusintha moyo wanu, ndi kukugwiritsani ntchito ku lemelelo wake. Monga nkazi wa ku Samaliya, mukhoza kupeza dela losangalatsa la utumiki mwa Yesu.

Sikunali koyenera kuti Yesu adutse m'Samaliya pa ulendo wake ochokera ku Yudeya kupita ku Galileya. Kunaliso kumbali. Palibe mudzi umene uli kutali kwambiri, palibe mzinda umene uli kutali kwambiri ndi njira ya Yesu. Mutha kufikira munthu m'modzi kumeneko ndi uthenga wabwino ndipo atha kubweretsa chitsitsimutso ku dela lonse.

Zinali zoyenera kuti Yesu asiye msewu waukulu ochokera ku Yudeya kupita ku Galileya kuti afikile mzimayi ameneyu, zikutanthawuza kuti ena aife tisiye msewu waukulu wa moyo. Tikuyenera kupita njira ina ndikusankha yovuta.

Kudzera mwa mzimayi ameneyi mzinda wonse unafikilidwa ndi uthenga wabwino. Yesu anawonetsera mfundo yofunika kwambiri ya kufalitsa uthenga pa zimene anakumana nazozi. Tikuyenera kufikira anthu okhulupirika andi azimayi komanso abambo amene adzakhala nako kuthekera kofikira anthu ndi uthenga wabwino.

**Ndipo zimene wazimva kwa ine mwa mboni zambiri, zomwezi uikize kwa anthu okhulupirika, amene adzadziwa kuphunzitsa enanso. (2 Timoteo 2:2)** Mukaphuzitsa anthu antundu uwu, adzakhala ndi kuthekera kofikira ambiri.

## ZOCHITIKA ZOTSIRIZA PA NTANDA:

Baibulo linalemba kuti azimayi amene anadzipereka okha kwa Yesu nthawi ya utumiki wake ali padziko lapasi anali omalizira kutchoka pantanda:

> **Ndipo analinso kumeneko akazi akuyang'anira kutali; mwa iwo anali Maliya wa Magadala, ndi Maliya amache wa Yakobo wamg'ono ndi wa Yose, ndi Salome;**
>
> **Amene anamtsata Iye, pamene anali m'Galileya, namtumikira; ndi akazi ena ambiri, amene anakwera kudza ndi Iye ku Yerusamelmu. (Marko 15:40-41)**

Chifukwa cha Chikondi cha Yesu Khristu, azimayi amenewa anadikira pantanda mpaka infa Yake. Kukhulupirika kwa iye pamena amalowa mu Yerusalemu ndi malemekezo a gulu lake, analiso okhulupirika mpaka imfa Yake.

**OYAMBA KU MANDA AKE:**

Mariya waku Magadalena ndi Mariya mayi ake a Yosefe anadikira kuti awone kumene Yesu akayikidwe ntembo wake utachotsedwa pantanda (Marko 15:47). Atapuma tsiku la sabata, anadzuka m'mawa pa tsiku loyamba la sabata napita kukadzoza thupi lake ndi makwala onukhila monga chikhalidwe chawo. Atafika pantanda anazindikira kuti Yesu mulibe. Azimayi anawona ngelo amene anati:

> **Palibe kuno Iye, komatu anauka; kumbukirani muja adalankhula nau, pamene analinso m'Galileya.**
>
> **Ndikunena kuti mwana wa munthu ayenera kukeperekedwa m'manja a athu ochimwa ndi kupachikidwa pantanda, ndi kuuka tsiku lachitatu. (Luka 24:6-7).**

Azimayi anali oyamba kulandira vumbulutso la kuwuka kwa akufa kwa Yesu pa manda ake.

**OYAMBA KULALIKIRA CHIUKITSO:**

Mzimayi atava nkhani ya chimwemwe ana:

> **Anfotokozera zonse khumi ndi m'modziwo, ndi otsala onse omwe.**
>
> **Ndipo mau awa anaoneka pamaso pao ngati nkhani zachabe, ndipo sanamvera akaziwo. (Luka 24:9 ndi 11)**

**OYAMBA KUWONA YESU:**

Kuwonekera koyamba kwa Khristu atawukitsikdwa kwa akufa anali Mariya wa kumagadalena. Nkhani iyi inalembedwa pa Yohane 20:11-18. Kenako Mariya anagawa uthenga wabwino…

> Mariya wa Magadala anapita, nalalikira kwa akumphunzirawo, kuti ndaona Ambuye ndi kuti ananena izi kwa ineye. (Yohane 20:18)

**OTEMBENUKA OYAMBA WA KU ULAYA**:

Opulumutsidwa woyamba wa ku Ulaya anali mzimayi dzina lake Lidiya:

> **Ndipo anatimva mkazi wina dzina lache Lidiya, wakugulitsa chibakuwa, wa ku mudzi wa Tiyatira amene anapembedza Mulungu; mtima wache Ambuye anatsegula, kuti amvere zimene anazinena Paulo. (Machitidwe 16:14)**

## MPHAVU YAIKULU YA AZIMAYI

Kuonjezera pa njira yapadera imene azimai anagwiritsidwira ntchito mundogosolo la Mulungu, ndibwino kuzindikira mphavu yawo yaikulu ndi ndikudziwa magwiritsidwe ntchito oyenera a mphavu. Mphavu yoyamba yaikulu kwa mzimayi inawonekera pamene Have anankokera Adam kuchimo. Tchimo loyamba limafotokoza za mphavu ya ubale umene umakhalapo pakati pa mwamuna ndi nkazi imene itha kugwiritsidwa ntchito bwino kapena molakwika.

Pa chifukwa cha ichi, Mulungu analamulira Aisrayeli kuti asakwatire akazi apakati pa amitundu. Anawachenjeza kuti azimayi amenewa atha kukhala ndi mphavu yakuchotsa ntima wa mwamuna kutali ndi Mulungu:

> **Nanga Solomo mfumu ya Israeli sanachimwapo nazo zinthu izi; chinkana mwa amitundu ambiri panalibe mfumu ngati iye, ndi Mulungu wache anamkonda ndi Mulungu wache anamlonga mfumu ya Aisraeli onse koma ngakhale iye, akazi achilendo anamchimwitsa. (Nehemiya 13:26)**

Mukaphuzira buku la Miyambo ya Solomoni, mupeza kuti zonena zambiri zokhudzana andi

"azimayi achilendo", zimene Solomoni anaphuzira,  mwachisoni, chifukwa cha mphavu yaikulu ya nkazi amene sali wa umulungu. Akulondolanso mutu omwewo m'buku la Mlaliki pamene akulunjika kwa azimayi amenewa kuti ali ndi mtima wonga misampha ndi manja ngati matangadza;

> **Ndipo ndinapeza kanthu kowawa koposa imfa, ndiko mkazi amene ndiye msampha, mtima wache ukunga maukonde, manja ache ndiwo matangadza yemwe Mulungu amuyesa wabwino adzampulumuka kwa iye koma wochimwa adzagwidwa naye. (Mlaliki 7:26)**

Baibulo limawonetsa kuti Solomoni…..

> **Ndipo anali nao akazi mazana asanu ndi awiri, ana akazi a mafumu, ndi akazi achabe mazana atatu; ndipo akazi ache anapambutsa mtima wache.**
>
> **Ndipo kunali atakalamba Solomo, akazi ache anapambutsa mtima wache atsate milungu yina; ndipo mtima wache sunakhala wangwiro ndi Yehova Mulungu wache monga mtima wa Davide atate wache. (1 Mafumu 11:3-4)**

Samisoni, munthu osankhidwa ndi Mulungu kubweretsa mamasulidwe kwa anthu a Israeli, anasintha chifukwa cha mphavu yaikulu ya mzimayi. Werengani nkhani ya Samison ndi Delila imene inalembedwa pa Oweruza 13-16.

Yesaya analembaso kuti utsogoleri wa azimayi amene osapembedza unapangitsa Israeli kuti asiye kutsata njira yolondola.

> **Anthu anga awabvuta ndi ana, awalamulira ndi akazi anthu anga inu, iwo amene akutsogolerani, ndiwo akuchimwitsani, nawononga njira zanu zoyendamo. (Yesaya 3:12)**

M'chipangano chatsopano, zinalembedwa kuti azimayi odzipereka komanso awulemu anabweretsa chinzunso pakati pa mpingo woyamba:

> **Koma Ayuda anakakamiza akazi opembedza ndi omveka, ndi akulu a mudziwo,**
>
> **nawautsira chinzunzo Paulo ndi Barnaba, ndipo anawapitikitsa iwo m'malire awo. (Machitidwe 13:50)**

Mphavu yaikulu ya azimayi siyolakwika. Mulungu anawapatsa azimayi kuthekera kwakukulu kotere. Kugwiritsidwa ntchito molakwika, kumawononga zinthu. Kugwiritsidwa ntchito ndi Mzimu Woyera, ndi mphavu imene itha kusintha mitima ya amuna ndi tsogolo la maiko onse. Izi zinafotokozedwa m'biri ya m'Baibulo ya azimayi monga Debora ndi Estere.

## MAVUTO APADERA AZIMAYI

Vuto loyamba tilipeza m'mawu a Solomoni amene amfuna azimayi amene amadziperekadi kwa Mulungu. Iye akulemba:

> **Chome moyo wanga uchifuna chifunire, koma osachipezai ndi ichi, mwamuna m'modzi mwa chikwi ndinampezadi, koma mkazitu mwa onsewo sindinampeza. (Mlaliki 7:28)**

Ndi chinthu chofunika kukhala mzimayi wotero pakati pa azimayi zikwi zikwi, amene ntima wake uli odzipereka kwa Mulungu!

## VUTO PAKHANI YA CHITSOGOZO:

Zolinga zambiri zimene azimayi amazikhazikitsa sizili zokhalitsa. Amapanga zisankho za ukwati, ndi maphuziro aukachenjede. Koma izi zikakwaniritsidwa chimatsalanso ndi chani pa zolinga zokhalira ndi moyo?

Mulungu akufuna azimayi kuti akhale ndi chitsogozo. Kaya ndi azimayi chabe apakhomo, wophuzira, kaya a  m'sukulu za ukachenjede, akuyenera kumakhudzidwa pofalitsa uthenga

kudziko lapansi. Kaya mukukhala m'matawuni, kumudzi, malo ovuta kufikirika, mutha kukhala mbali imodzi ya gulu la azimayi padziko lonse amene ali ndi cholinga chimoddzi; Kusindikiza uthenga wabwino wa Yesu Khristu.

**VUTO LA KUSUNGA MWAMBO**

Mulungu analankhula ndi azimayi pogwiritsa ntchito Yesaya ndi mavuto apadera:

> **Ukani, akazi inu, amene muli nkukhala phe, mumve mawu anga; inu ana akazi osasamalira, cherani makuti pa kulankhula kwanga. (Yesaya 32:9)**

Werengani uthenga onse wa Mulungu paYesaya 32:10-20. Uthengawu unalembedwa pamene asilikali a amafuna kugwira Yuda ngati chilango pa machimo ake, koma ndiwothandiza kwa nkazi aliyese amene amaika maganizo ku dziko lapansi ndi zosangalatsa.

Azimayi amene Mulungu analankhula nawo anali osasamala komanso otayilira chifukwa anali ndi ndalama ndi chisangalalo. Anasiya kutsata Mulungu natsata zosangalatsa za dziko lapansi. Dziko ndi mizinda imene iwo amakhala inatsala pang'ono kuti iwonongedwe, koma samadziwa za chiwonongeko chimene chimadza.

Vuto lomwelo lili pakati pa azimayi panopa. Ambiri anatayilila ndipo adzadza miyoyo yawo ndi chisangalalo chosakhalitsa. Ali osazindikira kuti chiweluzo chikubwera cha dziko lapansi ndikuti anthu onse amene awazungulira adzakumana ndi moyo opanda Yesu. Azimayi a chikhristu amakhala moyo otayilira pamene maiko awo akuyamba kusatsatira Mulungu. Amasangalala ndi zosangalatsa za kudziko pamene athu osakhulupirira Mulungu akukhala ndi ulamuliro mboma. Uthenga wa Mulungu kwa iwo ndi wakuti dzukani!

Kudzera mwa mneneri Yesaya, Mulungu anawawuza azimayi kuti manyumba awo, malo, ndi minda yawo zidzawonongedwa. Njira yokhayo imene atha kuperewa chiweluzo ndi kudzuka m'dzina la Yesu Mulungu, asatayilireso, ndikuvetsera kwa Mulungu nachita monga mwa mau a Mulungu. Chodabwitsa azimayi a ku Yudeya amene uthengawu umaperekedwa sanavere.

Chiweluzo chinafika, ndipo mizinda yawo inawonongedwa monga Mulungu anachenjezera.

Koma panali lonjezo la chiyembekezo. Chitantha chiweluzo, mzimu wa Mulungu ukanaperekedwa;

> **Kufikira mzimu udzathiridwa pa ife kkuchokira kumwamba, ndi chipulu chidzasanduka munda wodbalitsa udzayesedwa nkhlango.**
>
> **Pamenepo chiweruzo chidzakhala m'chipululu, ndi chilungamo chidzakhala m'mundsa wobalitsa. (Yesaya 32:15-16)**

Kudzera mphavu ya Mzimu Woyera malo amene anawonongeka anakhala othandiza chifukwa cha kukula kwa zomera nakhala nkhalango.  Ngakhale Mulungu amalanga, amabwezeretsanso kuthira mzimu wake pa amene anawaweruza. Kuchokera ku malo owonongeka kwatuluka zokolola zambiri.

Azimayi amene onatayilira atalandira malangizo amenewa kuti asunge mwambo navera Ambuye, sadzalangidwa. Akazindikira m'mene moyo wawo wauzimu ulili, zithu zadziko lapansi zimene zadzaza moyo wawo, nalapa zochimwa zao adzakhululuka.

Koma uthengawu utha kugwiritsidwa ntchito osati pa munthu m'modzi chabe. Chitsitsimutso chikanatha kuteteza chiwerezu cha dziko lonse. Mulungu analankhula ndi azimayi a ku Yudeya kuti atsogolere chikonzero cha moyo wa uzimu. Mulungu anati, "ngati inu azimayi muvere chidzudzulo changa, dzukani ndipo chitanipo kanthu, mutha kupewa chiweruzo pa dziko lanu.

Azimayi onse pa  dziko lapasi lelo akuyitanidwa…"Dzukani, azimayi amene mwatayilira...verani mawu…tcherani khutu ku mau anga."

-Siyani zosangalatsa za dziko lapansi!

-Dzikonzeni nokha moyo wauzimu!

-Dzigwedezeni nokha ndi maiko anu kuti chiweruzo cha Mulungu chisafike pa inu.

**VUTO LA KUDZIPEREKA**

Kudzuka ndikukhala mbali yoyenera ngati azimayi awuzimu zimafunika kudzipereka. Paulo akubweretsa chinthu chofunika kwambiri osati kwa azimayi okha komaso kwa anthu ena onse. Ndi maitanidwe akudzipereka:

> **Chifukwa chake ndikupemphani inu abale, mwa zifudo za Mulungu kuti mupereke matupi anu nsembe yamoyo, yopatulika, yokondweretsa Mulungu, ndikoko kupembedza kwanu koyenera.**
>
> **Ndipo musaafanizidwe ndi makhalidwe a pansi pano; koma mukhale osandulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu, kuti mukanzindikire chimemene chiri chifuno cha Mulungu, chabwino, ndi chokondweretsa ndi changwiro. (Aroma 12:12)**

Kudzipereka kwa Mulungu ndi kusunga mwambo  ku njira za Mulungu zimadzetsa njira imene imatsogolera ku chidziwitso cha chifuniro changwiro cha Mulungu m'moyo wanu.

**KUDZIDYESA NOKHA**

1. Tchulani ntchito zinayi zazikulu zimene azimayi anapanga m'chaputalachi:

(1)______________________________________________________________

(2)______________________________________________________________

(3)______________________________________________________________

(4)______________________________________________________________

2. Lembani ndime Yotsogolera

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

______________________________________________________________________

3. Werengani chiganizo chirichonse. Ngati chiganizo chiri cholondola lembani T panzere umene wapatsidwa. Ngati sichiri cholondola lembani F pamwamba panzere uli kumayambiriro kwa chiganizo.

a._____Solomo anali ndi akazi ambiri amene anatembenuza ntima wake naleka kutsatira Mulungu.

b._____Azimayi anazuza mpingo woyambirira, kuphatikizirapo Paulo ndi Barnaba.

c._____Mphavu yaikulu ya azimayi imachokera kwa Satana.

d._____Palibe chirichonse chimene azimayi angapange chokhudzana ndi moyo wawo wauzimu m'dziko lawo.

e._____Kudzipereka ndi kusunga mwambo sizimatanthawuza kuti mudzapeza chitsogozo pa moyo wanu.

(Mayankho a mafusowa aperekedwa kumapeto m'chaputala chomalizira cha bukuli.)

**KUDZIWA ZAMBIRI**

Buku lothandizira kuvetsetsa  Baibulo (Konkodasi) likuthandizani podziwa zambiri pa mutu wa azimayi. Limapereka mau otsogolera amene anagwiritsidwa ntchito m'Baibulo ndi malo amene mauwa amapezeka.

Ngati mungapeze bukuli, onani mau otsatirawa:

1. Mzimayi
2. Azimayi
3. Nkazi wapabanja
4. Akazi apabanja
5. Nakubala
6. Apabanja
7. Banja
8. Kukwatira
9. Nkhazi wa masiye

Mupeza ndandanda wa malo ambiri opatsidwa chifukwa cha mau aliwonse. Onani malo amenewa kuti mupitirize zimene Baibulo limaphunzitsa zokhudzana ndi azimayi.

Ngati mulibe buku lothaniza  kufotokoza Baibulo, lembani mzere kusi kwa malo amene akukamba za azimai m'Baibulo lanu mukamawerenga. Mapeto ake mudzapeza kuti malo onse amene akukamba za azimayi alembedwa mzere kunsi kwake m'Baibulo lanu.

## CHAPUTALA 14

## UTUMIKI WA AZIMAYI

**Zolinga:**

Mukamaliza chaputalachi muyamba kukwanitsa kuchita izi:

1. Kulemba vesi yotsogolera.
2. Kukonza utumiki wa azimayi
3. Kupeza zofuna za azimayi.

**Ndime yotsogolera:**

> **Ndipo Miriamu m'neneriyo, mlongo wa Aron, anagwira lingaka m'dzanja lache; ndipo akazi onse anaturuka kumtsata ndi malingaka ndi kuthira mang'ombe.**
>
> **Ndipo Miriamu anawayankha, Yimbirani Yehova, pakuti wapambanatu; Kavalo ndi wokwera wache anawaponya m'nyanja. (Exodo 15:20-21)**

### MAU OYAMBA

M'buku lina lililose la ku Harvestime International Institute timapereka ndondomeko yakagwiritsidwe ntchito ka zipangizo m'magulu. Pitani kumayambiriro a bukuli mupeza malangizowa. Ndondomeko zikuthandizani kuti mungagawane nawo bwanji anthu ena zimene mwaphuzira.

Monga munaphuzirira phuziloli, mukhoza kukhala kuti mukuva maitanidwe apadera awutumiki wapakati pa azimayi. Chaputalachi chimapereka ndondomeko zakuti utumiki wa azimayi mungayambe bwanji. Maganizo akuti mungalongosole zinthu bwanji anapatsidwa kuonjezerapo kuti mungadziwitse bwanji anthu za gulu lanu. Malangizo akuti mungapeze bwanji azimayi amene ali ndi zofunika za uzimu za pamoyo.

### KODI UTUMIKI WA AZIMAYI NDIWOVOMEREZEKA MONGA MWA MALEMBA?

Gulu loyamba la azimayi linapangidwa ndi Mariamu, nchemwali wake wa Mose. Zinalembedwa kuti:

> **Ndipo Miriamu mneneriyo, mlongo wa Aroni, anagwira lingaka m'dzanja lache; ndipo akazi onse anaturuka kumtsata ndi malingaka ndi kuthira mang'ombe.**
>
> **Ndipo Miriamu anawayankha, Yimbirani Yehova, pakuti wapambanatu; Kavalo ndi wokwera wache anawaponya m'nyanja. (Eksodo 15:20-21)**

Mariamu ansonkhanitsa azimayi ndi cholinga chakumulambira ndikumulemekeza Mulungu.

Mchipangano chatsopano kunalembedwa kuti pa Machitidwe 9:36-41 Dolika anali ndi utumiki kwa azimayi amasiye. Paulo akulangiza azimayi akulu kuti aphuzitse azimayi ang'ono (Tito 2:3-4). Kuchokera ku zitsanzo izi tikuwona kuti utumiki wa azimayi ndi ovomerezeka ndi malemba.

## CHIFUKWA CHANI PAKUYENERA KUKHALA UTUMIKI WA AZIMAYI?

Utumiki wa azimayi ndi ofunika chifukwa chakuti:

### AZIMAYI AMAFUNA UTHENGA WABWINO:

Panopa azimayi alipo okwana theka la anthu padziko lonse lapansi. Akufunika akuti amve uthenga wabwino wa chipulumutso kudzera mwa Yesu Khristu.

### AZIMAYI ALI NDI MAVUTO APADERA:

Azimayi m'maiko onse ali ndi zofuna za kuthupi ndi zina zokhudzana ndi maganizidwe. Ali ndi mavuto, ndi zofuna zosiyana ndi ena. Azimayi amafunika kuti adziwe kuti mwa Yesu muli mayankho pa mavuto awo.

### AZIMAYI AMAFUNIKA KUTI AKULE M'MOYO WA UZIMU:

Azimayi amafunika kuti akule m'mapephero, kudzipereka, kusunga mwambo, ndi chitsogozo pa makhalidwe.

### AZIMAYI ALI NDI MBALI YAWO MDONGOSOLO LA MULUNGU:

Akuyenera kuti azindikire kuthekera kwawo, cholinga, ndi malo awutumiki wawo m'thupi la Khritu.

## MAYAMBIDWE AWUTUMIKI WA AZIMAYI

Ndondomeko zakayambidwe ka utumiki wa azimayi ziri m'musimu:

### NDODNOMEKO YOYAMBA

Yambani kupemphera pa chitsogozo cha Mulungu ndi azimayi m'dera lanu.

### NDONDOMEKO YA CHIWIRI:

Bweretsani pamodzi gulu la azimayi a chikhristu kuti akuthandizeni kulongosola zinthu za utumiki wanu. Funani amene mitima yawo ambuye anaikhudza ndi masophenya ndi cholinga chofanana ndi chanu. Yambani kupepherera azimayi amdera lanu pamodzi.

**NDONDOMEKO YA CHITATU:**

Mukamapephera pephani Mulungu kuti kuzindikiritseni cholinga cha utumiki wanu kwa azimayi. “Mau a acholinga” akuyenera kuyankha fuso lakuti “chifukwa chani tiripo? Kodi Mulungu afuna kuti tikwaniritse chani?”

Ndibwino kudziwa cholinga chifukwa chakuti Baibulo limati “pamene palibe masophenya anthu amawonongeka.” Ngati anthu amafuna cholinga pa makhalidwe, gulu la anthu limafunika cholinga kuti lipitirizebe kukhala.

Pali zolinga zambirimbiri zimene zingapangitse kuti utumiki wa a zimayi ukhalepo. Gulu la anthu litha kukhala ndi cholinga chimodzi kapena zingapo mwa zolinga izi:

**Pemphero**: Mutha kukumana pamodzi ndi kupherera dela, dziko lanu, atsogoleri ndi dziko lonse la pansi. Kudzera m’mapephero mutha kufikira bwino madela onse a dziko nakhala mphavu yaikulu yothandiza mene amakhala patsogolo ndi ntchito ya kufalitsa.
**Kukambirana mawu a Mulungu**: Cholinga cha gulu lanu kutha kukhala kukambirana mau a Mulungu pamodzi ndicholinga chotsogolera azimayi pakukula muzimu.

**Kufalitsa**: Cholinga chanu chitha kukhala kufikira dela lanu, mzinda, mudzi ndi uthenga wabwino pogwiritsa ntchito njira zosiyanasiyana.

**Utumiki wa pakati pa azimayi achichepere:** Mutha kugwiritsa ntchito mfundo ya m’Baibulo ya azimayi a chikhristu a akulu kuphuzitsa azimayi ang’ono. Ngati ziri chomwechi, mau a cholinga analembedwa kale kwa in pa Tito 2:3-4.

Utumiki wa zofunika za pathupi: Mutha kutumikira ka gulu ka azimayi, monga azimayi amene sali pa banja, azimayi ndi mankwala ozunguza bonga, azimayi oledzera, azimayi akundende, ana, ana osokonekera, azimayi a m’masukulu zaukachenjede m’mizinda yanu, kapena azimayi m’manyumba alendo kapena mzipatala. Mutha kunva kuitanidwa kutumikira pakati pa azimayi am’dera lina kapena m’madela osatukuka, monga m’madera amene chuma ndichovuta.

Magulu amautumiki azimayi imapereka kuthekera kwakukulu pa cholinga cha gululo. Unikani dela lanu. Kodi ndi magulu oti azimayi amene sakufikiridwa? Ikhodza kukhala ntchito yapadela imene Mulungu wakusungirani.

**Othandizira mpingo:** Mutha kuyamba gulu lazimayi ngati othandizira mpingo. Cholinga chanu chingakhale kuthandiza zochitika zina mumpingo.

**Othandiza ofalitsa uthenga:** Cholinga cha gululi chingakhale kuthandiza ofalitsa uthenga popemphera, popereka ndalama ndi zinthu zina.

**Akhristu pa dziko lonse:** Cholinga cha gulu iri chitha kukhala kuika chidwi, kupemphera ndikuchita kanthu pa cholinga chapadziko lonse chofikira dziko lonse lapansi uthenga wabwino wa Khristu.

**NDONDOMEKO YA CHINAYI:**

**Khazikitsani tsiku, nthawi, ndi malo am'sonkhano wanu.**

**NDONDOMEKO YA CHISANU:**

Adziwitseni anthu za gululo m'dera lanu, adziwitseni azimayi za tsiku, nthawi, malo ndi cholilnga cha msonkhano wanu. Kaya dongosolo lanu lakudziwitsa anthu ndiyongolankhula chabe, m'midzi kaya ndi yokhudza zambiri m'mizinda, mukuyenera kukhala ndi uthenga okhazikika. Monga lamulo liriri m'chipangano chatsopano, "Pitani m'midzi ndi m'makwalala ndikuwalamulira kuti kuti afike." M'musimu muli maganizo anjira zimene mungazigwiritse ntchito podziwitsa anthu zagulu lanu. Maganizo amene mungawagwiritse ntchito atha kutengera chuma chimene muli nacho ndi dera limene inu mulimo:

1. Pemphani chilolezo kwa abusa anu kuti muike uthenga wanu m'malo azidziwitso ndi mzipinda zophuzirila ana.

2. Pemphani abusa kuti alengeze kuchokera pagome za msonkhano uliwonse patatsala sabata imodzi.

3. Pemphani abusa kuti aike chidziwitso m'mabuku ndi malo azidziwitso ngati mpingo wanu umasindikiza mabuku.

4. Perekani mapepala awuthenga wanu m'manyumba amabuku. Pemphani eni kuti ayike pamalo owoneka.

5. Ngati mzinda wanu uli ndi malo azamalonda, pemphani ngati angasindikize uthenga wanu (umene mwapereka) kwa anthu a mdela lanu amene amafika kuti apeze uthenga okhudzana ndi dela lanu.

6. Perekani uthenga wa m'mapepala kwa anthu okuzingulilani, kutchalitchi, m'magulu azimayi, ndi kuntchito kwanu.

7. Siyani mapepala authenga wanu m'malo ochapila, m'misika, nyumba zogulitsila zinthu……malo onse amene azimayi amakumanakumana… (Khalani otsimikizika ndi chilolezo cha oyang'anira zipinda zosungila zinthu).

8. Nyumba yowerengela mdela lanu ikhoza kukhala ndi malo olengezera uthenga. Ngati ziri choncho kaperekeni uthenga wanu.

9. Tumizani makalata oyitanira anthu kwa:

   -Akazi azibusa

   -Ndandanda wa maina umene munatenga kwa azimayi ndera lanu.

   -Atsogoleri a magulu ene amene sali achipembedzo.

   -Ndandanda wa azimayi umene anatengedwa ku tchalitchi mdela lanu ndi mu mpingo wanu.

10. Lengezani za msonkhano wanu pa wailesi, wailesi za kanema, ndi magulu osindikiza nkhani ngati izi zirimo m'dela lanu.

**NDONDOMEKO YA CHISANU NDI CHIMODZI:**

Panopa ndinu okozeka tsopano kuyamba msonkhano ngati gulu la azimayi. M'musimu muli maganizo ena:

Nsokhano oyamba:

1. Tengani dzina ndi adilesi ya aliyese amene wabwera. Izi zikuthandizani kuti muzumikizane nawo pa za misonkhano yakutsogolo.

2. Tsiku la nsokhano lisanafike, konzani uthenga wa dzina la gulu lanu, cholinga uyikeni pa mapepala. Apatseni anthu ndipo muwone nose pamodzi pa tsiku la nsokhano wanu oyamba.

3. Kambiranani madongosolo a amene muli nawo pa gulu lanu: mwa chitsanzo, mwayi wa utumiki, chiyanjano, maphuziro ndi zina. Azimayi akuyenera kuzindikira phindu limene alipeze pa moyo wawo wa uzimu ndipo akhudzidwe ndi madongosolo adela lanu.

4. Perekani mwayi wa kuyamika ndi kulambira Mulungu, utumiki wa mau a Mulungu, ndi mapephero azofunika za amene abwera. Gawo la utumiki pa nsokhano oyambirira ndizofunika kwambiri. Azimayi adzakwanitsa kubwera misonkhano yantsogolo ngati zofuna za pamoyo wawo wa uzimu zafikilidwa ndipo akuphunzira za Mulungu ndi mau ake.

5. Perekani ma pepala authenga wokhudza utumiki wanu kwa azimayi amene abwera ndi malangizo oti akauze anthu ena zagululo. Alimbikitseni kuti akagwiritsa ntchito zipangizozi kuitanira ena ku misonkhano.

**Misonkhano yotsatira**:

Apa pali maganizo pa misonkhano ya m'tsogolo:

1. Mukuyenera kumalandira alendo ndikuwalemba maina. Apatseni uthenga wa cholinga cha gulu lanu pa pepala.

2. Perekani mwayi wa kumuyamika ndi kumulambira Mulungu, utumiki wa mau a Mulungu, ndi mapephero a zofunika za pa moyo wa anthu.

3. Mutha kufuna kuphuzira mphuziro iri "Azimayi, Manenedwe a Baubulo". Mutha kufunaso kugwiritsa ntchito maphuziro ena amene a Harvestime International Institute amapereka.

**NDONDOMEKO YA CHISANU NDI CHIWIRI:**

Lumikizanani ndi onse amene anabwera pa msonkhano oyamba ndi kadi, lamya kapena powayendera tsiku la msonkhano lisanafike. Machitidwewa akuyenera kuchitika kwa alendo onse amene abwere m'misonkhano yamtsogolo.

**KAWUNIWUNI WA GULU**

Linganilrani mafuso awa: Ndi azimayi antundu wanji amene ali mgulu lanu? Zofuna zao zapadera ndi chani? Mukuyenera kudziwa izi ngati mungafune kuwatumikira moyenera.

**Moyo wawo ngati anthu:** Kodi azimayi amgulu lanu ali pa banja? Izi ndi zofunika pakuti zofuna zawo ndi sizofanana. Chitsanzo, mzimayi amene sali pabanja atha kukhala osasangalala pamene mzimayi wapabanja atha kusowa nthawi ya payenkha. Mzimayi amene akulela ana yekha ali ndi zofuna zapadela, mongaso mzimayi wa masiye kapena amene ukwati unatha.

Azimayi m'gulu lanu atha kukhala:

-Osakwatiwa

-Okwatiwa koma opanda ana

-Okwatiwa ndipo ali ndi ana

-Banja linatha ndipo ali ndi ana

-Banja linatha ndipo alibe ana

-Banja linatha ndipo sanakwatiwenso, akulela ana okha

-Banja linatha ndipo sanakwatireso, alibe ana

-Banja linatha ndipo anakwatira koma alibe ana

-Banja linatha ndipo anakwatiranso koma alibe ana

-Banja linatha koma anakwatiranso ndipo ali ndi ana

**Zimene amachita tsiku ndi tsiku:** Azimayi amene amapanga zinthu zosiyana alinso ndi zofuna zosiyanasiyana. Njira zopezera ndalama zosiyanasiyana zimene zingapezeke mdela lanu ndi monga izi. Onani kuti njira zosiyanasiyanazi zikhoza kuphatikizana, monga nkanzi wapakhomo amenenso amagwira ntchito kunja kwa nyumba.

-Mwana wa sukulu

-Azimayi amene amatumikira

-Amalonda kapena ogwira ntchito

-Opuma ntchito

-Azimayi apakhomo

-Ogwira ntchito za maganyu

**Malo okhala:** Kodi azimayiwa amakhala kuti? Malo amene amakhala amawonetsa zofuna zawo ndi mavuto awo:

-Mizinda

-Midzi

-Malo ovuta kufikirika

-Malo amene chikhalidwe ndi mapezedwe achuma ndiovuta kwambiri

-Olemera

-Ochita bwino

**Maubale:**

Azimayi amakhazikitsa maubale osiyanasiyana. Nthawi zina amakumana ndi mavuto okhudzana ndi ubale ndi:

-Banja/ amuna/ ana

-Ochita nawo malonda

-Mpingo kapena otumikira nawo

-Azawo

-Amene anawazungulira

**Mphunziro:** Pangani kawuniwuni wa maphunziro athu a gulu lanu. Izi ndizabwino kuti mudziwe m'mene mungapezere zipangizo zophunzirira. Maphunziro awo akhoza kukhala monga:

-Osaphunzira

-Sukulu za ku pulayimale

-Sekondale

-sukulu za ukachenjede

-Mamphunziro awukatswiri

**Zofunika:** Zofunika azimayi zitha kukhala za uzimu, zakuthupi, zokhudza maganizidwe, kapena zithu zina. Kuonjezera apo, atha kukhala kuti akuvutika ndi mavuto ena, monga kuledzera kapena mankhwala ozunguza bongo. Zinthu izi zikuthandizani kuti muzindikire zofunika za azimayi:

**Zofunika za uzimu**

-Chipulumutso

-Chiyeretso kapena kupatulidwa

-Ubatizo wa madzi

-Ubatizo wa mzimu woyera

-Machilitso ndi mamasulidwwe

-Kukula m'moyo wa uzimu kuonjezerapo mphatso za Uzimu, chipatso cha Uzimu, kudziwa chifuniro cha Mulungu, kuthana ndi mavuto a pa moyo, ndi kuthana ndi mayesero.

**Zofunika za m'mene amaverera:**

-Mantha

-Kusungulumwa

-Kukhumudwitsidwa

-Kupwetekedwa

-Kusakhululuka

-Kukhala ndi maganizo awekha

-Nkwiyo

-Udani

-Mangawa

-Nsanje

**Zofunika pa zachuma**

-Kusoweka ndalama zokwanira pa zofuna za pakhomo

-Mwayi wantchito

**Zofuna za kuthupi**

-Matenda

-Kulemera

-Mavuto amawonekedwe

**Zofunika zina:** Zofunika zina mgulu lanu ndi zinthu monga izi:

-Kutha kwa banja

-Kudzipha

-chikhalidwe

-Kuchotsa pathupi

-Fodya

-Mowa

-Za matsenga

-Kukhala ndi ziwanda komanso kuponderezedwa ndi ziwanda -Kuthana ndi imfa

Utumiki wabwino kwa azimayi umakhudzanso kupereka malangizo ndi kufikira zofuna za mamembala. Pezani zofuna za azimayi ndipo ndi kudzoza kwa mzimu woyera afikireni mwa Chikondi ndi kukhudzika kuti mukwaniritse zofuna zao.

**MAFUSO ODZIYESA NOKHA**

1. Kodi amena anapanga gulu la azimayi loyambiria ndi ndani

___

2. Ndikofunika bwanji kuti mukhale ndi mau a cholinga?

___

3. Lembani ndondomeko 6 zoyambira utumiki kwa azimayi.

(1)___

(2)___

(3)___

(4)___

(5)___

(6)___

(7)___

4. Lembani ndime yotsogolera

___

___

___

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto a chaputala chomalizira mbukuli)

## KUDZIWA ZAMBIRI

Ngati muli osangalatsidwa kupangitsa utumiki kwa azimayi, mutha kufuna kuyamba chaputala cha Naomi Netiwoki. Umenewu ndi utumiki wa azimayi othandizira Harvestime International Netiweki. Mfundo ziri m'musimu mutha kuzigwiritsa ntchito kuti muyambitse mdela lanu.

## DZINA

Dzina "Naomi Netiweki" lukuwonetsa cholinga cha gulu lapadziko lonse la azimayi.

### NAOMI…

Dzina lakuti Naomi likuchokera pa muthu wina m'chaputala cha Rute M'buku loyera. Dzina limatanthauza "zokondweretsa." Komabe moyo wa Naomi sunali osangalatsa.

Nthawi imene kunali chilala chachikulu, Naomi, mwamuna wake, ndi ana ake awiri anasamukira ku dziko loyipa la Amoabu. Ana ake onse anakwatira kuchokera kwa mabanja ochimwa. Kenako, ana awiri a Naomi anamwalira. M'modzi mwa apongozi ake dzina lake Olipa, anabwerera kwa  makolo ake. Owawidwa komanso wosweka ntima, Nomi anawawuza azake kuti asamutchulenso "Naomi" Koma kuti amutchule Mara kutanthawuza kuti "kuwawidwa." Moyo wake unasiya kukhala ndi tanthawuza la kuti, cholinga, ndi chitsogozo chifukwa cha nyengo yopweteka.

Koma Mulungu anachita modabwitsa posintha moyo wa Naomi. Anamupititsanso kudziko lakwawo nabwezeretsa zonse zimene anataya. Kenako, Naomi anali nako kuthekera kotsogolera mpongozi wake, Rute, ku cholinga cha Mulungu.

Dziko lose lapasi, pali azimayi amene akufuna Mulungu kuti asinthe moyo wawo. Ali okha, amphwayi, owawidwa, ndi osweka ntima, opanda cholinga ndi chitsogozo pa moyo wawo. Sakufuna chiyanjano cha amayi ndi kukambirana mawu a Mulungu kokha. Akufunika gulu limene lingawathandize kuzindikira cholinga cha Mulungu chapadera m'dongosolo la Mulungu pakugwiritsa ntchito mfundo zophuzitsidwa m'mawu a Mulungu. Naomi netiweki ikufuna kufikira "a Mara" a dziko lino, kuwatsogolera pakubwezeretsedwa kwa zonse zimene zinatayika, ndikuwaphuzitsa, kulimbikitsa, ndi kuwakonzekeretsa kuti achitepo kanthu pa kholola la uzimu la dziko lonse.

### NETIWEKI….

Mau akuti "netiweki" akuwonetsa mayalidwe azinthu m'bungwe. Ndife azimayi a zikhalidwe, mitundu, ndi mipingo yambiri amene tabwera pamodzi ndikudzipereka ku cholinga chenicheni.

## CHOLINGA CHATHU

Tikukhulupirira kuti maziko a kuchita bwino m'moyo wauzimu wagona pa mfundo za kupemphera, kudzipereka, kusuga mwambo ndi chitsogozo. Ndi cholinga cha bugweli kupititsa patsogolo mgwirizano wa azimayi amene:

**Kudzipereka**…kumawu a Mulungu kuti avetsetse ngati anthu, ndikugwiritsa ntchito ndikudziwitsanso ena.

> **Mau anu aikika kumwamba, kosatha, Yehova. (Masalimo 119: 89)**

Chivumbulutso cha Mulungu m'mawu ake kudzera mwa anthu, mfundo, mauneneri, ndi malonjezano. Povetsetsa ndipogwiritsa nthito, kukhala kwathu ndi Mulungu zitha kutsogolera

moyo odzipereka, kusunga mwambo, ndi moyo wokhala ndi chitsogozo monga zinafotokozeredwa pa Aroma 12-1-2

Kudzipereka ku…..njira za Mulungu, ndikufanana ndi chithuzithuzi cha Khistu ndi kudzazidwa ndi Mzimu woyera.

> **Chifukwa chache ndikupemphani inu abale, mwa zifundo za Mulungu kuti mupereke matupi anu nsembe yamoyo, yopatulika, kukondweretsa Mulungu, ndiko kupembedza kwanu koyenera. (Aroma 12:1)**

Kusunga mwambo…mdongosolo la Mulungu ndi cholinga cha umulungu mbali zonse za moyo ndi utumiki; osafanizidwandi ndi makhalidwe a dziko lapansi, koma ndi machitidwe a umulungu.

> **Ndipo musafanizidwe ndi makhalidwe  apansi pano: koma mukhale osadulika, mwa kukonzanso kwa mtima wanu. (Aroma 12:2a)**

Kutsogozedwa…ku cholinga cha Mulungu ngati ogwira ntchito ophuzitsidwa amene akutumikira m'munda wa Uzimu wa dziko lathu.

> **….kuti mukazindikire himene chiri chifuno cha Mulungu, chabwino, ndi chokondweretsa ndi changwiro (Aroma 12:2b)**

## MBALI YATHU

Pali ziphuzitso zamphavu za m'Baibulo zimene zimatibweretsa pamodzi ngati okhulupirira, mwa chitsanzo, choonadi cholimbikitsa kuchokera m'Baibulo (Masalimo 119:89). Paliso kudzipereka kwina pa cholinga,  ntchito yaikulu imene ambuye anatisiyira (Mateyu 28:19-20). Ziphuzitso zina zofunika kwambiri ndi monga Naomi netiweki, ma membala a netiweki pamodzi ngati mphavu ya uzimu ya Mulungu.

Ndi ubale wa kulumikizana umenewu, mpikisano wa mumpingo suloledwa. M'malo mwake, azimayi onse amayanjanitsidwa ndi cholinga komanso mzimu m'dela la akhristu amene samapanga mpikisano.

> **Koma ndikudandaullirani inu abale, mwa dzina la Ambuye wathu Yesu Khrstu, kuti munene chimodzi mozi inu nonse, ndi kuti pasakahale malekano pakati p ainu; koma mumangike mu mtima momwemo ndi m'hciweruziro chomwecho. (1 Akolino 1:10)**
>
> **Koma kuti ziwalo zifanane ndi kusamalana china ndichinzake. (1 Akolinto 12:25)**

## MAIKIDWE AZINTHU M'BUNGWERI

Utumiki wa Naomi netiweki ndi thambi ya Harvestime International Netiweki imene likulu lake liri m'dziko la Amerika. Nthambi za Naomi netiweki zimagwira ntchito bwino potsatira mfundo za mabugwe zimene ziri m'musimu:

Mtsogoleri wa Naomi Netiweki m'dela lirilonse ayenera:

-Kukhala obadwanso mwatsopano ndi kudzazidwa ndi mzimu.

-Kukhala odzipereka ku cholinga cha bungwe ndi mbali yawo m'bungwiri.

-Perekani repoloti chaka chikatha ku likulu lokhudzana ndi zochitika m'dela lanu.

**Antchito ena agululi** m'dela lanu atha kukhala othandizira mtsogoleri, mlembi, msungi chuma, ndi atsogoleri a mautumiki osiyanasiyana.

Gulu la m'dela lanu likuyenera kumagwiritsanso ntchito zipangizo zophuzitsira za ku

Harvestime Institute m'zochitika zao. Izi sizitanthawuza kuti zipangizozi zizigwiritsidwa ntchito m'sonkhano uliwonse. Kufananitsa kukuyenera kukhalapo pakati pa zochitika zina ndi mphunzitsi obwera monga m'mene mzimu woyera akukutsogolerani. Koma popeza cholinga cha Naomi Netiweki ndi kudzutsa mgwirizano wa azimay odzipereka, opemphera, osunga mwambo, ndi kutsogolerana, m'maphuziro okhazikika ndi ofunika kuti cholinga ichi chikwaniritsidwe. Dongosolo la Harvestime International amapereka ndongosolo limeneri.

Gulu la m'dela lanu likuyenera kupereka kwa ma membala ake mwayi wa utumiki m'dela lanulo komanso maiko ena. Naomi netiweki sikuti ndigulu chabe la chiyanjano cha azimayi kapena kukambirana kwa mau a Mulungu kokha. Cholinga chenecheni ndi kutsogolera azimayi ku cholinga cha Mululngu monga antchito ophuzitsidwa ndi obweretsedwa pamodzi ndipo ndi okonzeka kutumikira kumalo akholola la uzimu m'dziko lapansi.

Misonkhano ikhazikike pa utumiki wa pa dziko lonse lapasi:

-Mupemphererreso maiko ena ndipo chidwi pa umembala chikhazikikeso pa zofunika kwa ogwira ntchito m'malo a kholola pa dziko lapansi.

-Muperekeso ma reporoti okhudzana ndi gulu m'dela lanu komanso magulu ena padziko lonse lapasi amene gulu la m'dela lanu limagwira nawo ntchito.

-Zochitika zanu zithandizire ku cholinga cha utumiki posatengera kuti zochitika zanu akutsogolera ndi mphunzitsi obwera, kaneama kaya ndi phunziro lochokera m'zipangizo za International Institute.

M'dela lanu, gululi likuyenera kupereka mwayi wakuti azimayi akulu atsogolere azimayi ang'ono koma monga mwa maleba: Magwiridwe anchito achonchi akuyenera kuti akwaniritse zolinga monga ndandanda umene uli pa Tito 2:3-5.

Ubale wakulumikizana chonchi ukuyenera kulimbikitsidwa: Limbikitsani ubale wakulumikizana pakati pa mamembala anu. Izi zichitike m'misonkaano imene mwakhazikitsa. Mutha kuphatikiza zinthu ngati mwayi wa utumiki, pemphero, kuwerenga, chiyanjano pa anthu, ndi maziko akudziwana.

## CHAPUTALA 15

## AZIMAYI ONSE A BAIBULO

### Zolinga

Mukakamaliza chaputalachi muyamba kukwanitsa kuchitita izi:

1. Kupitiliza maphuziro anu a “Azimayi, Manenedwe a Baibulo”

**Ndime yotsogolera:**

> **Koma izi zinachitika kwa iwowa monga zotichenjeza, ndipo zinalembedwa kutichenjeza ife, amene amatsirizidwe (1 Akolinto 10:11)**

### MAU OYAMBA

M’phunziro iri muphunzira za ntchito ya azimayi kuyambira pachilengedwe kufikira nthawi ya mpingo. Tikhazikika kwambiri pa ntchito ya azimayi monga mwa Baibulo osakhala mbiri chabe ya azimayi. Cholinga cha izi chinali kukuthandizani kuzindikira dongosolo lanu nthupi la Khritu.

Pali zambiri zoti muphunzire zokhudzana ndi ntchito ya mzimayi kudzera ku mbiri ya azimayi a m’Baibulo. Kuti muphuzire bwino za azimayi a m’Baibulo, m’chaputalachi mwapatsidwa dzina ndi malo amene mzimayi wina aliyese amene anatchulidwa mbaibulo. Tikukulimbikitsani kuti mupitilize maphuziro anu powona mbiri ya moyo wa azimayiwa.

### KUWERENGA MBIRI

Mbiri ndi nkhani ya moyo wa munthu. Njira zowerengera mbiri zimaima kwambiri pa khalidwe la anthu a m’Baibulo. Pophuzira za miyoyo ya anthu amene Baibulo linalemba nkhani zao mukhoza kuphuzira kuchokera ku zimene anakumana nazo. Baibulo limati:

> **Koma izi zinachitika kwa iwowa monga zotichenjeza, ndipo zinalembedwa kutichenjeza ife, amene matsirizide a nthawi ya pansi pano adafika pa ife. (1 Akolinto 10:11)**

Zimene zinachitika m’miyoyo ya anthu amene Baibulo linalemba zinawuziridwa motsogozedwa ndi mzimu woyera kuti zikuthandizeni. Zimene anakumana nazo zikhoza kukuphunzitsani maphunziro akulu awuzimu. Powona zolephera zao mutha kuphuzira zolakwika za uzimu zimene zikufunika kuzipewa. Powona zimene anachita bwino mutha kukulitsa khalidwe la uzimu labwino m’moyo wanu.

Umu ndimene mungawerengere mbiri:

**NDONDOMEKO YOYAMBA: SANKHANI MZIMAYI AMENE MUFUNA KUWERENGA MBIRI YAKE**.

Mutha kusankha mzimayi amene amakusangalatsani inu. Mutha kufuna kusankha m'modzi kuchokera pa ndandanda umene uli pa Ahebri 11, Agalatiya 3:7 kapena Luka 4:27.

**NDONDOMEKO YACHIWIRI: BWERETSANI UTHENGA PAMDOZI.**

Bweretsani uthenga onse okhudzana ndi azimayi pamodzi. Ngati muli ndi mabuku othandiza kuwerenga Baibulo, agwiritseni ntchito kuti mulembe uthenga wa muthu amene nkhani yake mukuyiwerenga. Mwachitsanzo, ngati muli ndi konkodasi, khalani ndi ndandanda wa malo onse kuchokera m'Baibulo. Malo ambiri okhudzana ndi khalidwe la muthu amapezeka m'buku limodzi kapena mabuku angapo otsatiranana. Mutha kugwiritsa ntchito ndandanda umene uli m'gawo la kudziwa zambiri m'chaputalachi. Lembani ndandanda onse wa malo azimayi amene mukuphunzira nkhani yawo kenako werengani ndi kuphuzira khani iriyose.

**NDONDOMEKO YA CHITATU:**

Ndandanda ukubwerawu ukuwonetsa uthenga umene mutha kubweretsa pamodzi kuti muphunzire. Baibulo silingapereke zambiri zokhudzana ndi munthu  m'mbiri yake, koma yesetsani kulemba chilichonse chimene Baibulo linanena chokhudzana ndi nkazi amene mbiri yake mukuwerenga.

Gwiritsani ntchito fomu imene yapatssidwa m'chaputalachi kuti mulembe ndi kulongosola uthenga umene mwaubweretsa pamodzi. Uthenga umene mungaupeze ndi:

-Dzina ndi tanthawuzo la dzina.

-Abale: makolo, abale, alongo, makolo, ana.

-Kubadwa: malo, ubwino wakubadwa kwake, zochitika zodabwitsa zokhudzana ndi kubadwa kwake.

-Umwana wake ndi maphuziro ali wachichepere.

-Malo amene amakhala: Kodi nkhani ya mzimayi inachitikira kuti: kodi amachita chani pa moyo wake?

-Mafotokozedwe amawonekedwe ake.

-Zabwino zokhudzana ndi kukhalidwe lake.

-Zoipa zokhudzana ndi khalidwe lake.

-Zochitika zofunika:

-Kukumana koyamba ndi Mulungu

-Kutembenuka

-Maitanidwe a ntchito

-Vuto lalikulu kapena nthawi imene mzimayuyu anatembenuka.

Mwachitsanzo, chisankho cha Rute kuti amutsatire Naomi.

-Imfa: liti, kuti ndi zochitika zachilendo

**NDONDOMEKO YA CHINAYI: GWIRITSANI NCHITO ZIMENE MWAPHUZIRA.**

Gwiritsani ntchito moyo wa mzimayi amene mwawerenga nkhani yake. Mwa chitsanzo kodi ndi ziti zokhudzana ndi khalidwe lake labwino ndi chani? Pephani Mululngu akuthandizeni kuti zimenezi zikhazikike m'moyo wanu. Kodi khalidwe lake loipa ndi lotani? Kodi mukuwona chimodzi mwa izi m'moyo wanu? Pemphani Mulungu kuti akuthandizeni kuti mugonjetse.

Pangani chiganizo chimodzi chimene chimangilire mfundo yaikulu imene mwaphunzira pa za nkazi amene mukulondola. Mwa chitsanzo, chiganizo chokhudzana ndi moyo wa Hava ndi "Kusavera kumabweretsa chilango".

## NTCHITO YAIKULU

Ndi ntchito yaikuluyi mukumalizitsa phunziro lanu la "Azimayi: Manenedwe a Baibulo." Tikukhulupirira mwakondwera ndi kuzindikira chimene mau a Mulungu akunena zokhudzana ndi inu. Pemphero lanthu ndilakuti mugwiritsa ntchito uthenga umene mwaupeza mphunziroli kuti mulowe mbali yanu ya utumiki m'thupi la khristu. Tikuyembekezeranso kuti mugwiritsa ntchito bukuli podziwitsa azimayi ena amene akufuna mbali yawo mwa Yesu Khristu.

Tsopano gwiritsani ntchito fomu ndi malo m'gawo la "Kudziwa zambiri" popitiliza maphuziro anu.

## KUWERENGA BAIBULO POTSATIRA MBIRI YA MUNTHU

**Ndondomeko Yoyamba:** Sankhani muthu amene mukufuna muwerenge mbiri yake.

**Ndondomeko ya chiwiri:** Bweretsani uthenga pamodzi

Lembani ndandanda wa malo amene moyo wa muthuyo unalembedwa;

**Ndondomeko ya chitatu:** Pangani kawuniwuni wa uthenga Dzina

ndi tathawuzo la dzina:

Abale: makolo, azichimwene, alongo, makolo, ndi ana

Kubadwa: malo, ubwino wa kubadwa, zochitika zachilendo zokhudzana ndi kubadwa:

Nthawi ya umwana ndi maphuziro oyambirira:

Malo:

Azizake ndi othandiza, maubale ake ngati munthu:

Ntchito kapena zimene amachita m'moyo wake wa tsiku ndi tsiku:

Mafotokozedwe am'mene amawonekera:

Zabwino zakhalidwe lake:

Zoipa za khalidwe lake:

Zochitika zazikulu:

Kukumana ndi Yesu koyamba:

Kutembenuka ntima

Maitanidwe kutumiki

Vuto lalikulu kapena masnthidwe ake:

Imfa:

Ndondomeko ya chinayi: Gwiritsani ntchito zimene mwaphuzira.

Khalidwe labwino limene mukuyenera kutengera:

Khalidwe loipa limene mukuyenera kupewa:

Chowonadi chachikulu chimene mwaphunzira m'moyo wake…

**KUPHUZIRA ZAMBIRI**

## AZIMAYI ONSE A M'BAIBULO

Pamene pali azimayi angapo adzina limodzi, azimayi osiyana aikidwa ndi nambala, monga Mariamu 1, Mariam 2, ndi zina.

Abi (Abiya) 2 Mafumu 18:2; 1 Mbiri 2:24

Abigayeli 1 I Samueli 25:3-42; 27:3; 30:5; 2 Samueli 2:2; 3:3; I Mbiri 3:1

Abigayeli 2 2 Samueli 17:25; I Mbiri 2:16,17

Abigayeli 1 1 Mbiri 2:29

Abigayeli 2 2 Mbiri 11:18

Abisagi 1 Mafumu 1:3, 15; 2:17, 21,22,

Abitali 2 Samueli 3:4; 1 Mbiri 3:3

Akisa Yoswa 15:16, 17; Oweruza 1:12; 1 Mbiri 2:49

Ada 1 Genesis 4:19, 20,23

Ada 2 Genesis 36:2

Hagara Agalatiya 4:24,25

Ahinamu 1 1 Samueli 14:50

Ahinamu 2 1 Samueli 25:43; 27:3; 30:5; 2 Samueli 2:2; 3:2; 1 Mbiri 3:1

Apaimu 1 Mbiri 2:31

Ahola Ezekieli 23:4, 5, 36,44

Aholibama Genesis 36:2, 5, 14, 18, 25

Ana Luk 2:36-38

Ana Genesis 36:2 161

Apiya Filemon 1:2

Asenati Genesis 41:45, 50; 46:20

Atara 1 Mbiri 2:26

Ataliya 2 Mafumu 8:26; 11:1-3; 13-20; 2 Mbiri 22:2,10-12; 23:12,13,21; 24:7

Azuba 1 I Mbiri 2:18, 19

Azuba 2 I Mafumu 22:42; 2 Mbiri 20:31

Baara 1 Mbiri 8:8

Basemati 1 Genesis 26:34

Basemati 2 Genesis 36:34

Basemati I Mafumu 4:15

Bateseba II Samueli 11:3, 12:24; I Mafumu 1:11, 15, 16, 28, 31; 2:13, 18, 19; I Mbiri 3:5
Batisuwa I Mbiri 3:5

Bemike Machitidwe 25:13, 23; 26:30

Biliha Genesis 29:29; 30:3-7; 35:22, 25; 37:2; 46:25; I Mbiri 7:13

Bitiya I Mbiri 4:18

Kloe I Akolinto 1:11

Klaudiya 2 Timoteo 4:21

Kozibi Numeli 25:15, 18

Damarisi Machitidwe 17:34

Debora 1 Genesis 35:8

Debora 2 Oweruza 4:4,5,9,10,14; 5:1,7,12,15

Delila Oweruza 16:4,6,10,12,13,18

162

Dina Genesis 30:21; 34:1,3,5,13,25,26; 46:15

Dolika (Tabita) Machitidwe 9:36,39

Drusila Machitidwe 24:24

Egila II Samueli 3:5; 1 Mbiri 3:3

Elisabeti Luka1:5,7,13,24,36,40,41,57

Eliseba Eksodo 6:23

Efa 1 Mbiri 2:46

Efrata 1 Mbiri 2:50; 4:4

Efrati 1Mbiri 2:19

Estere Buku la Estere

Yunike 2 Timoteo 1:5

**Euodias Philemon 4:2**

Hava Genesis 3:20; 4:1; 2 Akolinto 11:3; I Timoteo 2:13

Gomeri Hoseya 1:3

Hadasa (Estere) Buku la Estere

Hagara Genesis 16:1,3,4,8,15,16; 21:9,14,17; 25:12

Hagiti 2 Samueli 3:4; I Mafumu 1:5; 2 Mafumu 2:13; 1 Mbiri 3:2

Hamoleketi1 Mbiri 7:18

Hamutali 2 Mafumu 23:31; 24:18; Yeremiaya 52:1

Hana I Samuel 1:2-22; 2:1,21

Hazeleleponi 1 Mbiri 4:3

Hela I Chronicles 4:5,7 163

Hefisiba 2 Mafumu 21:1

Herodiya  Mateyu 14:3,6; Marko 6:17, 19,22; Luka 3:19

Hodesi 1 Mbiri 8:9

Hodiya 1 Mbiri 4:19

Hogila Numeli 26:33, 27:1; 36:11, Yoswa 17:13

Hulida 2 Mafumu 22:14; 2 Mbiri 34:22

Husimu1 Mbiri  8:8,11

Ikabodi Mai ake a Samueli 4:19-22

Yisika Genesis 11:29

Jaeli Oweruza 4:17,18, 21, 22; 5:6; 24

Yekoliya 2 Mafumu 15:2; 2 Mbiri 26:3

Yediya 2 Mafumu 22:1

Yoadani 2 Mafumu14:2; 2 Mbiri 25:1

Yoseba 2 Mafumu 11:2

**Yekutieli 1 Mbiri 4:18**

Yemina Yobu 42:14

Mwana wa nkazi wa Yefita Oweruza 11:34, 35,40

Yerioti 1 Mbiri 2:18

Jerusa 2 Mafumu 15:33; 2 Mbiri 27:1

Yezebeli l 1 Mafumu 16:31; 18:4,13,19; 19:12; 21:5-25; 2 Mafumu 9:7,10,22,30,36,37 Yezebeli 2 Chivumbulutso 2:20

Yohana Luka 8:3; 24:10

164

Yokobedi Eksodo 6:20; Numeri 26:59

Yuda Yeremiya 3:7, 8,10

Juditi Genesis 26:34

Yuliya Aroma 16:15

Kerenihapuki Yobu 42:14

Ketura Genesis 25:1,4; 1 Mbiri 1:32,33

Keziya Yobu 42:14

Leya Genesis 29:16-32; 30:9-20; 31:4,14,33; 33:1,2,7; 34:1; 35:23,26; 46:15,18; 49:31; Rute 4:11

Loisi 2 Timoteyo 1:5

Wosachitidwachifundo Hoseya 1:6, 8

Nkazi wa Loti Genesis 19:26; Luka 17:32

Lidiya Machitidwe 16:14,20

Maaka 1 Genesis 22:24

Maaka 2 2 Samueli 3:3; 1 Mbiri 3:2

Maaka 3 1 Mafumu 15:2; 2 Mbiri 11:20-22

Maaka 4 1 Mafumu 15:10,13; 2 Mbiri 15:16

Maaka 5 1 Mbiri 2:48

Maaka 6 1 Mbiri 7:15, 16

Maaka 7 1 Chronicles 8:29; 9:35

Mala 1Mbiri 7:18

Mahalalati 1 Genesis 28:9

Mahalalati 2 2 Mbiri 11:18

165

Mala Numeli 26:33; 27:1; 36:11; Yoswa 17:3

Nkazi wa manowa Oweruza 13:2-23

Mara Rute 1:20

Malita Luka 10:38,40,41; Yohane 11:1,5,9,20,24,30,39

Mariya mai ake a Yesu Mateyu 1:16,18,20; 2:11; 13:55; Marko 6:3; Luk0 1:27-56; 2:5,16,19,34; Mateyu 1:14

Mariya wa Magadala (2) Mateyu 27:56,61; 28:1; Mark0 15:40,47; 16:1,9; Luka 8:2; Yohane 19:25;

20:1, 11, 16, 18

Mariya wa ku Betaniya (3) Marko 14:3-9; Luka 10:39; 42; Yohane 11:1-45; 12:3

Mariya 4 Mateyu 27:56, 61; 28:1; Marko 15:40,47; 16:1; Luka 24:10; Yohane 19:25

Mariya 5 Acts 12:12

Mariya 6 Romans 16:6

Matiredi Genesis 36:39; 1 Mbiri 1:50

Mehetabeli Genesis 36:39; 1 Mbiri 1:50

Mesulemeti 2 Mafumu 21:19

Mikaya 2 Mbiri 13:2

Mikala I Samueli 14:49; 2 Samueli 3:13,14; 6:16,20,21,23; 1Mbiri 15:29

Milika l Genesis 11:29; 22:20, 23,24;15;24;47

Milika 2 Numeli 26:33; 27:1; 36:11; Yoswa 17:3

Miriamu 1 Eksodo 15:20; 21; Numeli 12:1,4,5,10,15; 20:1; Deuteronomo 24:9; 1 Mbiri 6:3; Milika 6:4

Miriamu 2 1 Mbiri 4:17

Nama l Genesis 4:22

166

Nama 2 1 Mafumu 14:21; 31; 2 Mbiri 12:13

Nama 1 Mbiri 4:5,6

Naomi Book of Rue

Nehusita 2 Mafumu 24:8

Nowadiya Nehemiya 6:14

Nowa Numeli 26:33; 27:1; 36:11; Yoswa 17:3

Olipa Rute 1:4,14

Penina 1 Samueli 1:2,4,

Persida Aroma16:12

Fanueli Luka 2:36

Febe Aroma 16:1,2

Nkazi wa Pilato Mateyu 27:19

Nkazi wa Potifala Genesis 39:7, 8, 9, 12,19

Priskila (Priska)  Machitidwe 18:2, 18,26; Aroma 16:3; 1 Akolinto 16:19; 2 Timoteo 4:19 Puwa Eskodo 1:15

Mfumu yaikazi yak u Seba 1 Mafumu 10:1, 4, 10,13; 2 Mbiri 9:1, 3, 9,12; Mateyu 12:42; Luka11:31

Rakele Genesis 29:16-31; 30:1-25; 31:4-34; 33:1,2,7; 35:16-25; 46:19-25; Rute 4:11; I Samueli

10:2; Yeremiya 31:15; Mateyu 2:18

Rahabi 1 Yoswa 2:1, 3, 6; 17, 23, 25; Ahebri 11:31; Yakobo 2:25

Rahabi 2 Mateyu 1:5

Rebekah Genesis 22:23; 24; 25; 26; 27; 28; 29:12; 35:8; 49:31; Aroma 9:10

Rcuma Genesis 22:24

Roda Machitidwe 12:13

167

Rizipa 2 Samueli 3:17; 21:8, 10,11

Rute Buku la Rute

Salome Mateyu 20:20; 27:56; Marko 16:1-8

Nkazi wa ku Samaliya Yohane 4:7-42

Safila Machitidwe 5:1

Sela 1 Genesis 11; 12; 16-18; 20; 21; 23-25; 49:31; Yesaya 51:2; Aroma 4:19; 9:9; Ahebri 11:11; I Petro 3:6

Sela 2 Genesis 46:17; Numeli 26:45; 1 Mbiri 7:30

Selomiti 1 Levitiko 24:11

Selomiti 2 I Mbiri 3:19

**Shelomith 3 2 Mbiri 11:2**

Seera I Mbiri 7:24

Simeati 2 Mbiri 12:21; 2 Mbiri 24:25

Simiriti 2 Mbiri 24:26

Shiphrah Exodus 1:15

Someri 2 Mafumu12:21; 2 Mbiri 24:25

Nkazi wa ku Sunemu 2 Mafumu 4:8-37; 8:1-6

Susana Luka 8:3

Suntuke Afilipi 4:2

Nkazi wa ku Sulofonika Mateyu 15:21-28; Marko 7:24-30

Tabita (Dolika) Machitidwe 9:36,39

Takipenesi 1 Mafumu 11:19,20

168

Tamara 1 Genesis 38:6, 11, l3, 24; Rute 4:12; 1 Mbiri 2:4

Tamara 2 2 Samueli 13:1-32; 1 Mbiri 3:9

Tamara 3 2 Samueli 14:27

Tafati 1 Mafumu 4:11

Tamala Mateyu 1:3

Timna Genesis 36:12

Tiriza Numeli 26:33; 27:1; 36:11; Yoswa 17:3

Trufena Aroma 16:12

Trufena Romans 16:12

Vasiti Estere 1:9, 11, 2, 15-17, 19; 2:1, 4, 17

Nkazi wangawiro Miyambo 31:10-31

Nkazi wa masiye wa ku Zarefati 1 Mafumu 17:8-24; Luke 4:25,26

Nkazi wobwebweta 1 Samuel 28:7-25

Nkazi wokonda wachikondi wa ku Thebezi Oweruza 9:53

Zebida 2 Mafumu 23:36

Zeresi Estere 5:10; 14; 6:13

Zeruwa 1 Mafumu 11:26

Zeruya 1 Samueli 26:6; 2 Samuel 2:13,18; 3:39; 8:16; 14:1; 16:9-23; 1 Mafumu 1:7; 2:5,22; I

Mbiri 2:16; 11:6,39; 18:12,15: 26:28; 27:24

Zibiya 2 Mafumu l2:1; 2 Mbiri 24:1

Zila Genesis 4:19, 22,23

Zilipa Genesis 29:24; 30:9,10; 35:26; 37:2; 46:18

Zipora Eksodo 2:21; 4:25; 18:2

## MAYANKHO A MAFUNSO

### CHAPUTALA 1

1. Ndime zenizeni ndi Genesis 2:18 ndi 21-24
   Muthanso kugwiritsa ntchito Genesis 1:27
2. Kukonza mizinda ndi madera. Genesis 1:28
3. Osati kuthupi kokha, komanso ubale wauzimu.
4. Chikondi – Aefeso 5:25-26
   Ubwenzi – Genesis 2:18
   Wothangatira – Genesis 2:18
   Kudzipereka – Genesis 2:24
5. Akhale monga Mulungu kwa munthu, kumthandizira mwamuna.
6. Ndipo Mulungu analenga munthu m'chifanizo chake, m'chifanizo cha Mulungu adamlenga iye; adalenga iwo mwamuna ndi mkazi (Genesis 1:27).

### CHAPUTALA 2

1. Genesis 3:15
2. Genesis 3:15
3. a. Inde b. Ayi c. Ayi d. Inde e. Inde
4. a. MW Genesis 3:3 d. S Genesis 3:15
   b. MW Genesis 3:7 e. M Genesis 3:17
   c. MW Genesis 3:0 f. W Genesis 3: 16

### CHAPUTALA 3

1. Miyambo 31:10
2. Miyambo amatanthauza “mau achidule koma olankhula zambiri”
3. Mkazi wachilendo ndi mkazi wopanda Mulungu, wodetsedwa ndi wosalungama.
4. Mkazi wangwiro ndi mkazi woopa Mulungu, wachiyero ndi wolungama.
5. Ngati simunapeze mayankho awa, onaninso Chaputala 3.
6.

| | | | |
|---|---|---|---|
| a. | S | j. | S |
| b. | S | k. | S |
| c. | S | l. | V |
| d. | S | m. | V |
| e. | V | n. | S |
| f. | S | o. | S |

| | | | |
|---|---|---|---|
| g. | S | p. | V |
| h. | V | q. | V |
| i. | S | r. | V |

## CHAPUTALA 4

1. 3, 1, 2, 6, 5, 4
2. Yerekezani mndandanda wanu ndi zolinga zomwe ziri mu Chaputala 4
3. Nkhani za m'bukhu la Rute nthawi ya oweruza.
4. Moab ndi Betelehem
5. Wolemba bukhuli sadziwika.
6. Rute 1:16-17
7. a. Inde b. Ayi c. Ayi d. Ayi e. Ayi f. Ayi

## CHAPUTALA 5

1. Estere 4:14
2. Yerekezani mayankho anu ndi zolinga zomwe ziri mu Chaputala 5.
3. 4, 1, 2, 3.
4. Wolemba bukhuli sadziwika.
5. Ku nyumba yachifumu ku Susani

## CHAPUTALA 6.

1. Kuti mumachita chifuniro cha Mulungu kapena ayi.
2. Mateyu 12:50
3. 3, 7, 1, 6, 5, 4, 2.

## CHAPUTALA 7

1. Ndipo palinso zinthu zina zambiri zimene Yesu anachita, zoti zikadalembedwa zonse phe, ndilingalira kuti dziko lapnsi sislikadakhala nao malo a mabuku amene akadalembedwa. (Yohane 21:25)
2. Khobidi lotayika — Luka 15:8-10
   Nkazi wokakamira — Luka 18:1-8
   Anamwali Khumi — Mateyu 25: 1-13
   Nkazi wa chotupitsa — Mateyu 13:33

3. Apongozi ake a Petro — Mateyu 8:1-15
   Nkazi wa nthenda ya mwazi — Mateyu 9:20-22
   Mwana wankazi wa mzimayi wa Kukanani — Mateyu 15:21-28
   Nkazi wolumala — Luka 13:11-13
   Mwana wa nkazi wa Yairo — Mateyu 9:18-19
   Mwana wamwamuna wa nkazi wamasiye wa ku Naini — Luka 7:11-15
   Mchimwene wa Mariya ndi Marita — Yohane 11:1-44

**CHAPUTALA 8:**

1. Ndiponso pa akapolo anga ndi pa adzakazi anga m'masiku awa ndizathira cha Mzimu wanga; ndipo adzanenera. (Machitidwe 2:18)
2. Yang'anani mayankho powerenga mitu ya ing'ono m'chaputalachi. Ndandanda wa utumiki uliwonse umene azimayi m'buku la Machitidwe umapezeka m'mitu imeneyi.
3. a. Inde b. Ayi c. Ayi d. Ayi

**CHAPUTALA 9:**

1. Pamenepo ndi iwo akubalalitsidwa anapitapita akulalikira mauwo. (Machitidwe 8:4)
2. 2, 4, 5, 3, 1

**CHAPUTALA 10:**

1. Muno mulibe Myuda, kapena Mhelene, muno mulibe kapolo, kapena mfulu, muno mulibe mwamuna ndi mkazi; (Agalatiya 3:28)
2. a. Inde b. Ayi c. Ayi d. Inde e. Inde f. Ayi f. Ayi h. Inde

**CHAPUTALA 11:**

1. Ndipo musayanjane nazo ntchito za mdima zosabala kanthu koma maka-makanso muzitsutse (Aefeso 5:21)
2. Kuti mutumikire Ambuye opanda zosokoneza.
3. a. Inde b. Inde c. Ayi d. Inde e. Inde f. Ayi h. Inde
4. Nkazi ayenera kuvala modzilemekeza ndipo akuyenera kuima kwambiri pa makulidwe amoyo wa Uzimu kusiyana ndi mawonekedwe athupi.

**CHAPUTALA 12**

1. Kuti akonzere oyera mtima; ku ntchito ya utumiki, kumangirira thupi la khristu. (Aefso 4:12)
2. Onani Aefeso 4:12

   Mayeretsedwe a woyera ntima

Ntchito ya utumiki
Kulimbikitsa thupi la Khristu.

3. Tikhala:

    Amodzi m'chikhulupiriro
    Okulitsa chidziwitso chathu cha Khristu.
    Oyeretsedwa poyang'ana Yesu ngati chitsanzo chanthu.
    Okhazikika, osanamizidwa ndi ziphunzitso zonyenga.
    Okula m'moyo wa Uzimu mwa Khristu.

    Onani Aefeso 4:12-15.

## CHAPUTALA 13

1. Werengani mitu yaing'ono m'chaputala 13. Mukanapanga ndandanda wa chinthu chimodzi mwa zinthu zazikulu zimene zinachitika.
2. Ambuye anapatsa mau; Akazi akulalikira uthengawo ndiwo khamu lalikuru. (Masalimo 68:11)
3. a. Inde b. Inde c. Ayi d. Ayi e. Ayi

## CHAPUTALA 14

1. Miriamu.
2. Gulu liyenera kukhala ndi cholinga chopangitsa kuti likhale. Cholinga chimayankha funso lakuti, "Chifukwa chani gulu lilipo? Kodi tikufuna kukwaniritsa chani?"
3. 1: Pepherani.
    2: Pamodzi itanani gulu la azimayi kuti athandize kuika zinth m'malo ake.
    3: Khazikitsani cholinga chagulu
    4: Khazikitsani maikidwe azinthu m'bungwe lanu.
    5: Khazikitsani tsiku, nthawi, ndi malo a nsokhano.
    6: Adziwitseni anthu za msonkhano.
    7: Lumikizanani ndi onse amene akuyenera kubwera kunsonkhano.
4. Ndipo Miriamu mneneriyo, mlongo wa Aroni, anagwira lingaka m'dzanja lache; ndipo akazi onse anaturuka kumtsata ndi malingaka ndi kuthira mang'ombe. Ndipo Miriamu anawayankha, Yimbirani Yehova, pakuti wapambanatu; kavalo ndi wokwera wache anawaponya m'nyanja.

## CHAPUTALA 15:

M'chaputalachi mulibe mafuso.